

Mwinjiro Wake

Kapena Wanga

FRANK B. PHILLIPS

Wozukuta M'chichewa (translated in Chichewa by):
Kingsley Matiti.

Information on how to get additional copies may be obtained by contacting Justified Walk Ministries at
(269) 471-9224

Additional information about this book, sermon series, and other resources by, or recommended by, Frank B. Phillips are listed at the end of this book, and on the internet at www.justifiedwalk.com

All Scripture quotations are from the King James Version unless otherwise noted. All other quotations, unless otherwise noted, come from the writings of Ellen White.

Copyrighted 2003
All rights reserved

Cover design by Jessica Schultz

Published by Justified Walk
5574 Deans Hill Rd.
Berrien Springs, Michigan 49103

Bukhu ili silogulitsa. Mtengo wake unaperekedwa kale Pamtanda. Poyang'anizana ndi kutha kwa nthawi ndi kufunikira kwa uthenga wa m'bukhuli, tikugawira bukhuli mwachangu.

Ngati mwadalitsika ndi uthenga wa m'bukhuli, chonde gawirani anzanu kuti nawonso amve za Yesu
“Munalandira kwaulere; Perekaninso kwaulere”

ZA MKATIMU

<i>Mawu Otsogolera</i>	4
<i>Chiyambi: Chobvala cha ukwati</i>	7
<i>1. Zachinsinsi! Dziwani zachinsinsi izi!</i>	12
<i>2. Zobvomerezeka ndi a zachilamulo</i>	21
<i>3. Kodi Ungwiro ndiwabwino motani?</i>	32
<i>4. Chipembedzo Chapamanda</i>	38
<i>5. Akhristu Amabadwa, Osati Kupangidwa</i>	47
<i>6. Kuchokera ku Kulungamitsidwa</i>	
<i>Kupita Ku Chiyani?</i>	56
<i>7. Makwerero Anapangidwira Kukwerapo</i>	66
<i>8. Maziko Olimba “ Kuonjezera Chikhulupiro”</i>	78
<i>9. Kutambasula Maziko a Chikhalidwe Chabwino</i>	84
<i>10. Mphamvu Zopanda Malire, “Chidziwitso”</i>	89
<i>11. Zoyamba Zikhale Zoyamba, “Kudziletsa”</i>	94
<i>12. Chipiriro: Ntchito Yangwiro Ya Mulungu</i>	100
<i>13. Palibe Malo Oima</i>	105
<i>14. Chiyani, Palibenso Mpikisano ?</i>	110
<i>15. Chikondi Chopanda Malire</i>	114
<i>16. Kodi Yesu Anayesedwa Monga Ife?</i>	118
<i>17. Unditsate Ine</i>	127
<i>18. Khalani Mwa Ine</i>	134
<i>Mawu Owonjezera A: Chikhalidwe Cha Khristu</i>	142
<i>Mawu Owonjezera B: Chifuniro Cha Munthu</i>	168
<i>Mawu Owonjezera C: Makwerero A Chiyero</i>	178
<i>Mawu Owonjezera D: Mabuku Othandizira</i>	180

Mawu Otsogolera

Bukhuli linalembedwa ndi Malemu Frank B. Phillips nthawi yomwe iwo adapuma pantchito, pamene kwa zaka zokwanira khumi, iwo pamodzi ndi akazi awo a Dorothy, adali kalikiliki kulalikira uthenga wozizwitsa wokhudza “Khristu Chilungamo Chathu” m’misonkhano yachitsitsimutso. Anthu ambiri adakhudzika ndi kutsitsimuka nawo Uthennga wao. M’chaka cha 1978 kudali Sabata Ya Kupemphera yomwe idachitikira pa Andrews University Ku America. Panthawiyi, Mbusa Phillips adafunsidwa kuti asindikize mauthenga onse amene adalalikira. Iye adalembadi mauthengawao, koma mosadziwika bwino, mauthengawo adangoiwalidwa ndipo sadasindikizidwe kwa zaka zokwanira makumi awiri.

Posachedwapa, kupyolera mu njira zodabwitsa, mauthenga onse a M’busa Phillips asindikizidwa mu bukhu, m’ma kaseti, mu chimbale komanso mu njira ya mtokoma pa dziko lonse. Mulungu Akugwiritsadi uthenga womwe udabisika kwa nthawi yaitali, kufikira anthu ochuluka amene ambiri a iwo sanamvepo uthenga wa Khristu Chilungamo Chathu.

Tiri wokondwa kukupatsirani uthenga womwewo mu chiyankhulo chimene inu mukhoza kuchimva, kuti powerenga uthengawu ubweretse kusinthika m’moyo wanu wa Uzimu mu dziko ili loyipa ndi uchimo, komanso kuti mukhale nyali yoikidwa pamwamba pa phiri, younikira ena za choonadi.

Chobvala Cha Ukwati **CHIYAMBI**

Fanizo La Chobvala Cha Ukwati liri ndi tanthauzo lalikululu kwa anthu a Mulungu lero. Mogwirizana ndi Fanizo la Anamwali khumi, mafanizowa sadafikirebe chimaliziro chawo. M' mafanizo onsewa, chimaliziro chake chikudikirira nthawi yomwe Yesu Adzabwere kudzatenga Mkwati-bwi. Mu fanizo lachiwirili Mkwatibwi ndiye akudikirira Mkwati.

Ukwati ukuimilira chiyanjano cha umunthu ndi Umulungu. Chobvala cha ukwati choyenera kubvalidwa, chikuimira Khalidwe La Khristu lomwe ndi lofunikira kwa oyitanidwa onse ku ukwati kuti alandiridwe ndi Atate monga mkwatibwi wa Mkwati.

Mateyu 22 akutionetsera mbali zitatu zimene Mfumu, yemwe ndi Atate wa Mkwati, adatuma antchito ake kukatenga mkwatibwi kubwera naye ku ukwati. Mkwatibwiyu adasankhidwa kale ndipo adadziwiratu kuti ayenera kuwatiwa ndi Mkwati. Baibulo likuta, “Anadza kwa iwo a Iye Mwini, ndipo iwo sanamlandira Iye.” Yohane 1:11. Mpingo, womwe ndi Mkwatibwi Wake wosankhika, unali wotanganidwa kwambiri kotero kuti sunafune kulumikizana Naye monga banja potsatira chifuniro cha Mkwati.

Bvuto linali chobvala cha ukwati. Mkwatibwiyu adafunitsitsa kuchena chobvala chosankha yekha, osati Chobvala cha chikalekale chomwe Tate wake wa Mkwati Adafuna kuti mkwatibwiyu abvale.

Mkwatibwiyu adakwiya kwambiri kotero kuti mapeto ake adaganiza zongothana naye Mkwatiyu. Kuti izi zichitike iye adabvomera ku mulandu wonse wa chilekanitsochi. Khoti lidakhala, ndipo ngakhale oweruza, pamodzi ndi unyinji wa anthu udaoneratu kuti Mkwati ndi Wosalakwa, Mkwatibwiyu adafuula ndi mawu aakulu, "...Mpachikeni! Mpachikeni!" Yohane 19:15. Adapachikidwadi. Mkwatibwiyu adangopepukidwa kwa kanthawi kochepe. Mawu a Mkwati adayambanso kumubvuta: "Gumulani kachisi uyu, ndipo m'masiku atatu Ndidzamuukitsanso." Yohane 2:19. Mkwatibwi adakumbukira zozizwitsa zomwe Mkwati Adachita Akali ndi moyo ndipo mantha aakulu adamugwera.

Pokwaniritsadi Mawu Ake, tsiku lachitatu Mkwati Adabwera Adakali ndi moyo ndi Wathanzi. Adauza m'modzi wa ogwirizira ukwati kuti Ayenera kupita kaye kwa Atate kukaonetsetsa kuti zonse ziri m'malo mwake molingana ndi Chifuniro Cha Atate Wake. Yohane 20:17.

Ulendowo Adapitadi ndipo adabwerera tsiku lomwelo Naonekeranso kwa abale Ake. Izi zidapangitsa ambiri a abale Ake kuganizira mwakuya. Kodi Uyu ndiyemwe Adapachikidwa masiku atatu apitawo? Adatsimikizikadi kuti Adali Yemweyo. Chimwemwe cha Mkwati chidali chodzadza ndipo Adatuma abwenzi Ake kupita kukaitana onse kuti adze kwa Iye. Mkwatibwi uja adakananso kupita chifukwa cha nkhani yomwe ija ya chobvala cha ukwati.

Muzu wa bvuto lonseli udali wakuti onse ogwirizira (kuimira mpingo) amene adakhulupirira mkwati, adalandira chobvala cha ukwati. Nkhani siidali yoti akagula kuti kapena akasoketsa kuti, chobvalacho chidalipo kale. Bvuto lidali kubvala !

Nthawi idafika pamene Mkwati Adaona kuti sakwatiwanso ndi mkwatibwi wake wokondedwa chifukwa chokana kubvala chobvala cha ukwati. Chotero Adauza abwenzi Ake kuti aleke kuumiriza mkwatibwi wake wokondedwa kuti amubvomere. Adawauza kuti apite kwina ndi kwina

kuti amupezere mkwatibwi amene adzabvomere kubvala chobvala cha ukwati.

Iwo adapita kutali, “kufalikira ku dziko lonse” kula-likira uthenga wabwino ndi kuitana onse (Akolose 1:23) koma ambiri analibe nazo chidwi.

Kwa zaka pafupifupi mazana khumi, asanu ndi atatu (1800) antchito ochuluka adatumidwa kukaimirira Mkwati ndi kukaitana onse kubwera ku ukwati. Koma funso la-chikalekale limabwerabe – chobvala cha ukwati. Ena nku-mati sikofunika kukhwimitsa malamulo. Ena nkumaona ngati chobvala cha iwo eni n’chokwanira. Mkanganowu udapitirirabe.

Nthawi idafika imene ngakhale antchito omwe nawonso adakhala ngati akusokonezeka. Ankaitana alendo a ukwati popanda kutchulapo za chobvala cha ukwati. Ena n’kumati “ Ngati mukupereka ndalama zochuluka, chobvala cha ukwati n’chosafunika.” Ena n’kumati , “Ife chobvala cha ukwatico sitikuchidziwa, ingodzisiyani; kungokhulupira basi, ndipo mudzalandiridwa ndi Mkwati.”

Zaka zidapita ndipo mkwatibwi adali wosakonzekabe. Koma Mkwati adali ndi chidwi kuti adzatenge Mkwatibwi Wake, chotero adatuma m’modzi wa ogwirizira, nampatsa malangizo apadera. Nthawi ndi nthawi Wakhala akutumi-za malangizo opita kwa Mkwatibwi Wake kupyolera mwa atumiki ake. Mu njirayi, Mkwati Akuyembekeza kufotozoza mophweka ena mwa mabvuto amene akhala obvuta kumvetsetsa, pogwiritsa ntchito mphatso yotere. M’mauthengawa muli malangizo a m’mene chobvala cha ukwatichi chingabvaliridwe, lomwe lakhala bvuto kwa nthawi yaitali. Malangizowa adalandiridwa ndi ena, komanso ena adawakana. Iwo amene adalandira malangizowa kukuoneka kuti alibe bvuto ndi nkhani ya chobvala cha ukwatiyi. Iwo adapeza kuti ndi m’dalitso umene udapereka mayankho ku mabvuto awo onse. Kwa iwo amene adakanabe malangizowa mabvuto a mgonagonawa adakali nawobe.

Patapita nthawi Mfumu Idaona kuti ukwati udayenera

kuchitikabe basi. Chotero, adalankhula ndi m'bale Jones komanso m'bale Waggoner m'chaka cha 1888 kuti akakomane ndi ena ogwirizira ukwati omwe adali mu msonkhanokwambirana za m'mene angokonzetsere mkwatibwi kukhala pa ukwati. Makosana awiriwa adanenetsa kuti uthenga omwe iwo amalalikira udali njira ya choonadi pokonzekera ukwati.

Apanso chobvala cha Ukwati chinali bvutobe. Ena adaona kuti kunali bwino angochisintha pang'ono chobvala cha ukwatichi kuti chikhalane ndi zofuna zawo. Ena anangoneneratu kuti tiribe nazo ntchito. Owerengeka okha ndiwo adaona chobvalachi ngati mphatso ndipo adachilandira, nachibvala monga chiliri moyo wawo wonse.

Komabe molingana ndi Mkwati, bvutoli lidali likalipobe. Mkwati Adakonza njira ina yodzutsa ku tulo mkwatibwi wake. Izi zidachitika kumayambiro a zaka za m'ma 1900. Mabuku adalembedwa ndikugawidwa a m'mene anthu angakonzekere kukomana ndi Mkwati. Komabe Mkwatibwi sanali otsimikizika za chobvala ngakhale Mkwati adali Akumuitanabe, "Dzuka, dzuka: bvala mphamvu zako, iwe Ziyoni; bvala zobvala zako zokometsa..." " Yesaya 52:1.

Mopilira Mkwati adadikirabe kufikira sakadadikiranso. Mabvuto a m'dziko amanka achulukirachulukirabe. Mu ndale, mu chuma, mu chikhalidwe ndi mu zachilengedwe. Mu uzimu ngakhale ku thupi dziko lonse likupita ku chionongeko. Komabe Mkwati Watsimikizika kukonzetsera Mkwatibwi za kubweranso kwake posachedwa podandaulira za chobvala cha ukwati.

Palibe chobvala choposa chobvala cha ukwati mu dziko lonse. Chobvalachi chimabweretsa mtendere, chimwemwe, kukwanitsidwa ndi chikondi mu mtima wa munthu. Komatu n'chosaoneka kwa iye wochibvalayo, ngakhalenso kwa ena otenga nawo mbali mu ukwati (Mpingo). Komabe chidakali mphamvu ya maginito yokokera ena kulandira kuitanira kwa Uthenga Wabwino.

Ichi ndi chifukwa chake pokhapokha pamene mfumu idabwera kudzaona alendo oitanidwa ku ukwati idaona wina amene anasowa chowiringula. Mateyu 22:12. Iyeyu adali pa ntambasale kufikira nthawi imene mfumu inabwera. Pamenepo ndipamene adaonekera ng'amba ndipo adasowa chowiringula. Kumbukirani kuti iyeyu adalandira mwinjiro pamene adaitanidwa, komano sadaubvale. Akadatino chiyani? Chobvalacho chidali poteropo, chositidwa bwino, chopindidwa bwino. Iye ankadziwa zomwe chimaimira komano kwa iye kuchibvala kudali bvuto. Nzosadabwitsa kuti adasowadi chowiringula.

Cholinga cha bukhuli ndicho kuonetsera m'mene tingalandirire komanso kubvala chobvala chimenechi chomwe aliyense ayenera kukhala nacho komanso kuchibvala ngati tikufunitsadi kudzakomana naya Ambuye ndi mtendere opanda chowiringula chirichonse. Pamene muwerege mutu wotsatirawu mupeza amene ali mwini wa mpungwepungwe wonsewu, komanso m'mene mungamupewere. Pokhapo ndipo pamene tidzaone mowala, “njira” ndi “zifukwa” za Nzeru Yakuya Ya Mulungu Yopulumutsa.

Mokhoza Kumvetsera ulaliki wa M'busa Frank Phillips M'chingerezi omwe uli pa CD, poimba foni ku Justified Walk Ministries pa nambala iyi:

(269) 471-9224

Kapena mukhoza kupeza zambiri m'chingerezi pa mtokoma uwu:

www.Justifiedwalk.com

Mabukuwa ndi aulere ndipo inu simudzalipirapo Ndalama iliyonse.

1.

ZACHINSINSI

Dziwani za Chinsinsi izi!

Maganizo a munthu ndilo bwalo la amaliwongo lomenyerapo mkangano waukulu pa dziko lonse lapansi. Yesu Khristu Akufunitsitsa kulumulira maganizo athu kuti tithe kufikira mwakuya kuthekera kumene Iye Mwini adalengera bongo wa munthu. Naye satana mbali inayi akuyesetsa kuti iyenso alamulire maganizo omwewo amene, “chilakolako cha thupi chidana ndi Mulungu.” Aroma 8:7

Maganizo a munthu akuyerekezedwa ndi kompyuta imene zoganiza zake zimachita kuikidwamo ndi otabwanya awiri: Khristu kapena satana. Monga ichitira kompyuta, maganizo athu amayendera molingana ndi uthenga omwe bongo umalandira. Kenakono chisankho chimapangika molingana ndi chifuniro cha maganizo athu.

Khristu ndiye chiyambi cha maganizo onse abwino. Motsutsana, satana naye amafuna kulumulira maganizo athu, ndipo palibe munthu wotetezeka pokhapokha titalumikizana kotheratu ndi Mulungu. Pali mphamvu ziwiri zomwe zimalumulira maganizo a munthu – Mphamvu ya Mulungu ndi mphamvu ya satana. Satana amalumulira maganizo onse omwe sadasankhe kulumulidwa ndi Mzimu Wa Mulungu.

Tiyeni tione m'mene mphamvu zikuluzikulu izi za Chabwino ndi choipa zigwirira ntchito. Njira yomwe Mulungu Agwirira ntchito ndi anthu ikupezeka pa Yesaya 1:18 “ Tiyeni tsono tiweruzane...”. Mulungu Akufuna koyamba, mtima, komanso chikondi. (Mtima ndi maganizo zikutanthauza chinthu chimodzi mu Baibulo ngakhalenso mu zolemba za Ellen White)

“Mwananga, undipatse mtima wako, maso ako akondwere ndi

njira zanga. “Miyambo 23:26.

“Njira yoyambira kukonza kochokera kunja kwa mtima kumalizira mkati ndi yolephereka nthawi zonse ndipo siidzatheka.

Njira ya Mulungu ya kwa inu ndiyo yoyamba ndi pachimake pa mabvuto onse, mtima. Kuchokerano mumtima, mudzatumphuka mfundo za chilungamo; kukonzanso kudzakhala kwa mkati ndi kunja komwe.”

“Nthawi zambiri anthu amakamba za munthu amene akuyamba kumene chikhrisu nkumati, “Tamuonani, wangosiya khalidwe loipa ili ndi lija basi.” Komatu zomwe munthu ali nazo kapena zomwe munthu achita sindizo bvutolo, koma zizindikiro za bvuto lenelenilo. Mulungu Akuti, “...Pakuti munthu ayang’ana chooneka ndi maso, koma Yehova Ayang’ana mu mtima.” 1 Samuel 16:7. “Chinjiriza mtima wako koposa zonse uzisunga; pakuti magwero a moyo aturukamo.” Miyambo 4:23.

“Monga chotupitsa mkate chigwira ntchito Kuchokera mkati kufikira kunja, chomwechonso zidalira Kukonzanso mtima wa munthu mkati kuti chisomo Cha Mulungu chisintho moyo. Alipo ambiri amene Amayesa kukonza khalidwe ili ndi ilo loyipa naganiza kuti Potero adzakhala Akhristu, komano oterowo akuyambira Polakwika. Ntchito yathu yoyamba tiyambe kukonza mtima.”

Titha kuona kuti njira ya Mulungu yofikira chiyang’aniro Chake ndi njira yoyamba ndi mtima kapena maganizo a munthu. Ngakhale izi zimayenderabe kulolera kwa ife eni. “Taona ndaima pakhomo ndigogoda...” Chibvumbulutso 3:20. “Ngati inu muli ofuna ndi omvera mudzadya zabwino za dziko.” Yesaya 1:19

“...Mulungu Adzalandira okhawo amene ali ofuna.”

Chotero Iye Sadzalola kumvera kongotsatira malamulo a ntchito, kapena kuumirizidwa ngakhaleenso kukwaniritsa chikumbumtima chotsutsika.

“Munthu amene amangosunga Malamulo a Mulungu chifukwa chongofuna kupulumutsa ntchito, kapena chifukwa chofunsiidwa kutero, sadzaona chimwemwe chomwe chimadza ndi kumvera. Wotereyu ndi munthu wosamvera. Pamene Chifuniro cha Mulungu chimaoneka ngati chipsinjo ndi katundu wolemera chifukwa

chikulepheretsa ufulu wathu, apo ndipo tidzadziwa kuti moyowo sindiwo wa Chikhristu. Kumvera kwenekweni kumachokera mkatikati mwa mtima wa munthu. Kumachokera ku akasupe a chilungamo ndi chikondi cha Lamulo La Mulungu.”

Njira ya satana yogwirira ntchito inayamba kumwamba, kumene adakhoza kufalitsa mpanduko omwe udayamba m’aganizo a iye mwini.

“Idali mfundo yake yofuna kusokoneza maganizo a omutsatira pogwiritsa ntchito mikangano yochenjera yokhudza zifuniro za Mulungu. Chirichonse chophweka, iyeyu adachipanga kukhala chobvuta kumvetsetsa, ndipo ndi luso lakuya adabweretsa chikaiko pa mawu ophweka kumva a Yehova.

Nzeru imeneyi satana wakhala akuigwiritsa ntchito pano pa dziko lapansi kwa zaka tsopano pafupifupi zikwi zisanu ndi chimodzi.

Mdaniyu ndi katakwe pa ntchito yake, ndipo ngati anthu a Mulungu satsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, adzakodwa mu msapha wake.

“ Kwa zaka zochuluka satana wakhala akuyeserera pa momwe umagwirira ntchito bongo wa munthu, ndipo iyeyu akudziwa bwino lomwe. M’masiku otsiriza ano satana walumikizitsa bongo wa anthu ndi wa iye mwini, kuupatsa maganizo a iye mwini, ndipo izi akuzichita mwa chinyengo chakuya, kotero kuti iwo amene asankha kutsogozedwa ndi iye sangakhoze kuzindikikira ichi.”

Ntchito ya satana idayamba kumwamba pomabweretsa mafunso ndi chikayiko ndi maganizo, mu mjira yakuti angelo amene anagwa naye pamodzi sanadziwe kuti akuwatsogolera ku chionongeko. Potero, njira iliyonse yomwe inatheka kumwambako singalephereke pano pa dziko lapansi.

Tonsefe ndife mboni za chipambano chake.

Tsopano tiyeni tiombe mkota pa zomwe tanenazi. Mphamvu ziwiri Zonsezi zikufunitsa kulamulira maganizo a munthu kotheratu, kopanda kugawana ndi wina. Mulungu Akufuna munthu wogonjera kwa Iye mwa kufuna kwake kwa munthuyo; naye satana akufuna munthu amene sangathe kudziimira payekha – mphatso yochokera kwa mdierekezi mwini.

“ Mdaniyo akukonzekera misonkhano yake yokopa anthu m’masiku ano otsiriza. Iye wazizimbaitsa kotheratu kothero kuti nkobvuta kumuzindikira kapena kukhulupira kuti alikodi kapenanso kutsimikizika za mphamvu zake zozizwa. Ambiri adaiwala za mbiri yake yakale; ndipo pamene iye abvumbuluka, sadzaz-indikirika kuti ndi m’dani wao, chinjoka chakalekale, komano adzamuyesa iye bwenzi, iye amene akuchita zabwino.

Ponyadira za kudziimira pa okha, iwo adzamvera ndi kutengeka ndi chikoka chake, poganizira kuti iwo akutsogoleredwa ndi Mulungu. Maso awo akadatsegulidwa kuti aone akuwatsogolera akadaona kuti sakutumikira Mulungu koma m’dani wachilungamo chonse. Akadaona kuti kudziimira paokha komwe akhala akunyadira kwakhala nsinga zolimba zomanga maganizo awo.”

Mulungu Akunena kupyolera mwa Yesu Khristu, “ Chifukwa chake ngati Mwana Adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu.” Yohane 8:36. Komano satana naye akuti “Changamukani, musakhale kapolo wa aliyense.”

Mulungu Amagwiritsa ntchito kukambirana moonana maso ndi maso , pamene satana amagwiritsa njira zodzizimbaitsa pomupanga munthu kuti akudziganizira yekha maganizo ake ndi zisankho zake, chikhalirenicho zonse akutsogolera ndi satana.

Munkhondo yonseyi chinthu chimodzi chomwe satana amayesetsa kuchibisa ndicho chakuti – Iyeyo ndi wofooka kale ndi kale. Kuyambira pachiyambi satana wakhala akulakalaka kugwetsa munthu, ndi cholinga chakuti iyeyo pamodzi ndi munthu wakugwayo akhululukidwire pamodzi ndikupezanso mwayi wina wolowanso kumwamba. Koma njira ya Mulungu Idali ina. Popeza satana ndi angelo ake adagwa poukira moonekera, ndikuti munthu adagwa poyesedwa, kuchimwa kwawo kudali kosiyana. Poto Mulungu Adalamula kuti munthu yekha ndi amene apatsidwe mwayi wolandira mphatso ya mphamvu ya Mulungu ya chiombolo ya Mwana Wake kupyolera mu nzeru ya chipulumutso.

Mosakhalitisa satana adadziwa kuti nzeru yake yapangitsa kuti Yesu, Mwana Wa Mulungu Akhale munthu ndi kupereka dipo la uchimo m’ malo mwa munthu wochimwa. Apatu satanayu adasangalala. Komabe adali ndi bvuto limodzi. Akadatani kuti munthu akhalebe mu ulamuliro wa satana? Apatu ndipo pagona chinsinsi chakuya cha satana!

Mkatikati mwa bongo wa munthu Mulungu Adaikamo mphatso ya mtengo wapatali – chisankho. “Iyi ndi mphamvu yotsogolera mu chilengedwe cha munthu, mphamvu ya chisankho. “Chisankho chanu ndicho kasupe wa zonse zomwe inu mumachita.” Ngati satana atakhala nayo mphamvu yolamulira mphamvu yanu ya chisankho, kudzamukhalira kophweka kugwetsera munthu ku chionongeko pomuganizitsa munthuyo kuti adakali nayo nthawi yochuluka kusintha monga afunire.

Nangano tinene bwanji za chinsinsi chosungikachi? “Chisankho, chomwe ndi mbali yofunikira kwambiri mu khalidwe la munthu, chidaperekedwa ku ulamuliro wa satana pamene munthu adagwa; ndipo satanayo wakhala akugwiritsa ntchito chisankho cha munthu wakugwachi monga iye afunira, komano pongomu-kankhira munthuyo ku chipasuko chotheratu.

Nanga n’chifukwa chiyani ichi chiri chinsinsi chofunika kuchidziwa? Chifukwa iyi ndi njira yomwe satana akulamulira munthu popanda kuzindikiridwa kuti iyeyo satana walowererapo. Iyi ndiyo njira yomwe satana adagwiritsa ntchito kumwamba. Satana akudziwa kuti Mulungu sangamulande ulamuliro woterewu kwa iye, pakuti Mulungu Sadzaumiriza chisankho kapena chifuniro chathu. Ambuye Ali ndi njira imodzi yokha – Kutiombola ife kuti tikhalenso Ake. Chifukwa cha mphatso Yake yopereka Yesu Khristu kwa ife anthu, Mulungu Akuti, “Dziperekeni kwa Ine; mundipatse chifuniro chanu; chotsani chifuniro chanu kwa satana, ndipo Ine Ndidzakulamulirani; potero Ndidzakhoza kugwira ntchito mwa inu kufuna ndi kuchita chifuniro Changa.

Munthu akuyenera kuchotsa chifuniro chake kwa satana asanachipereke kwa Khristu. Satana akudziwa bwino lomwe kuti sangaumirize kapena kulamulira chifuniro chimene chachoka kwa iye. “satana alibe mphamvu yolamulira chifuniro cha munthu ngakhale kuumiriza munthu kuchimwa. Pokhapokha Khristu Akulamulira, satana alibe mphamvu. “satana akudziwa kuti sangathe kugonjetsa munthu pokhapokha atalamulira chifuniro chake.”

“Mdierekezi sangatiumirize ife kuti tichite choipa. Sangalamulire maganizo pokhapokha maganizowo atapendekeka kwa iye. Chifuniro chikuyenera kubvomera ndipo chikhulupiriro chigwiritse Khristu, satana asanaonetsere mphamvu yake pa ife.” Ufooko wa satana nawu: “ satana amadziwa kuti munthu

wofooketsetsa koma amene akhalabe mwa Yesu Khristu, ali nayo mphamvu yoposa mphamvu zonse a angelo a kumidima ndipo ngati satanayo atadzionetsera pamtetete akhoza kugonjetsedwa.”

Apatu timvesetsane kuti pamene tachotsa chifuniro chathu kwa satana, tiribe mphamvu mwa ife tokha kusunga chifuniro chathucho. Chiyenera kuperekedwa kotheratu kwa Yesu. Ndi Mulungu Yekha Amene Angathe kuchisunga chifunirocho ku machenjero a satana. Pokhapokha chifuniro chathu tasankha kuchiika mwa Khristu, satana angathenso kutilanda ndi kutila-muliranso. “Palibe wina amene angathe kukonzanso khalidwe loonongedwa ndi uchimo koma Khristu Yekha Ndiye Angathe. Iye Adadza kudzachotsa ziwanda zomwe zidalamulira chifuniro chathu.

Pali mfundo inanso yofunika kumvesetsa ya momwe satana ndi ziwanda zake amalamulira chifuniro cha munthu. “Iwo amene sangagonjetsedwe ndi satana ayenera kuteteza kotheratu njira zonse za moyo wawo; iwo akuyenera kulewa kuwerenga, kuwonera kapena kumvetsera izo zomwe zimakopa maganizo a chibvundi.” “Aliyense ateteze njira zonse zachibadwidwe – kuona, kukhudza, kulawa, kununkhiza ndi kumvetsera, kuti satana asapezerepo danga; popeza awa ndiwo makomo a moyo wa munthu.”

Njira za chibadwidwezi ndizo bwalo losewererapo mdierekezi – kulawa, kukhudza, kuona, kumvetsera, kununkhiza – zonsezi ziri ndi gwero limodzi la umo momwe ife tikhumbira, satana asanatikokere mu zolinga zake. Pena tidzifunse tokha kuti ndi zisankho zingati zomwe timapanga patsiku kupyolera m’mene ife eni timvera m’thupi lathu, poyerekeza ndi kupanga chiganizo choyenerera.

Pamene tikuchotsa chifuniro chathu kuti chisalamulidwensu ndi satana ndi kuchipereka kwa Yesu, Iye Amachitsukuluzwa m’chiyero nachibwezera kwa ife cholumikizidwa ndi chifuniro Chake. Umo ndi m’mene Iye Akhala mwa ife ndi ife mwa Iye. Zotsatira zake n’zakuti pochita chifuniro Chake, tikuchita chifuniro chathunso.

Kudzipereka komwe tikukambaku sindiko kwa ulesi – kongochitika mphwayi ziri toloo! “Ndi kupyolera mu chifuniro chomwechi pamene tchimo limakhozanso kubwerera kwa ife. Kupereka chifuniro chathu kukufanizidwa ndi kukolowola diso

kapena kudula dzanja lathu ngati litichimwitsa.”

Tiyerekeze kuti mkhrisu wakodwa mu msampha wa chizolowezi cha tchimo lomwe limamukomera nthawi zonse. Iye akudziwadi kuti akuyenera kulekana nalo tchimolo komanaso amapemphera nthawi zonse kuti Ambuye Amuthandize kumuchotsera tchimolo. Mwina iyeyo nkumamvadi mumtima mwake kuti alekane nalo tchimolo kulipereka kwa Mulungu. Chomwe wotereyu ayenera kudziwa n’chakuti ichi ndi chisonyezo chakuti mkhristuyo sanafikirepo popereka chifuniro chake kwa Mulungu. Wotereyu adakalalakabe kutsogolera moyo wake wa iye mwini pa yekha ndipo sadafike pomvetsetsa kuti pamene Mulungu Alamulira chifuniro, ife eni timayenerabe kupanga chisankho, pamene tikufuna kuchita chifuniro chake osati chathu. Tikuyenera kumvetsetsa kuti chilakolako chathu chachibadwidwe kuchita “zomwe ife tifuna” chimasinthika kuchita chifuniro Chake pogonjera tsiku ndi tsiku. Apatu timapindula pokhala moyo watsopano umene tchimo liribenso mphamvu pa ife, ndipo moyo wathu umakhala ndi mtendere wamumtima.

Pamene chifuniro chathu chilamulidwa ndi Mulungu, njira zathu zija zisanu zachibadwidwe zimasandulika maganizo oyenera, osati m’mene ife tikumvera m’thupi mwathu. Poto timakhala mwa chikhulupiriro osati mwa kuthupi. Kukhala mwa chikhulupiriro sikutanthauza kuti sitiri mu thupi ayi, koma zikutanthauza kuti thupilo liri m’malo mwake. Zonse zidzatsatira chifuniro osati zotsatira za m’mene ife eni tikumvera.

Tsopano apa mwadziwa chinsinsi chakuya cha m’daniyo! Ngati simunaganizirepo zochotsa chifuniro chanu kwa satana ndierekezi bwanji muyambepo lero? Ingolankhulani momveka kwa satanayo kuti, “Ndikuchotsa chifuniro changa kwa iwe ndikuchipereka kwa Yesu.” Mukatero nenaninso kwa Yesu kuti, “Chonde Ambuye, tengani chifuniro changa sindingathe kuchisunga.”

Yesu Akulonjeza kutenga, kuyeretsa, kutsuka ndikubwezera chifunirocho kwa inu, molumikizidwa ndi chifuniro chake. “Pamene mupereka chifuniro chanu ndi nzeru zanu ndikuphunzira kwa Yesu, pamenepo mudzapeza malo mu Ufumu wa Mulungu.”

Palibe mphamvu ina iriyonse kumwamba ngakhale pa dziko lapansi imene ingatiumirize ife kupanga chisankho chotere. Tikumbukire kuti ndi makwerero ophweka mu nzeru Ya Mu-

lungu Ya Chipulumutso imene satana amayesetsa kutifooketsa kuti tisakhulupirire ndi kuigwiritsa ntchito. Mphamvu ya satana kwa ife idzathyoka ngati titatsata kudzipereka chifuniro chatu kwa Mulungu tsiku ndi tsiku. Iye akudziwa kuti mfungulo ili m'manja mwathu. Kodi mungayambepo kugwiritsa mfunguloyi? Idzakutsegulirani mphamvu za kumwamba pamene mulumikiana ndi Mulungu.

Nawa mafunso okuthandizani kuchita zomwe mwaphunzira pa mutuwu:

A. FUFUZANI

Kodi “Chinsinsi chobisika” cha satana ndi chiti nanga “kufooka” kwake ndi kuti?

Maganizo oipa amabwera kudzera m'makomo athu a chibadwidwe: Makomowo ndi ati? ndi njira zANJI zomwe mungatsekere makomowa?

B. NTCHITO YA MOYO WANU

“Nenani momveka kwa satana, “Ndikuchotsa chifuniro changa kwa iwe ndipo ndikuchipereka kwa Yesu. Ndipo munene kwa Yesu, “Chonde Tengani chifuniro changa sindingathe kuchisunga ndekha” Pemphani mu pemphero kuti iyi ikhale ntchito ya moyo wanu...ndipo **KHALANI MOYO WOTERO!!**

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, umu ndi momwe moyo wanga ukhalire: (Kusintha komwe kukhalepo pamene Ambuye Akuyankha pempho langa)

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Mapazi opita kwa Khristu, (Steps to Christ), tsamba 26
2. Maumboni, (Testimonies) bukhu 4, tsamba 542
3. Kudziletsa, (Temperance), tsamba 276
4. Maumboni kwa Abusa, (Testimonies to Ministers). tsamba 79
5. Maumboni, (Testimonies) bukhu 2, tsamba 169

6. Malangizo a Kadyedwe ndi Chakudya, tsamba 35
7. Mafanizo A Yesu (Christ Object Lessons), tsamba 97
8. The SDA Bible Commentary, bukhu 7, tsamba 977
9. Mafanizo A Yesu (Christ Object Lessons), tsamba 97
10. Makolo ndi Aneneri (Patriarchs and Prophets) tsamba 41
11. Mauthenga osankhika (Selected Messages)
bukhu 2, tsamba 352-353
12. Makolo ndi Aneneri (Patriarchs and Prophets).
Tsamba 35-40
13. Maumboni (Testimonies) bukhu 5, tsamba 294
14. Mapazi Opita Kwa Khristu
(Steps To Christ), tsamba 47
15. Malangizo kwa Achinyamata,
(Messages to Young People), tsamba 135
16. Malangizo kwa Achinyamata,
(Messages to Young People), tsamba 154
17. Malangizo Kwa Achinyamata,
(Messages to Young People), tsamba 154
18. Mkangano Waukulu, (The Great Controversy),
tsamba 510
19. Kudziletsa, (Temperance), tsamba 16
20. Chokhumba Cha Mibadwo,
(The Desire Of Ages), tsamba 125
21. Mkangano Waukulu, (The Great
Controversy), tsamba 530
22. Chokhumba Cha Mibadwo,
(The Desire of Ages), tsamba 38
23. Machitidwe a Atumwi, (The Acts of the Apostles),
tsamba 518
24. Banja la chi Adventist, (The Adventist Home),
tsamba 401
25. Malingaliro a Paphiri, (Thoughts from the
Mount of Blessing), tsamba 61
26. Mauthenga Osankhika, (Selected Messages),
bukhu 1, tsamba 110

2.

Lobvomerereka NDI A ZACHILAMULO

“Chifukwa chake inu mukhale angwiro, monga Atate wanu wa kumwamba Ali Wangwiro.” Mateyu 5:48. Chiganizo ichi chomwe chikuchokera pa Chiphunzitsa cha Paphiri, chikutisonyezeratu kuti maganizo a Mulungu okhudza munthu sanasinthe. Iye Anamupanga munthu kukhala wangwiro.

Pamene Adamu adagwa kuchoka mu ungwiro wake, mtundu wonse wa anthu udatenga tchimo lake. Komabe ngakhale izi ziri chomwecho kugwa kwa munthu mu uchimo sikunachotsere chiyani’ganiro cha ungwiro chimene Khristu Akuchilankhula pa Mateyu 5:48.

Komabe, Mulungu Ali nayo njira imene munthu akhoza kufikira ziyani’ganiro Zake. Njiira yake ndi yophweka kotero kuti munthu aliyense akhoza kuimvetsa, ngakhale ili yakuya kotero kuti ndi Mulungu Yekha Amene Adziwa kuya kwake. Yohane 3:16.

Satana, poonetsera molakwika khalidwe la Mulungu kwa munthu, wapangitsa kuti njira ya Mulunguyo imveke molakwika. Zotsatira zake ndi zakuti munthu wadzipangira yekha njira zochulukira zofikira chiyero.

Timamva chisoni poona anzathu a mtundu wa chi Hindu, amene amachita kugubuduzika pa kama wa zobayabaya, kuti apeze chiyerochi. Chikhalirenicho nafenso timayesetsa kufikira chiyerocho popanga zinthu zabwino zimene ife timaganiza kuti mkhristu wabwino ayenera kuchita kuti akafike kumwamba.

Ziribe kanthu kuti chinyengo chayandikira motani ku choonadi. Chinyengo ndi chinyengo basi. Pamene chinyengo chikuoneka ngati chayandikana ndi choonadi, ndipameneno icho

chimankirakira kukhala chabodza. N'chifukwa chake “Chikhomo choipitsitsa cha uchimo m'dziko lomwe tikukhala sindicho... moyo wa munthu wochimwitsitsa kapena munthu wotaidwa kunja; koma ndi moyo umene umaoneka wangwiro, wolemekezeka ndi waulemu, komano mkati mwake muli katchimo kang'onon'gono, katchimo kamodzi ka mgonagona.”

Tchimolo likhoza kuoneka laling'ono. Komano si msinkhu wa tchimo womwe uli wofunika komano kukana kuzindikira khalidwe la uchimolo ndi kupereka mpanduko wathu kwa Yesu. Ndikulimbanalimbana ndi ntchito Yake m'moyo wathu komwe kumaswa mtima wa Yesu, popeza palibe chomwe Iye Angachite pokhapokha ife tiri ololera kudzipereka monga dongo m'manja a Woumba mbiya.

Njira Ya Mulunguyi Ikukambidwa mwachidule motere mu bukhu la Mapazi Opita Kwa Khristu.

“Zidali zotheka kwa Adamu, asadagwe, kuti akhale ndi khalidwe langwiro pomvera Lamulo La Mulungu. Koma iya adalephera kuchita izi, ndipo chifukwa cha tchimo lake chikhalidwe chathu ndi chakugwa ndipo sitingadzilungamitse tokha. Popeza ndife ochimwa, ndi opanda chiyero, sitingathe kumvera mwaungwiro Lamulo Lachiyero La Mulungu. Ife tiribe chilungamo cha ife tokha chimene tingakhoze nacho kukwaniritsa Lamulo La Mulungu. Komano Khristu Watipangira ife njira yopulumukirapo. Iye Adakhala padziko pano pakatikati pa mikwingwirima ndi mayesero ofanana ndi amene ife tiyenera kukomana nawo. Iye Adakhala moyo wosachimwa. Iye Adatifera ife, ndipo, iye Ali Ololera kutenga machimo athu ndikutipatsa ife Chilungamo chake. Ngati inu mudzipereka kwa Iye ndi kumulandira Iye monga Mpulumutsi Wanu, pomwepo ngakhale moyo wanu wakhala wochimwitsitsa, chifukwa cha Iyeyo mukuyesedwa wolungama. Khalidwe La Yesu Likulowa m'malo mwa khalidwe lanu, ndipo mukulandiridwa ndi Mulungu monga ngati kuti simudachimwe.”²

Apatu tikuona njira yozizwitsa ya Mulungu mu ndime imodzi. Njira Ya Mulunguyi ndi yakuya koposa momwe ife tingaionere

patali. Paulo akuti, “Iye [Mulungu] Wadzibvumbulutsira Yekha kwa ife chifuniro Chake chobisika – Ichitu chidali Chifuniro Chake chimene chidakhazikidwiratu mwa Khristu- kuti Chikwaniritsidwe pakufika pa nthawi: ndicho chakuti: miyamba yonse, onse okhala m’mwamba ndi padziko afikire pa umodzi mwa Khristu.” Aefeso 1:10.

Tangoganizani! Miyamba yonse kubwera pamodzi mu chiyanjano changwiro pokokedwa ndi mphamvu ya maginito ya Chikondi Cha Mulungu chodzera mwa Yesu Khristu.

Komatu izi sizokhazo. Timalandira cholowa “...Mwa Iye tinalandira cholowa Chake (kukonzetseredwatu) monga mwa chitsimikizo mtima cha Iye [Mulungu] Mwini. Aefeso 1:11. Kodi mungaganize zomwe zimachitika pamene tikhala olandira cholowa? Izitu zimatanthauza kuti ife timakhala ziwalo za banja lake -Thupi Lake ndi mafupa Ake. Ifetu si ana a kunjira; komano olumikizidwa mwa mpesa weniweni. Izi zikambidwa mwakuya mu ndime yakutsogolo kwa bukhuli.

Tsopano, popeza mu njira ya Mulungu Yesu ndiye mphamvu yolunzanitsa imene mayiko onse akukomanirapo, ndipo munthu aliyense wamangikirapo ndi zingwe zachikondi, tikhoza kuona kuti khalidwe la Khristu (Mwinjiro Wake wa chilungamo) woperekedwa kwa ine – munthu wochimwa, ndi njira yokhayo imene angelo, okhala a m’mayiko ena, komanso amuna ndi akazi a m’maiko onse a padziko lapansi angathe kubvomereza opanda kufunsa funso, kuti ife tiri otetezedwa mpaka muyaya. Pokhapokha ife tikhala monga Iye mu chikhalidwe, tidzatha kuonetsera kukhazikika kumene sikudzagwedezeka.

Ndiri ndi chikhulupiriro kuti kufikirano pano tapeza kuti njira yokhayo yofikira ku ungwiro ndiyo kulungamitsidwa – kukhala ngati sindinachimwepo. Ndiri ndi chikhulupiriro kuti zikumveka tikamati kulungamitsidwa ndiko kutanthauza kuti Khalidwe Langwiro La Yesu Khristu Labvekedwa pa munthu wochimwa, wopanda chiyembekezo.

“Nangano kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro ndi chiyani?” Ndi ntchito Ya Mulungu kukwirira m’dothi ulemerero wa munthu ndi kumuchitira munthuyo izo zimene iye sangathe kuchita payekha ndi mphamvu zake. Pamene anthu angathe kuona kuperewedwa kwa

iwo weni, ndipokhapo pamene iwo angathe kubvekedwa ndi Chilungamo cha Yesu.”³

Tiyeni tsopano tione m'mene kulungamitsidwa kumachitkira. Baibulo limafotokoza momveka bwino mu chiganizo chimodzi. “Popeza tsono tayedwa olungama ndi chikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” Aroma 5:1. Munjira ina, imfa ya Yesu imamupangitsa Iye kulungamitsa aliyense amene ali wofuna kulungamitsidwa. “Pamtanda wa Gologota Iye Adalipira dipo la chipulumutso cha anthu. Potero Iye ali nayo mphamvu yopulumutsa amunsinga kuwachotsa mdzanja lonjata la mdierekezi wamkuluyo.” Apa titha kuona kuti chikhulupiriro ndicho njira yokhayo, osati chiyambi chokha cha kulungamitsidwa. Ife sitiima pa nthaka ya chikhulupiriro, komano chikhulupirirocho chimandithandiza ine kuima, pokhulupirira Mawu a Mulungu. Chikhulupiriro chiri chenechenidi choposa makomo athu aja asanu a chibadwidwe. (Pezani SDA Bible Commentary, bukhu 6, tsamba 1073.)

Tsopano pali mbali inanso yofuna kuiona pamene tikukamba za nkhanayi ya chikhulupiriro. Paulo akuti, “Koma podziwa kuti munthu sayesedwa wolungama pa ntchito ya lamulo koma mwa chikhulupiriro cha Yesu Khristu, ifedi timakhulupirira mwa Yesu Khristu, kuti tikayesedwe olungama ndi chikhulupiriro cha Khristu, ndipo si ndintchito za lamulo; pakuti palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo.” Agalatiya 2:16.

Tiyenino titaona ndemanga yomwe idalembedwa mu Review & Herald, wa pa April 24, 1888:

Tiyenera tiphunzirepo pa moyo wa Mpulumutsi wathu, Popeza ndi Yekhayu Amene ali chitsanzo chang-wiro chakuti munthu akhoza kukoperepo. Tiyenera kulingalira pa nsembe yakuya ya Umulungu ya pa Gologota, ndikupenyererapo kuipitsitsa kwa tchimo komanso chilungamo cha Lamulo. Mutatero mudzakhala mutaphunzira mwakuya za nzeru ya chipulumutso ndipo mudzalimbikitsidwa komanso kupatsidwa ulemu. Kumvetsetsa kwanu kokhudza khalidwe la Mulungu kudzakhala kwakuya: ndipo ndi nzeru yonse ya chipulumutso yoonetsedwa powala m;maganizo mwanu,

mudzakhoza kukwaniritsa maitanidwe anu a ntchito ya umulungu. Kuchokera ku chitsimikizo chakuya mudzathano kupereka umboni kwa anthu za kusasinthwa kwa khalidwe la Lamulo la Mulungu loonetsedwa ndi imfa ya Yesu pa mtanda, kuipitsitsa kwa tchimo komanso Chilungamo Cha Mulungu polungamitsa wochimwa wokhulupirira mwa Yesu pokhapokha kuti wochimwayo no adzakhalano womvera Malamulo a Boma la Mulungu kumwamba ndi dziko lapansi.”⁵

Chonde werenganinso chiganizo chomarizirachi mu ndime yangothayi ndikuona umo m'mene Mulungu Alungamitsira anthu.

Ifetu sitingathe kumvetsetsa chikhulupiriro chotere. Ichi ndi chikhulupiriro chodabwitsa cha Mulungu mu njira yakeyake ya chipulumutso kwa ine – wochimwa. Ifeno tingoti, “Ambuye, ndikhulupirira, thandizani kusakhulupirira kwanga.”

Ndiri wokondwa popeza Mulungu Adapereka kwa wina aliyense muyeso wake wa chikhulupiriro. Ndiyeno n;chochuluka motani? Chokwaniratu kufikira monga tate uja wosauka amene mwana wake wamwamuna anagwidwa ndi ziwanda.. Chikhulupiriro chathu chimatsegula khomo kuti Yesu Athe kutithandiza molingana ndi chosowa chathu ndi Ulemerero Wake. Yesu sindiye chiyambi chokha, komanso womaliza wa chikhulupiriro chathu. Ahebri 12:2.

Chotero njira ya kulungamitsidwa ndi yotsatira malangizo a zachilamulo. Pamene pali ntchito yofuna za chilamulo, timayesetsa kupeza munthu amene amadziwa za chilamulozo. Yesu ndi Yekhayo Amene Anakhoza ndipo Aki Wokhoza kutiimirira ife mu nkhani imeneyi ya zachilamulo. “Pamtanda wa Gologota Iye Adalipira dipo la mtundu wonse wa anthu. Potero Iye ali nayo mphamvu yotipulumutsa ife ku ku dzanja lamphamvu la m'dani wamkuluyo.”

Pamene asilikali ankakhoma misomali m'manja a Yesu, “Yesu Adali kubvekedwa mphamvu zokhala mkulu wathu wa zachilamulo pamaso pa Mulungu Atate.” Kulungamitsidwa, komwe ndi mbali yokhudza za chilamulo, ndikongokhudza mbali yathu yokhayo ya zachilamulo osati ife monga tiliri mu umunthu wathu. Pamene chigawenga chakhululukidwa chifukwa cha

zachilamulo, chigawengacho chimakhala chomasuka, komabe khalidwe lake ndi lauchigawengabe basi.

Mu njira yomweyi, kulungamitsidwa kumatanthauza kukhala wolungama kwaulere. Komatu sizikutanthauza chilungamo chochepetsedwa mphamvu. Palibe chimene nthawi, kukhalitsa, luso kapena ntchito zingathe kuchita kuonjezera ku mphatso yozizwitsayi. Yesu Adakhala padziko lino kwa zaka makumi atatu mphambu zitatu ndi theka ndipo adakwanitsa kukhala ndi khalidwe langwiro. Iyi ndiyo mphatso Yake yosaneneka ya kwa ife.

Tangoyeserani kuganiza motambasula kufikira mapeto ndipo mupeza kuti palibe chimene inu mungathe kuonjezerapo kumphatso yosaneneka ya Ungwiro Wake yopatsidwa kwa ife.

Apatu ndipamene chikhalidwe cha munthu chimayesedwa kuganiza kuti sitingathe ife kukhala angwiro pokhapokha titachitapo kanthu pa ife tokha. Inde, pali ntchito yolimpirako yomwe inu ndi ine tiyenera kuchitapo yomwe posachedwa tiyione, Chofunikira ndicho kudziwa kuti Mulungu Yekha ndiye Amene Angathe kuchita ntchito Yake Ya Umulungu, ndipo munthu naye achitenso ntchito yake ya umunthu. Nkosatheka Mulungu kuchita ntchito yomwe munthu ayenera kuchita, popanda kukolana ndi Lamulo La Iye Mwini, monganso kuli kosatheka munthu kuchita ntchito ya Mulungu, imene tikudziwa kale kuti sangathe.

Kuyeretsedwa – komwe ndi chilungamo cha Mulungu chopatsidwa kwa ife, ndi ntchito imene imatisiyanitsa ndi ntchito Yake. Nkhani ya Kuyeretsedwayi tiyikamba pa mutu ukubwera kutsogoloku.

Ndikupyolera mu kulungamitsidwa pamene ife tilandira chibvomerezo chakuti timasunga Malamulo a Mulungu. (Weren-gani Khristu Chilungamo Chathu, tsamba 99, *Review & Herald*, August 22, 1893.)

“Popeza tsono tayeresedwa olungama ndi chikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” Aroma 5:1. Yesu Khristu Samangondiyeretsa kokha, komanso amakhazikitsa mtendere pakati pa ine munthu wochimwa, ndi Mulungu, Mlengi wanga amene kwa Iye ine ndakhala oukira kwa nthawi zambiri. “Okhulupirirayo sikuti akufunsidwa kupanga mtendere wa iye mwini ndi Mulungu; izitu sizingatheke. Iyeyu ayenera kulandira Yesu Khristu monga mtendere wake, popeza pamene pali Khristu palinso Mulungu ndi mtendere.”

“... Chifukwa chisamaliro cha thupi chidana ndi Mulungu; pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu, pakuti sichikhoza kutero. Ndipo iwo amene ali m’thupi sangathe kukondweretsa Mulungu.” Aroma 8:7-8. Chisamaliro cha thupi ndi mau amene ayenera kuchititsa mantha chiwalo chirichonse cha mpingo kuti chiyambepo kuchitapo kanthu. Mosiyana ndi m’mene tiganizira, liwu loti chisamaliro cha thupi siliimira munthu wa m’dziko amene sadziwa Mulungu, komano munthu wa mumpingo amene amadziwa Mulungu, komano safuna kumudziwa Mulunguyo mwakuya.

Paulo akutiiza za makwerero atatu a moyo wa anthu. Makwererowa ndiwo: Umunthu wachibadwa, umunthu osamalira za thupi, ndi umunthu wa umulungu. 1 Akorinto 2:14,15, komanso 1 Akorinto 3:1. Tonsefe tiri pa limodzi la makwerero atatuwa. Umunthu wachibadwa ndiwo umene ife tinangotengera m’mene tinkabadwa. Umunthu wa umulungu ndilo khalidwe limene limapatsidwa kwa ife ndi Mulungu Mwini pamene ife tibadwanso mu uzimu ndi kukula mwa Khristu. Umunthu osamalira za thupi uli pakati pa umunthu wachibadwa ndi umunthu wa umulungu. Ndi khalidwe latsopano limene limapatsidwa kwa munthu pamene munthuyo abadwa mu Mzimu osati mwa thupi, komano opanda kukula.

“... Kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiro ndi wa chizindikiritso cha mwana wa Mulungu, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Khristu.”

Umu ndi m’mene Yohane akunenera pa Chibvumbulutso 3:14-22...simuli wozizira kapena wotentha...wofunda, osati wozizira kapena wotentha... Ndidzakulabvula mkamwa mwanga...”

“ Fanizo la kulabvulidwa mkamwa mwake liku-tanthauza kuti Iye sangaperekenso mapemphero anu kapena chionetsero chanu cha chikondi kwa Mulungu. Iye sangasindikize chiphunzitso chanu cha mawu Ake kapenanso ntchito yanu ya uzimu mu njira iriyonse. Iye sangapereke machitachita anu a chipembedzo ndi pempho lakuti chisomo chiperekedwe kwa inu.”⁹

Tonsefe timadziwa kuti pokhapokha mapemphero athu atadzozedwa ndi Mzimu wa Ambuye Yesu, Mulungu Sangatimvere.

“... Palibe munthu adza kwa Atate koma mwa Ine,” Yohane 14:6. Izi zikutipanga ife kukhala pa malo pamene tiyenera kupanga chisankho. Ichi n’chifukwa chimene Yesu Anati, “...Mwenzi utakhala wozizira kapena wotentha.” Chibvumbulutso 3:15. Mawu a pa Chibvumbulutso 3:18 akutsatana ndikuti, “Ndikulangiza ugule kwa ine golidi woyengeka m’moto...” Tidziwe ichi kuti munthu amagula golidiyu popanda ndalama iriyonse, komanso popanda mtengo. Yesaya 55:1.

Wina adati “ Chipambano chimabadwa m’ mabvuto.” Mabvuto athu ndiko kuona kupusa kwa kukhala wofunda ndi kuona kufunikira kwake kopeza golide amene Mulungu wathu atilangiza ife kupeza. Apatu pafunika nzeru, popeza ambiri adafikira mfundo iyi komano anatsatira njira ya satana. Iwo amaganiza kuti akuchoka m’ mabvuto awowo, chikhalirenicho satanayo akuwatsogolera m’ mabvuto akuya.

“Kuyambanso mwatsopano”, “Kutsimikizika kuchita bwino,” “Kukhala wokhulupirika, izi n’ zabwino ndithu, komatu sizingathe kusintha moyo.

“Monga chotupitsa pamene chisanganizidwa ndi mkate, chimagwira ntchito yake kuyambira mkati kufikira kunja, chomwechonso zimadalira kukonzanso mkati mwa mtima wathu kuti chisomo cha Mulungu chithe kusintha moyo. Kusinthika kwa kunja kokha nkosakwanira kutiyanjanitsa ife ndi Mulungu. Alipo ambiri amene amayesetsa kusintha pongokonza khalidwe ili ndi ilo loyipa, naganiza kuti potero akhoza kukhala akhristu, ukutu n’ kuyamba malo olakwika. Ntchito yathu yoyamba ndiyo kukonza mtima.”¹⁰ (*Selected Messages*, bukhu 1, tsamba 353.)

Chisankho chomwe tiyenera kupanga ndicho kulola Mtima Wa Yesu kukhala Mtima wathu. “Mukhale nawo mtima mkati mwanu umene unalinso mwa Khristu Yesu.” Afilipi 2:5

“ Mulungu Wakonza njira yakuti ife tikhoza kukhala monga Iye, ndipo Iye Adzakwaniritsa ichi kwa onse amene saonetsera chifuniro choukira ndi kusokoneza chisomo Chake.”

“ Ndi chikondi chosaneneka, Mulungu wathu Watikonda, ndipo chikondi chathu chimakhala chochangamuka kwa Iye pamene tikuganizira mwakuya utali, ufupi ndi kuya ndi kutalika kwa chikondi chake chimene chiposa chidziwitso chonse. Mwa bvumbulutso la kukongola kwa chikondi cha Khristu, mwa chidziwitso cha chikondi Chake choonetsedwa kwa ife tikali anthu ochimwa, mtima woumitsitsawo umasungunuka ndi kumizidwa mchikondi chake ndipo wochimwayo amasinthika nakhalanso mwana wa Kumwamba. Mulungu sagwiritsa njira zokakamiza; Chikondi ndicho njira yomwe Iye Amagwiritsa kuchotsa tchimo mu mtima. Mwa chikondi Iye Amasintha kunyada kukhala kudzichepetsa, komanso udani ndi kusakhulupirira kukhala chikondi ndi chikhulupiriro.”¹¹

Ndi chikhulupiriro monga chotengeramo, komanso chikondi monga mphamvu Yake, zonsezo zochokera kwa Khristu, tikhoza kuona kuti ntchito yonse ndi Yake. Atamandike Mulungu! Ndizake mwa mphamvu ya kutigulanso mwa imfa Yake ya pamtanda. “Pamtanda wa Gologota Iye Adalipira dipo la mtundu wa anthu. Potero Ali nawo ulamuliro opulumutsa ku mphamvu ya mdierekezi wamkuluyo.” Izi zikutionetsera poyera kuti Khristu adakonzeratu zonse zokhudza nkhani ya zachilamulo zimene Lamulo Langwiwo La Mulungu Limafuna, Iyeyo Asadabwere kudzapulumutsa munthu ku dzenje la tchimo limene munthuyo adagweramo. Pakuti Khristu ndiye “... Mwana wa nkhosa wophedwa kuyambira makhazikidwe a dziko lapansi.” Chibvumbulutso 13:8.

Tsopano tidziwa kuti njira ya Mulungu imatsekeratu pakamwa mfundo ya satana yoti munthu ndi wake chifukwa munthuyo anachimwa. Taonani, kudala kotani nanga kwa mphatso ya mtengo wapatali yomwe Mulungu Apereka kwa munthu, pamene Mulungu Akubwezeranso chifuniro chimene Adamu adachitaya panthawi yomwe adagwa! Mphatso iyi ya kubwezeretsedwanso kwa chifuniro ndiyo imatipanga ife kusankha kukonda, kutumikira ndi kumvera mbuye wina ngakhale tikudziwa kuti tiribe mphamvu yokwaniritsa chomwe tasankhacho.

Chisankho chimenecho chidamasula Mulungu kuchita ntchito Yake yolungamitsa mwachilamulo, ndikupereka kwa ine, munthu wochimwane, Khalidwe Lake Langwiro lomwe adalikhazikitsa padziko pano, atazungulidwa ndi mayesero oopsa a satana. Ichi n'chifukwa chake zolemba za mlandu wathu zimaoneka motere, "Monga ngati kuti sindinachimwepo," ndipo palibenso china chirichonse chimene satana angachitepo pa nkhani iyi. N'chifukwa chake, "Ngati Mwana Adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu."

Ndibwerezense: Chotengeramo chake ndicho chikhulupiriro, mphamvu yake ndiyo chikondi, njira yake ndiyo nzeru ya chipulumutso. Litamandidwe Dzina Lake! Izi nzokhazikika ndi chilamulo kwina kulikonse padziko lonse lapansi. Sizachilamulo zokha, komanso zikupanga magwero a chimwemwe chenecheni ndi chisangalalo cha dziko lonse lapansi.

Mafunso othandizira kuchita zomwe mwaphunzira pa mutuwu.

A: Fufuzani

Ndi chiyani chimene Mulungu Amakhulupirira kuti chidzachitika mwa wokhulupirira amene Iye Wamulungamitsa? Ndi 'makwerero atatu ati a moyo wa munthu' amene Mtumwi Paulo akufotokoza?

B: PANGANI KUKHALA MOYO WANU!

"Chotengeramo ndi chikhulupiriro, mphamvuyo ndi chikondi, kapangidwe kake ndi nzeru ya chipulumutso, ndipo Liyamikike Dzina La Ambuye, ndizokhazikika m'chilamulo padziko lonse. Sizachilamulo chokha, komanso ndi magwero a chimwemwe chenicheni ndi chisangalalo cha padziko lonse."

Pemphani ndi pemphero kuti izi zikhale moyo wanu, . . . ndi KUZIPANGA KUKHALA MOYO WANU!!

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndikusintha kotani komwe kudzaoneke m'moyo wanga pamene Ambuye Ayankha pemphero langa.)

Mabukhu Omwe agwiritsidwa ntchito:

- 1 Thoughts From the Mount of Blessing. Tsamba 94.
- 2 Mapazi Opita Kwa Khristu (Steps to Christ) Tsamba 62.
- 3 The Review and Herald, September 16, 1902, Khristu Chilungamo Chathu, Tsamba 104.
- 4 Mafunso a paziphunzitso, (Questions on Doctrine) Tsamba 672.
- 5 Khristu Chilungamo Chathu, (Christ our Righteousness), Tsamba 35.
- 6 Mafunso a paziphunzitso, (Questions on Doctrine), Tsamba 672.
- 7 Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire Of Ages), Tsamba 744.
- 8 Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 395.
- 9 Maumboni, (Testimonies), Bukhu 6, Tsamba 408.
- 10 Mafanizo a Yesu, (Christ's Object Lessons), Tsamba 97
- 11 Thoughts from the Mount of Blessing, Tsamba 76, 77.
- 12 Mafunso a paziphunzitso, (Questions on Doctrines), Tsamba 672

3.

KODI UNGWIRO

Ndi Wabwino Bwanji?

“Mulingalirani chotsutsana ndi Yehova? Iye Adzatha psiti; nsautso sidzaukanso kachiwiri.” Mau awa a m’baibulo ndi amodzi mwa malonjezano ozizwitsa amene akupezeka m’baibulo.

Mau a Mulungu Akunenanso kuti, “Ngati Mwana Adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu.” Yohane 8;36. Lonjezano ili lozizwitsa lakuti munthu sadzagwanso mu uchimo lidzaonetsedwa mu mtendere uwu Umene Iye Atipatsa ife. Apa tikuonetsedwa ku nthawi ya kutsogolo, pamene, ngakhale ndi m’maganzo momwe tchimo silidzaonekeranso.

Apatu, maganzo athu ndi akuti, pamene tchimo lidzachokeratu, sipadzakhalanso ganizo lililonse lofuna kuchimwa. Potero, kumvera kudzangokhala chikhalidwe cha munthu. Umu ndi m’mene zinalili kumwambako nthawi yomwe tchimo linayamba. Ndingokukumbutsani kuti munthawi ya mtambasale ndi chipambano ndiyo nthawi imene munthu amatayana ndi Mulungu wake. Kodi umu sindimomwe ulili mpingo lero? “Wolemera, wachuma,” koma wopanda chikondi.

Nangano Mulungu Akukwanitsa bwanji kupanga lonjezano lotero? Pa Malaki 4:1 Mulungu Akuti Moto wa n’ganjo yotentha umene udzayeretsa dziko, ndiwo umene udzachotseratu tchimo, osasiya muzu kapena nthambi. Pa Yohane 15:5 Yesu Akuti, “Ine Ndine Mpesa, inu ndinu nthambi zake....” Apatu Yesu Ankalankhula kwa ophunzira Ake, pamene m’modzi wa iwo adadzichotsamo yekha mwa khumi ndi awiriwo. Kodi sitingathe kunenanso kuti satana ndiye muzu umene nthambi za dziko lapansi likumerapo? Zonsezi zidzaotchedwa ndi moto.

Koma tikuyenera kuyan’gana mwakuya zomwe lonjezano

la mulungu likunena pa Nahumu 1:9, lemene likuti Mdaniyo sadzaukanso kachiwiri. Mdani woyamba adauka podziganizira iye yekha.

Pakhala pali kuthekera mu ufulu woperekedwa ku chilengedwe cha Mulungu, kwakuti muzu wa tchimo ukhoza kuphuka. Mulungu Angakhoze bwanji kulengeza kuti palibe ndi m'modzi yemwe wa owomboledwa Ake, kapena wina wochokera ku mayiko omwe sadachimwepo, ngakhalenso mgelo wa kumwamba, sadzaukiranso, ngakhale mu lingaliro lomwe? Chozizwitsa cha zozizwa nanga! Iyitu idzakhala mphamvu ya nzeru ya chipulumutso mu chilengedwe chonse cha Mulungu! Mulungu, Amene Amadziwa za mtsogolo, Watitsimikizira kuti izi zidzathekadi.

Ntchito Ya Mulungu Yafika kale ku mapeto, kwa iwo amene akhala kumwamba. Mayiko omwe muli zolengedwa za Mulungu pamodzi ndi angelo akhala akukondwerera kuti aomboledwa ku mphamvu ya tchimo ndi kwa satana. Chibvumbulutso 12:12. Komabe, dziko lathu lino, lomwe ndi kongoyembekezerako chabe, pamodzi ndi onse okhalamo, akudziwa bwino zakuti satana ndi angelo ake adakalipobe.

Ngakhale izi ziri chomwecho, kwa enafe tchimo silidafkirebe poipitsitsa. Khalidwe latchimo lakupha silinatifikirebe. Timaganiza kuti tidzangolisansa ngati fumbi titangotsala pang'ono kulowa kumwamba.

“Ungwiro wa angelo udalephera kumwamba. Ungwiro wa umunthu udalepheranso mu Edene...Chiyembekezo chatu chokhacho ndicho kukhulupirira mwakuya m'mwazi wa Iye Amene Akhoza kupulumutsa kotheratu iwo onse amene adza kwa Iye. Kupulumutsa kotheratu kukutanthauza kupulumutsidwa ku undekha, osati mu undekha. Khaliwe loononga la uchimo limaonetsedwa pamene ife tidzikhulupirira tokha m'malo mokhulupirira Mulungu.

Kodi tidziti ndicho chifukwa chake lero dziko lapansi aliyense akungofuna kuti maganizo ake okha ndiwo amveke? Mayiko akufuna ufulu wawo. Mizinda ikuluikulu, mizinda ing'onoing'ono ndi midzi yomwe onse akufuna kudziimira pa-okha. Nawo mabanja akungosweka mwa kanthawi kochepe. Ana akungodzichitira zofuna iwo eni, potsatira ufulu wakalankhulidwe, womwe wakula mu dziko lapansili.

Satanatu akuchita ntchito yake mwaluso. Chotero undekha

ndi kudzimvamo zapangidwa kukhala ngati yankho ku mabvuto a anthu. Tangoganizani m'mene izi zinayambikidwira kumwamba kalekalelo. Ifetu sitingathe kusunga undekha, natiganizira kuti tikalowa mu ufumu wa Mulungu. Ngati inu ndi ine tidzafike pa chiyero chenicheni, zidzaimira kulekana nawo undekhawu ndi kulandira moyo wa Yesu Khristu.

Maganizo a undekhawa samangotilepheretsa kokha kulowa kumwamba, komanso, "Pamene undekha ulowerera mu zintchito zathu, ndiye kuti choonadi chimene ife timawauza anzathu, sichinatiyeretse ife eni ngakhalenso kukonza mitima ya ife eni. Umunthu sungatiikire ife umboni wakuti ife ndife zotengeramo zoyenera zogwiritsidwa ndi Mbuye.

Nangano tingamasuke bwanji ku undekhawu? Ahebri 12:6 akutiya, "Pakuti iye amene Amkonda Amlanga." Cholinga ndicho kuchotsa muzu wonse woipa umene ungabweretsa bvuto.

"Penyani musakane wolankhulayo..." Ahebri 12:25. Nzapafupi kubisa umunthu ponamizira kuti sitimumva Mulungu pamene Iye Atiyankhula.

Mulungu Sanatilonjeze kuti tidzayamba tamvetsetsa zonse bwino lomwe tisanayambe kutsata kuitana kwake. Ahebri ndime 11 akutionetsera mndandanda wa okhulupirira amene sanayambe amvetsetsa kaye chifuniro cha Mulungu, komabe iwo adangomvera. Abele, Enoke, Nowa, Abrahamu, ndi ena a iwo owerengeka. Ena akhoza kuchitchula chikhulupiriro choterechi kuti ndi chakhungu, komano ndikukumbutseni kuti ana a Mulungu "...amayenda mwa chikhulupiriro, si mwachionekedwe." 2 Akorinto 5:7

Kodi ungwiwo ndi wabwino kotani? Ungwiwo sindiko kufikirapo pa ubwino, komano ndiko kumukhulupirira Mulungu kotheratu, kopanda kukaika kulikonse kapena kufunsa mafunso. Linali khalidwe lotereli lomwe linali ndi Yobu, lomwense lina-pangitsa Mulungu kunena kuti Yobu anali "...munthu wangwiwo ndi oongoka..." Yobu 1:8.

Kuyamikiridwa kotereku ndi Mulungu Mwini kudabwera ngakhale Yobu akuikira umboni mu Yobu 42:6 kuti, "...chifukwa chake ndekha ndidzinyansa ndi kulapa M'fumbi ndi mapulusa." Nayenso Nowa anaikidwa umboni wakuti, "...Wolungama...ndi wangwiwo..." Genesis 6:9. Komano monga Loti, Mose, Abrahamu, Davide ndi Solomoni, mbiri zao molingana ndi Baibulo zinali zosakhala bwino.

Ungwirowo ndi wabwino bwanji? Zimayendera.

“Monga chotupitsa pamene chisanganizidwa ndi mkate chimagwira ntchito kuyambira mkati kufikira kunja, chomwechonso zikudalira kukonzanso kwa mtima kuti chisomo cha Mulungu chithe kusintha moyo. Palibe kusintha kwa kunja kumene kuli kokwanira kutibweretsa ife m’chiyanjano ndi Mulungu wathu. Alipo ambiri amene amayesetsa kukonzanso pokonza khalidwe loyipa ili ndi ilo, naganiza kuti munjira yotereyi adzatha kukhala akhristu, komatu oterewa akuyamba pa malo olakwika. Ntchito yathu yoyambirira ndiyo kukonza mtima.”⁴

“Munthu amene amangoyesetsa kusunga Malamulo A Mulungu chifukwa wafunsidwa kutero – sadzafikira chimwemwe chomwe chimadza ndi kumvera. Wotereyu samvera. Pamene Malamulo A Mulungu Ayesedwa kukhala katundu olemera chifukwa akutsutsana ndi chifuniro cha munthu, pamenepo tidzadziwa kuti moyowo sindiwo moyo wa Khristu. Kumvera kwenikweni ndi ntchito yoyambira mkati. Imayambira ku akasupe a chikondi cha chilungamo, chikondi cha Lamulo La Mulungu. Gwero la chilungamo chonse ndilo kumvera Momboli wathu. Izi zidzatithandiza ife kuchita zabwino, chifukwa ndi zabwino – popeza kuchita zabwinoko n’kokondweretsa Mulungu.”⁵

Mulungu Ali nayo njira imene ife tingakhalire angwirowo – osati mwa mphamvu za umunthu,” Kuti wina angadzikuze.” Ungwirowo ndi mphatso yozizwitsa yochokera kwa Yesu Khristu yoperekedwa kwa onse okhulupirira.

“Lamulo limafuna chilungamo, - moyo wachilungamo, khalidwe langwirowo; izi munthu sangapereke. Munthu sangafikire chiyang’aniro cha Lamulo La Chiye-ro La Mulungu. Komano Khristu, pofika padziko lapansi monga munthu, anakhala moyo wachiyero, nakhala nalo khalidwe langwirowo. Izi Amazipereka monga mphatso yaulere kwa onse amene amlandira Iye.”⁶

Ungwiro ndi wabwino bwanji?. Ungwiro ndi kufikira chi- yang’aniro choonetsedwa ndi moyo wa Yesu nthawi ya kukhala kwake pano pa dziko. Moyo Wake unaonetsera kukhulupirira kwathunthu, kudalira kotheratu pa Mulungu Atate pokwaniritsa chifuniro cha Mulungu.

Tsopano Iye Anamaliza ntchito Yake – Anamaliza zonse m’ malo mwa ife podziwa kuti sitikadatha patokha kuchita izo zimene Lamulo lifuna. Nangano mbali yathu ndiyotani? Kugwiritsa ntchito chifuniro chathu! Kusankha kum’ khulupirira! Ngakhale tikudziwa kuti sitingathe kuchita zomwe tasankha kuchita. Posankha, timatsegula khomo kuti Khristu Achite ntchito mwa ife imene ife patokha sitingathe kuichita. Chotero, mwana wa Mulungu amasankha kukhulupirira mu zinthu zonse.. Potero iye adzalola Khristu kuti Amuthandizire kumukhulupirira, ndi- kusalola kuti zomuzungulira zibweretse chikaiko mu njira yomwe Khristu Akugwirira ntchito Yake.

Ngati tikana kukaikira njira zomwe Iye Agwirira ntchito mwa ife, m’ malo mwake kungokhulupirira kuti Iye Akudziwa chomwe Akuchita, pamenepo tidzadziwa chinsinsi cha Khristu cha chi- pambano Chake – ngakhale zinthu zikuoneka kuti nzosapambana.

Nditseke ndimeyi ndi mawu awa amene adalemba m’ modzi mwa anthu amene anakhala moyo umene iye adaukhulupirira:

“Atate mwini Adamukuta Yesu Khristu, ndipo palibe china chirichonse chidamugwera Iye pokhapokha icho chimene chinaloledwa mwa chikondi chakuya cha Mulungu, kuti chikhoza kukhala mdalitso ku dziko. Awa adali magwero ake a chithonhozo, ndiponso akhoza kukhala magwero athu. Iye amene wakutidwa ndi Mzimu wa Khrisu akhala mwa Khristu..Choipa chotumizidwa kwa iye chimafikira kaye kwa Mpulumutsi, amene amamuzinga ndi kupezeka kwake. Chirichonse chom’ gwera iye chimachokera kwa Khristu. Iye safunikiranso kuti adzitetzeze ku choipa, popeza Khristu ndiye Womutetezera. Palibe china chirichonse chingamukhudze wotereyu pokhapokha chitaloledwa ndi Ambuye Mwini, ndipo tidziwa kuti zonse zololedwa ndi Ambuye, ‘zinthu zonse zithandizana kuwachitira ubwino kwa iwo amene akonda Mulungu.’ Aroma 8:28.”⁷

Ungwiro ndi wabwino bwanji? Ubwino wonse womwe ife tidzakhale nawo ndiwo kukhulupirira kotheratu mwa Yesu. “Kupyolera m’kuthekera kwa Yesu, kupyolera M’chilungamo Chake, chopatsidwa kwa ife mwaulere, tiyenera kufikira ku chiyero cha khalidwe la mkhristu.

Mafunso othandiza kumvetsetsa zomwe mwawerenga pa mutu uwu.

A: FUFUZANI

Kodi pamene Yesu “Adzakupangani inu mfulu,” kumvera kudzangobwera “mwachibadwa” kwa ife, ndikuti sitingachimwenso?

Nangano, ‘ungwiro’ umatanthauzanji?”

B: PANGANI ICHI KUKHALA MOYO WANU!

“Kudzera mu kuthekera kwa Yesu, kudzera mu chilungamo Chake, choperekedwa kwa ife mwa chikhulupiriro, tikuyenera kufikira ku ungwiro wa khalidwe la Yesu” Pemphani kuti ichi chikhale mbali ya moyo wanu...ndipo **KHALANI MOYO WOTERO!!**

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Padzakhala kusintha m’moyo wanga pamene Ambuye Adzayankha pemphero langa).

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

- 1 The SDA Bible Commentary, bukhu 5, Tsamba 1132, Zizindikiro za Nthawi, (Signs of The Times, Dec,30, 1889).
- 2 Thoughts from the Mount of Blessing, Tsamba 143.
- 3 Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), bukhu 1, Tsamba 405.
- 4 Mafanizo A Khristu, (Christ Object Lessons), Tsamba 97.
- 5 Mafanizo A Khristu, (Christ Object Lessons), Tsamba 97,98.
- 6 Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire Of Ages), Tsamba 762.
- 7 Thoughts from the Mount Of Blessings, Tsamba 71.
- 8 Maumboni, (Testimonies), bukhu 5, Tsamba 744.

4.

Chipembedzo **CHAPAMANDA**

“Kapena kodi simudziwa kuti ife tonse amene tinabatizidwa mwa Khristu Yesu tinabatizidwa mu imfa Yake?” Aroma 6:3. Akhristu ambiri amene anabatizidwa mu njira yomiza m’madzi, amadziwa bwino tikamati kubatizidwa m’dzina la Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Komano ndi ochepa okha amene amadziwa kuti ubatizo umakhala mu imfa ya Yesu.

Paulo akuti, “Chifukwa chake tinaikidwa m’manda pamodzi ndi Iye mwa ubatizo kulowa mu imfa; kuti monga Khristu Anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemerero wa Atate, chotero ifenso tikayende m’moyo watsopano.” Aroma 6:4

Ubatizo umayimira imfa, imene ikadakhala itachitikiratu m’moyo wa munthu wokhulupirira. Imfa yomwe tikukambayi ndiyo imfa ya khalidwe lomwe tinabadwa nalo. Khalidwe lakale lobvundali ndilongoyenera imfa basi. Zotsatira za chinthu chakufa ndizo kukwiriridwa kopanda mdzukiro. Paulo akufotokoza motere, “Podziwa ichi kuti umunthu wathu wakale unapachikidwa pamodzi ndi iye, kuti thupilo la uchimo likaonongedwe, kuti ife tisakhalenso akapolo a uchimo.” Aroma 6:6

“Mosakaikila, bvuto lalikulu ndi anthu okhulupirira ndilakuti amafuna kukhala moyo wa Yesu, asanayambe kaye kufa imfa ya Yesu. Iwo amakhala ndi ganizo lakuti Iye Anafa n’cholinga chakuti ife tisafe, potero, mwa chikhulupiriro mwa yesu amayembekezera kuti adzakhala moyo wopanda kufa... Paulo akuti, ‘Ndipo iwo amene ali m’thupi sangathe kukondweretsa Mungu,’ Aroma 8:8. Ndipo “Koma iwo a Khristu Yesu

Adapachika thupi, ndi zokhumba zake, ndi zilakolako zake. Agalatiya 5:24.”¹

Kumvetsetsa kwa kufunikira kwa nkhanayi nkofunika ngati tingafune chipambano choyenda ndi Ambuye.

“ Nkhani yobadwanso mwatsopano ndi yosowa kwambiri mu m’bawo uno wa dziko, Ichi n’chifukwa chake lero m’mpingo muli mpungwepungwe wochuluka. Anthu ochuluka amene amatchedwa akhrisu sanayeretsedwe ndipo alibe chiyero. Iwowa anabatizidwa koma adangokwiridwa asanafe. Chotero sanaukebe ku moyo watsopano wa mwa Khristu.”²

Chiganizo chotsatirachi chinalembedwa m’chaka cha 1897 komabe chikukhudzana ndi nthawi yathu lero. Paulo akunena moonjezera motere, “Chifukwa chake ngati munthu aliyense ali mwa Khristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano.” 2 Akorinto5:17.

N’chifukwa chiyani khalidwe lakale liyenera kufa? Yesu Akuyankha kuti, “Pakuti iye amene afuna kupulumutsa moyo wake adzautaya: koma iye amene ataya moyo wake chifukwa cha ine adzaupeza.” Mateyu 16:25. Zikuoneka ngati palibe chomwe tingachite kuchiza khalidwe lakaleri la uchimo. Khalidwero ndi longoyenera kufa basi. Ngati pafunika moyo watsopano, moyo wakalewo ukuyenera kufa basi.

Wolemba mabuku wina, dzina lake Meade MacGuire akutipatsa ife maganizo akuya omwe ali otithandiza kupyolera mu bukhu lake lotchedwa Mtanda Wake ndi Wanga, (His Cross and Mine).

“Pali kusiyana kwakukulu pakati pa machimo ndi tchimo. Ambiri amapeza mabvuto ochuluka m’moyo wao wa chikhristu chifukwa chosatha kulekanitsa pakati pa mawu awiriwa. Pansipansi pa kusaweruzika kwathu komwe timachita nthawi ndi nthawi pali phata la tchimo komwe zonse zichokera. Ngakhale zochita zathu zonse zauchimo zinakhululukidwa, timapitirira kumangochimwirachimwirabe. Pakufunika china chachikulu

kuti chichitikepo koposa kungokhululukidwa machimo kokhako.”³

Mlembi MacGuire akupitiriza motere:

“Apa pafunika kusiyanitsa pakati pa tchimo ndi machimo. Machimo, mchitidwe wa kusamvera, kuswa Lamulo Lachiyero La Mulungu, zonsezi Mulungu Ali wolola kutikhululukira kudzera mwa Yesu Khristu poyankha pemphero lolapa ndi lachikhulupiriro. Koma Tchimo, Mulungu Sangalikhululukire.

Tchimo ndilo khalidwe limene limatipangitsa ife kusamvera Lamulo La Mulungu. Chibadwa chatu chomwe timabadwa nacho m’dziko sichingasithe, monga momwe tiwerengera mawu a Mpulumutsi wathu: ‘Chobadwa m’thupi chikhala mthupi; ndi chobadwa mu uzimu ndi mzimu.’ Njira yokhayo yomwe tingathane nalo khalidwe loyipali ndiyo imfa. Njira yokhayo yolandirira khalidwe labwino ndiyo kubadwanso.”⁴

Imfa ndi njira yokhayo yothana ndi khalidwe loyipa.

Umu ndi momwe imfa imachitikira m’moyo wa okhulupirira. Zilakolako ndi zokhazikika m’thupi ndipo zimayesetsa nthawi zonse kugwira nthcito. Mawu akuti thupi, kapena zakuthupi, kapena zilakolako, onsewa akuimira zilakolako za uchimo. Ife tikulamulidwa kupachika zilakolako zimenezi za tchimo, ndi zonse zomwe tizikonda, ndi zoutsa chibaba. Nanga tingachite bwanji kuti izi zitheke? Kodi Izi zikhoza kutheka pongozunza thupili? Ayi ndithu. Chomwe ine ndiyenera kuchita ndicho kupheratu mayesero onse a tchimo. Kupha ganizo limene limabwera la uchimo. Ndilole kuti ganizo lirilonse lilamulidwe ndi Yesu Khristu.⁵

Italics missing

Mu Aroma mutu 6, Paulo akufotokoza kuti imfa ya khalidwe lakale la uchimo ndiyo yeneyeni. Pa ndime 11 tikuzidwa kuti tikhale ofafa ku uchimo koma amoyo kwa Mulungu. Apa ndipamene akhristu ambiri amalephera. Nzophweka kungokhulupirira izi kuti nzophunzitsidwa ndi odziwa malembo, komano kuzichita m’moyo wathu n’kobvuta ndithu.

Satana ndiye amene amabweretsa kuganiza kotereku. Pamene Mulungu Atchula mfundo, satana amatsutsa, kuikhotetsa nga-

khalenso kuisintha kumene kuti zimukomere. Satana amadziwa kuti ngati mkhristu atakhulupiriradi kuti khalidwe lake lakale lafadi, apo ndiye kuti mphanvu yake ya satanayo yathyokadi.

Pofuna kutsindika mfundo yake yakuti sipafunikira kufa mu uchimo, satana amayesetsa kumupanga mkhristu kuti adzikhala moyo wa momwe munthuyo akumvera, osati mwa chikhulupiriro. Potero amapangitsa wokhulupirirayo kugwa mu uchimo. Kenakono nkumamutsutsa kuti wachimwa. Ndiyeno amagwiritsa ntchito kulephera kwa munthuku monga chisonyezo chakuti umunthu wakalewo sudafebe. Satanayu amangogwiritsa chabe njira za kaganizidwe ponena kuti, “ngati umunthu wakalewo ukadakhala wakufa, iwe sukadayesedwa mu uchimo.”

Apatu nkofunika kuti mkhristu asiye kuyesetsa kugwiritsa maganizo ake podzera mu ziyangoyango za momwe iye akumvera. M'malo mwake mkhristuyo ayenera kukhulupirira Mawu Mulungu.

Ngati mkhristu wadzipereka yekha kwa Mulungu, ayenera kudziwa kuti, “...Koma iwo a Khristu adapachika thupi ndi zokhumba zake, ndi zilakolako zake.” Agalatiya 5:24. Tiyenera ife kuzama m'mau a Mulungu ndikusiya kumalimbana ndi machenjerero a satana ngatidi tikufunitsitsa kukhala akhristu. Mulungu Akuti khalidwe lanu lakale la uchimo liri lakufa ngakhale mudagwa mu uchimo poyesedwa. Komano satana akuti ayi, khalidwe lanu silinafe. Tsopano funso loti tiyankhe sindilo lakuti timakhulupirira chiyani, komano tiyankhe kuti timakhulupira ndani?

Nangano ndingakwanitse bwanji izi? Werenganinso mutu uja woyambirira wa bukhuli ndipo kumbukirani kuti satana ndiye amene amalamulira umo momwe ife timvera m'thupi. Ziganizo zotsatirazi zikutsimikiza nkhanayi:

“Tsiku ndi tsiku tikuyenera ife kudzipereka kwa Mulungu ndikukhulupira kuti Iye Amalandira nsembe popanda kuyang'ana ngati ife tafikirapodi pa chidzalo cha chikhulupiriro chathu. Chikhulupiriro, ndi m'mene timamvera m'thupi mwathu, ndi zinthu ziwiri zosiyana monga Kum'mawa kusiyanira ndi kumadzulo. Chikhulupiriro sichidalira momwe ife timvera m'thupi. Tikuyenera ife nthawi zonse kulirira kwa Mulungu mu pemphero.

Kaya tikuchita kumva motani m'thupimu, tiyeni tikhale moyo wa pemphero ndi kusiya zonse kwa Iye. Chitsimikizo chathu ndi Mawu a Mulungu, ndipo ngati ife tapempha, tiyenera kukhulupirira osakayikanso.”⁶

Kuti ife tione m'mene kulili kobvuta kumvetsetsa nkhanayi ya chikhulupiriro ndi momwe tikumvera m'thupi, tiyeni tiganizire motambasula ganizo lotsatirali:

“... mulungu Akuyenera kutumikiridwa monga m'mene Iye Alili, osati chifukwa cha m'mene ife tikumvera m'thupi ayi. Tisamange mtolo umodzi chikhulupiriro ndi momwe ife tikumvera. Ziwirizi nzosiyana ndithu. Chikhulupiriro ndi chathu chomwe ife tiyenera kuchita nacho. Chikhulupirirochi ife tiyenera kuchita nacho ndi kuchisunga. Khalani moyo wokhulupirira, ndi wokhulupirira nthawi zonse. Chikhulupiriro chanu chigwiritse mdalitsowo, ndipodi mdalitsowo udzakhala wanu. M'menetu inu mumvera m'thupi, ndi zosiyana ndi chikhulupiriro choterechi. Pamene chikhulupiriro chibweretsa m'dalitsowo m'moyo wanu, ndipo inu musangalala chifukwa cha m'dalitsowo, sichikhalanso chikhulupiriro komano kumva za m'thupi.”⁷

Chiganizo chomalizirachi mu ndime yangothayi sichophweka kuchimvetsetsa. Chonde, chiwerengeninso. Tsopano tiyenino tionenso mwakuya. Taona kale kuti chikhulupiriro, ndi m'mene umvera munthu m'thupi mwako, ndi zoyandikana kwambiri. Tikhozanso kunena kuti kukhala m'chikhulupiriro kumafunika kukhala tcheru, kuti tisangokhala ndi m'mene timveram'thupi ife weni.

Chitsanzo chimodzi cha m'baibulo chikhoza kutithandiza kumvetsetsa izi. Tikamawerenga bukhu la Luka 10:17, timamva kuti, “Ndipo makumi asanu ndi awiri aja anabwera mokondwera nanena, Ambuye, zingakhale ziwanda zinatigonjera ife m'dzina lanu.” Tangoganizirani chimwemwe chomwe akuphunzirawa anali nacho atangobwera ku ntchito yomwe anatumidwa. Iwo anali asanamvepo n'kalelonse umo m'mene ankamvera pa nthawiyo. Chimwemwe chawo chidali choonekera chifukwa chikuchita kutchulidwa.

Tsopano tamvani momwe Yesu Mwini Adawayankhira mu ndime 18: “Ndipo Anati kwa iwo, Ndinaona satana ali nkugwa ngati mphenzi wochokera kumwamba.”

Kuyankha kodabwitsa nanga! Ndikutha kuona nkhope za ophunzira aja, ndiganiza inunso mukutha kuona m'mene zinka-onekera, sichomwecho? Ndikukhulupira kuti panalitu zokambakamba pakati pa azibambo amenewa. “Mwinatu Ambuyewa Sanathe kumvetsetsa zomwe ife timatanthauza. Nangano bwajji Akuoneka achisoni Ambuyewa? Sindikutha kuwamvetsetsa. Nkuthekanso kuti mwina ena a makosanawa adalimba mtima kumufotokozera Yesu zomwe iwo amatanthauza.

Komatu Yesu Amayankha molingana ndi kuzama kwa chidziwitso komwe Iye Anali nako komwe iwo sankakudziwa. Maganizo a Yesu Adabwerera m'mbuyo mwenimweni ku nthawi imene lusifala adagwa kuchokera kumwamba, ndipo apa Iye Ankatanthauza kuti, “Ndinaona mzimu womwewo womwe unali mwa satana kalekalelo, ndipo tsopano mzimu womwewo ukuonekeranso pano.” Kwa satana kudapatsidwa mwayi wokhala ndi mphamvu zambiri. Iyeyu adakondwa ndi mphamvuzi naiwala m'dalitso woposa wa chiyanjano chake ndi Gwero la mphamvuzo. Mawu ofunikira amene akuonetsera choonadichi ndiwo akuti “ziwanda zinatigonjera ife.”

Tamveranino ndime 19 ndi 20: “Taonani, Ndakupatsani ulamuliro wakuponda pa njoka ndi zinkhanira ndi pa mphamvu iriyonse ya m'daniyo; ndipo palibe kanthu kadzakuipsani konse. Koma musakondwere nako kuti mizimu idakugonjerani, koma kondwerani kuti mayina anu alembedwa m'mwamba.”

Dalitso lalikulu Loperekedwa ndi Mulungu – Dalitso limene linachotsa moyo wa Mwana Wa Mulungu - linachotsedwa ndi kuikidwa pambali. M'malo mwake, ganizo lomwe lidadya mtima linali ganizo lochotsa ziwanda basi. Mtanda wa Gologota unali dipo lalikulu loperekedwa kuti mayina athu alembedwe m'mwamba. Mphamvu yochotsa ziwandayo sikadachita kutengera kuti Yesu Adzachite kutifera. Nthawi zambiri ife timangoganzira za zozizwa zomwe zingabwere m'moyo wathu kufikira chosowa chathu, chikhalirenicho tiwala za Mphatso yaikulu ya Mulungu Yotilola ife kukhala ana a banja Lake, “... Pakuti tiri ziwalo za Thupi Lake.”

Popeza tsono taona bvuto longokhalira momwe ife timvera, tiyenino tione kuti nanga tingatani kuchita nalo bvutoli. Kodino

timangokulukuta mano, osadziwa chochita? Kapena timangokhala nazo ndikuganiza kuti zidzachoka zokha? Kodi ndibwino kulankhulapo kuti zitichoke kumtimaku kuti tipepukidwe? Izitu ndi zimene anthu ambiri amaudindo awo angagwirizane nazo.

Maganizo athu onsewa akhoza kutha pongoyan'gana gwero la maganizowa. Tisaiwale paja kuti Mulungu Amagwira ntchito koyamba ndi mtima wa munthu, (maganizo a munthu). Ndiponso Mulungu Amagwira ntchito Yakeyo kuyambira mkati ndikufikirakunja. Komano satana, tapeza kuti iye amagwiritsa ntchito m'mene munthu amvera, ndipo iyeyo amayambira ntchito yake kunjwa kwa thupi nkumapitano mkati.

Mulungu Amagwiritsa ntchito maganizo athu kuti tipange chisankho chathu. Satana amagwiritsa ntchito makomo asanu aja a moyo wa munthu. Iyeyo amalambalala kuganizira mwakuya. Chonde kumbukirani, "Pali mphamvu ziwiri zolamulira maganizo a anthu – Mphamvu Ya Mulungu ndi mphamvu ya satana." Ndi mfundo izi nkophweka kudziwa magwero a maganizo athu ndi kudziwa chochita.

Komano tingathane nalo bwanji bvuto la momwe tikumvera ngakhale tikudziwa kuti ndi lochokera kwa satana mdierekezi? Tikumbukire malangizo ochokera m'bukhu la Banja la chi Adventist (The Adventist Home), tsamba 128. Iphani yesero lirilonse lobweretsa tchimo." Izitu nzosatheka mu mphamvu za ife eni. Apa ndipo pamene tiyenera kugwiritsa ntchito mphamvu ya chifuniro.

Tiyenera tisankhe kumukhulupirira Mulungu ngakhale kuti tikumva motani m'thupi mwathu. Titatero, tidzibvomereze tokha kuti sitingathe kulamulira umo momwe ife tikumvera m'thupi. Tikatero tiyeni tithawire kwa Ambuye mu pemphero, kubvomereza kulephera kwathu komano kumuthokoza chifukwa cha Mphamvu Yake Yoposa ndi Kulolera Kwake kutipulumutsa ife. .Iye Adzapulumutsa! Zinyon'gonyong'o zidzachoka, ndipo mtendere udzakhala mu mtima mwathu.

Nkofunika kuchita izi mwa kanthawi kufikira satana atatsimikizikadi kuti sangathenso kutilamulira ife kuti titsatire m'mene ife tikumverera. Yendani m'chikhulupiriro –kaya tikumva bwanji kaya sitikumva kalikonse. Khalani mukuganizira, ndinafa, ndipo moyo wanga wabisika pamodzi ndi Khristu mwa Mulungu. Ako-lose 3:3. Satana angatani ndi munthu wakufa? Pamene chifuniro

chisankha kuchita icho chimene sitingathe kuchita, Mulungu Amalemekezedwa, popeza Amakonda kutichitira izo zomwe patokha sitingathe kuzichita.

Chipembedzo cha pamanda mwina sichingakhale ndi chikoka chachikulu kwa ife, monganso momwe chinalibe chikoka ndi Yesu. Komabe, ndi njira yokhayo yochokeramo mu bvuto la uchimoli. Yesu Adawauza Ahelene amene anadza kwa Iye atangotsala pan'gono kupachikidwa "...Indetu, Indetu Ndinena ndi inu, Ngati mbewu ya tirigu siigwa m'thaka nifa, ikhala pa yokha iyo; koma ngati ifa, ibala chipatso chambiri." Yohane 12:24.

Ndipemphe kuti manda anu akhale kunyumba kwanu, kumalo antchito, ku ofesi ngakhale kwina kulikonse kumene undekha ungakhoze kuonekerako m'moyo wa tsiku ndi tsiku. Kukhalabe mkhristu sikungotengera ntchito ya tsiku limodzi lokha, koma ndi koposera apo. Pamodzi ndi Paulo tikhoza kunena kuti, "Nthawi zonse tiri kusenzasenza m'thupi kufa Kwake kwa Yesu kuti moyonso wa Yesu Uwoneke m'thupi mwathu. Chotero imfa igwira ntchito mwa ife, koma moyo mwa inu." 2 Akorinto 4: 10 ndi 12.

Pali njira imodzi yokha yokokera anthu kwa Yesu osati kwa ife eni. Ngati undekha utabisidwa (utapachikidwa), Yesu Adzaonetsedwa. "Khristu Akudikira ndi khumbo lakuya kuti Adzionetsere Yekha ku Mpingo Wake. Pamene Khalidwe La Yesu Lidzaonetsedwa mwakuya mwa anthu Ake, Pomwepo Iye Adzadza kudzatenga Ake a Iye Mwini.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwawerenga mu ndimeyi.

A: FUFUZANI

Mulungu nthawi zonse Ali wololera kukhululuka mwachisomo kupyolera mwa Khristu; komabe zikuoneka ngati palibe njira yogonjetsera tchimo koma imfa. Siyanitsani 'tchimo' ndi 'machimo'.

N'chifukwa chiyani tiyenera kuonetsetsa 'chikhulupiriro' sichiyenera kukhala 'monga ife timvera m'thupi', nangano tingalamulire bwanji momwe ife timvera m'thupi?

B: UKHALE MOYO WANU

“Ndiyamikire kuti manda anu akhale m’nyumba zanu, ku ofesi kapena kulikonse kumene undekha ungate kuoneka pa machitachita a patsiku. Kukhala mkhristu sindiyi ntchito ya tsiku limodzi lokha koma kufa tsiku ndi tsiku ku undekha. (Werengani 2 Akorinto 4:10 ndi 12). Pemphani ndi pemphero kuti uwu ukhale moyo wanu...ndipo KHALANI MOYO WOTERO!!

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndikusintha kwanji komwe kudzaoneke m’moyo wanga pamene Ambuye Adzayankhe pemphero langa).

Mabukhu omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Moyo Wa Chipambano, (The Life Of Victory), Meade MacGuire, Tsamba 35.
2. The SDA Bible Commentary, Bukhu 6, Tsamba 1075, zolembera 148, 1897.
3. Mtanda Wake ndi Wanga, (His Cross and Mine), Meade MacGuire, Tsamba 80.
4. Mtanda Wake ndi Wanga, (His Cross and Mine), Meade MacGuire, Tsamba 91.
5. Machitidwe a Atumwi, (The Acts of The Apostles), bukhu 2, Tsamba 243.
6. Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), bukhu 2, Tsamba 243.
7. Maumboni, (Testimonies), bukhu 1, Tsamba 167.
8. Kudziletsa, (Temperance), Tsamba 276.
9. Mafanizo A Yesu, (Christ Object Lessons), Tsamba 69.

5.

Akristu

AAMABADWA, OSATI KUPANGIDWA

Nkhani ya kubadwanso yomwe yakambidwa kwa nthawi zochulukira mu Chipangano Chatsopano ndi nkhani yomwe ambiri saimvetsa bwino. Kwa anthu ambiri, amangoganiza kuti zimatanthauza kungokhulupirira Yesu Khristu. Kwa enanso, kumulandira Yesu monga Mpulumutsi ndiko tanthauzo la Kubadwanso. Komanso kwa ena, Ubatizo womiza m' madzi ndilo tanthauzo la Kubadwanso.

Ndinene pano kuti Kubadwa mwatsopano ndi nkhani yaikulu ndi yamphamvu molingana ndi m'mene ikuonetseredwa m'mawu a Mulungu, imene anthu ambiri amaiona kukhala yobvuta kumvetsetsa zomwe malembo anena.

“Munthu amene alidi mwana wa Mulungu sachita uchimo, popeza khalidwe La Mulungu limakhala mwa iye kwa nthawi zonse ndipo wotereyo sachimwa.” 1 Yohane 3:9.

“Yense wokhulupirira kuti Yesu ndiye Khristu, wabadwa kuchokera kwa Mulungu; ndipo yense wakukonda Iye amene anabala akondanso iye amene anabadwa wochokera mwa Iye.” 1 Yohane 5:1

“Pakuti chirichonse chabadwa mwa Mulungu chililaka dziko lapansi; ndipo ichi ndi chilako tililaka nacho dziko lapansi, ndicho chikhulupiriro chathu.” 1 Yohane 5:4.

Titha kuona kuti kubadwanso ndiko m'phamvu ya moyo wa chikhristu. Tsono tipeze kuti ndichiyani chomwe chimapanga kubadwansoku kuti kukhale mbali ya moyo wathu wa uzimu. Yohane akuti, “Ndipo uwu ndi umboniwo, kuti Mulungu Anati-patsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa Mwana Wake. Iye wakukhala ndi Mwana ali nao moyo; wosakhala ndi

Mwana wa Mulungu alibe moyo.” 1 Yohane 5:11, 12.

Nkutheka kuti pamene ife tikufunafuna kuti choonadi ndi chiyani, tikhoza kunyalanyaza kuona kuti Choonadiyo ndi Ndani? Nkufunafuna kwathu kuti choonadi n’chiyani tikhoza kudumpha kuzindikira kuti choonadiyo Ndani. Tiyesetsa kuona kuti n’chiyani chomwe chikuwaphimba maso onse a kafukufuku wa mal-embo, potero titsegule njira yozindikira za choonadi chozizwachi.

“Taona Ndaima pakhomo Ndigogoda; wina akamva Mawu Anga nakatsegula pakhomo, Ndidzalowa kwa iye ndipo Ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine.” Chibvumbulutso 3:20. Mawuwatu akukambidwa kwa mpingo wa Laodikaya wa lero, popeza akupanga gawo la uthenga wapadera wa Yesu ku Mpingo Wake wa m’masiku otsiriza. Potero kuli kofunikira kudziwa yankho la funso lobwerezedwa bwerezedwa lakuti, “Ndingabadwensho bwanji kachiwiri?” Kapena awa ndi mawu ongokambidwa mwa chizolowezi? Ndi zenizenidi? Ngatidi ziri zenezeni, ndigawo lanjji la moyo wanga lomwe ndingam’patse Yesu Khristu? Nangano moyo wanga wa uzimu? Nangano ntchito yanga? Nangano moyo wanga wa nthawi yopumula? Nkofunika motani Iye Asanalowe m’moyo mwanga?

“Ganizo lililonse likuyenera kugonjera kwa Yesu Khristu. Makhalidwe onse a chinyama ayenera kuperkedwa ku Mphamvu zoposa. Chikondi Cha Mulungu chikuyenera kulamulira kuposa zonse; Yesu Khristu Akuyenera kukhala pa mpando wolamulira mumtima mwathu. Matupi athu akuyenera kuyesedwa Ake ogolidwa. Ziwalo za thupi zikuyenera kukhala zida za chilungamo.”¹

Izitu zikufunika kuchitapo kanthu mwakuya osangoti kungoleka zizolowezi zathu zoipa kokha, makhalidwe athu a uchimo, chikondi cha dziko lapansi ndi chuma chathu cha m’dziko. Zikutanthauza kuti ganizo lililonse lilamuliridwe ndi Iye. Makhalidwe athu onse a uchimo obadwa nawo, ndi ziwalo zonse za thupi zionetsere chilungamo chake.

Kuti izi zitheke, Yesu Akuti, “Ndikulangiza ugule kwa Ine golidi woyengeka m’moto, kuti ukhale wachuma, ndi zobvala zoyera, kuti ukadzibveke, ndikuti manyazi a usiwa wako asa-

onekere; ndi mankhwala opaka m’maso mwako kuti ukaone.” Chibvumbulutso 3:18.

“Ndi chiyani chomwe chikundipangitsa ine kuoneka wat-soka, wamaliseche, pakati pa iwo amene akuoneka olemera ndi achuma? Ndiko kusowa Chilungamo Cha Yesu.” Ngakhale kukhulupirira kotheratu mu ziphunzitso za mpingo zolondola izi sizingathe kupulumutsa wina aliyense. Uku sindiko kulam-ula kwa mpulumutsi wathu komano ndi limodzi la Malamulo a chibadwa a Mulungu. Ili ndi lamulo lomwe limati, “Chifukwa chisamaliro cha thupi chidana ndi Mulungu; pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu, pakuti sichikhoza kutero.” Aroma 8:7.

Pachifukwa ichi, Nikodemo adadza kwa Yesu nthawi yausi-ku. Mtima wake unali wolemera, popeza adafunutsitsa kuphim-bidwa ndi Chilungamo cha Yesu, chomwe ndi chitsimikizo cha chipulumutso, komano sanadziwe kuti akadachipeza motani. Yesu Adaona chosowa chake ndipo Anamuuza chofunikiracho. “...Ngati munthu sabadwa mwatsopano sakhoza kuona Ufumu wa Mulungu.” Yohane 3:3. Chuma cha Nikodemo, chikoka chake m’dziko, zomwe iye adachita, zonsezi zinali zosakwanira kufikira chifuniro cha Yesu cha kubadwanso mwatsopano.

Nali bvuto la Nikodemo. Polephera kuona yankho, iye ada-funsa, “...Izi zingatheke bwanji?” Yesu n’kuti Atamuuza kale kuti, “Chobadwa m’thupi chikhala thupi; ndipo chobadwa mwa Mzimu chikhala mzimu.” Yohane 3:6. Nikodemo sadafune kuona zoterezi. Undekha unali utamanga maziko mwa iye.

Mawu A Yesu kwa Nikodemo Adakalipobe mpaka lero. Thupi silingapachike chakuthupi, ngakhale patakhalo malonjeza-no otani, kapenanso kudzipereka konse komwe ife tingapange, ngakhalenso kuikirapo mphamvu kotani. Nthawi zonse padzakha-labe kaumunthu koonekera kofunabe kulumulira. Wina adati kuli bwino kuganiza kuti undekha ndi tchimo, kulekana ndi kungolekeratu osauganizira n’komwe.

Khristu Waima pakhomo la Mpingo Wake ndi mawu odandaulira, “...Wina akamva mawu Anga nakatsegula pakho-mo, Ndidzalowa kwa iye...” Chibvumbulutso 3:20. N’chifukwa chiyani Yesu Akudzionetsera motero? Chifukwa chakuti ambirife, monga ngati Nikodemo, tidakalibe akhungu ku undekha Tidakaf-unikirabe kudziwa kuti akhristu amabadwa, osati kupangidwa.

Akhristu ambiri achilungamo amakhala ndi ganizo lakuti ndi thandizo La Mulungu, chibadwa chawo chakale – thupi –

chikhoza kuyeretsewa, kutsukidwa, komanso kumasulidwa ku tchimo lamkati, nakhozanso kukhala moyo wachipambano kwa Mulungu. Ichi ndi chinyengo cha satana! Nzeru yake ndiyo kutsogolera anthu kuti adzikhulupirira kuti chibadwa cha munthu chikhoza kusinthidwa. Iye amadziwa kuti chikuyenera kufa basi komano amayesetsa kukwirira choonadico ndi mabodza kuti ife tikhalebe akhungu.

“Moyo wa mkhristu simoyo wongosinthidwa mongokhotetsedwa, kapenanso simoyo wongochulukitsidwa pa umoyo wakale, koma ndi moyo wosinthiratu chibadwa chake. Pamafunika kufa ku undekha ndi ku uchimo, ndikubweretsanso moyo wina watsopano, Kusintha kotereku kungachitike pokhapokha ndi Mphamvu ya Mzimu Woyera Wogwira ntchito mkati mwa ife.”³³

“Khristu Anadza ku dziko, Nabvala umunthu ndi kuima monga Woimirira munthu, kusonyeza mu mkangano waukulu ndi satana, kuti munthu, monga m'mene analengedwera ndi Mulungu, ngati atalumikizana ndi Atate mdi Mwana, ali okhoza kumvera Lamulo lirilonse La Mulungu.”³⁴

Mawu amenewa ndiofunuka kuwaganizira mwakuya. M'mauwa tikupezamo chifukwa chenecheni chomwe Yesu Anayenera kubadwa ndi moyo wosachimwa wofanana ndi womwe Adamu woyamba adali nawo asanachimwe. Ndi chokhacho chobadwa ndi Mzimu chomwe Mulungu Angagwire nacho ntchito kuchiumba ndi kuchikhazikitsa mu Chifuniro Chake. Chibawa cha uchimo ndi chosakhazikika ndipo sichingathe kubvomera chifuniro cha Mlengi. Khumbolo likhoza kukhalapo m'maganizomu, koma thupili ndi lachibvundi, lokanika. Zotsatira zake ndizo kugonja.

Pamene Yesu Anati, “...Ngati mbewu ya tirigu siigwa m'nthaka, nifa, ikhala pa yokhayokha...” Yohane 12:24, Ankayankhulatu za ubatizo, umene, mchoonadi chake umayimira imfa.

“Nkhaniyi ya kubadwanso mwatsopano ndi nkhani yosowa mu m'badwo uno wa dziko lapansi. Ichi n'chifukwa chake muli mpungwepungwe wochuluka m'mipingo yambiri. Ambiri, amene amadzitcha akhristu, natenga dzina la Khristu ali opanda chiyero ndi osayeretsedwa. Inde, adabatizidwa, komano adakwiridwa

adakali amoyo. Undekha udali usadafebe mwa iwo, potero sadauke ku moyo watsopano wa mwa Khristu.”⁵ (Izi zinalembedwa m’chaka cha 1897).

“Koma kwa onse amene Anamlandira Iye, kwa iwo Anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu akukhulupirira dzina lake; amene sanabadwa ndi mwazi kapena ndi chifuniro cha thupi, kapena ndi chifuniro cha munthu, koma cha Mulungu.” Yohane 1:12,13. Ndizomveka kuti kuuzira kwa Mawu a Mulungu kumaphunzitsa kufunikira kobadwanso mu Mzimu, munthu asanakhale mwana wa Mulungu kapena chiwalo cha banja la Mulungu. Komabe ngakhale izi ziri chomwecho, imfa ikuyenera kuyamba usanakhale moyo.

Yankho la bvuto ili ndi lopyola kuthekera kwa umunthu. Munthu, ngakhale m’kuchimwa kwake, akhozabe kugwiritsa ntchito chifuniro chake chopatsidwa ndi Mulungu, ndikusankha kufa ndikubadwanso mwatsopano.

Njira imeneyi yakambidwa kale mu ndime yoyamba ya bukhuli. Ife tinalibepo mbali yakuchita ndi chibadwidwe chathu, koma atamandidwe Ambuye, chifukwa ife tiri nayo mbali mu nkhani imeneyi yobadwanso. Komabe m’kubadwanso kwachiwiriku tiyenerabe kulumikizana ndi Atate ndi Mwana. Izi ndizo zimene kulungamitsidwa kumakwaniritsa.

Atate Amalungamitsa wokhulupirira, poyang’anira kuti wokhulupirirayo walandira Ambuye Yesu ndi nsembe Yake yotitetezera pa Mtanda.

Yesu Anakhala Moyo Wake molumikizana ndi Atate Wake. Iye Adati, “...Sakhoza Mwana kuchita kanthu payekha.” Yohane 5:19. Moyo Wake womvera ku Malamulo onse sankangodzichitira mwa Yekha, komatu mwa magawo onse adadalira pa Atate. Umo ndi m’meneMoyo Wake uli chitsanzo chakuti ife titsatire.

Yesu akutiuzza ife kuti, “...Pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kanthu.” Yohane 15:5. Popanda Yesu, ngakhale m’moyo watsopano, sitingathe kumvera Lamulo La Mulungu. Komano Yesu, Wokhala mwa ife, monganso Atate Anakhala mwa Iye, zimatheka kumvera. Amachita izi mwa ndi ife. Iyitu ndiye nkhani yabwino, sichoncho nanga?

Funso lomwe tiyenera kufunsa ndilo lakuti, “Kodi ndi chiyani’ganiro cha Lamulo liti lomwe ndiyenera kukwaniritsa?”

Yankho lake tilipeza mu zolemba izi: “Mulungu Amafuna kudzipereka kotheratu kwa mtima, kulungamitsidwa kusana-chitike; ndipo pofuna kuti munthu afikire polungamitsidwa, payenera kukhala kumvera kopitiriza, kupyolera mwa chikhulupiriro chochitachita ndi chamoyo chomwe chimagwira ntchito ndi chikondi ndi kuyeretsa moyo.

Mutha kuona kuti pamene chiyang’aniro cha kulungamitsidwa ndicho kudzipereka, chiyang’aniro chosungitsa kulungamitsidwaku ndicho kumvera kopitirira. Kodi kulungamitsidwaku kumatipanga ife kumvera? Ayi. Kulungamitsidwaku kumangokhudza mbali yathu ya zachilamulo – M’mene tiriri ndi Mulungu wathu. Nangano tingakwaniritse bwanji chiyang’aniro chachiwirichi? Umu ndi m’mene tingachitire:

“Pamene Mulungu Agwira ntchito Yake mu mtima, ndipo munthu apereka chifuniro chakecho kwa Mulungu ndi kumvana ndi Mulungu, Mulunguyo Amachita ntchito mu mtima wa munthu zomwe Mulungu Amachita ndi Mzimu Woyera, potero pamakhala chiyanjano pakati pa zolinga za mtima ndi zochita za moyo. Tchimo lina lirilonse likuyenera kusiidwa, ndikuonedwa ngati ndilo linapachikitsa Mbuye Wathu, Mwini moyo ndi ulemero, ndipo wokhulupirirayo akuyenera kukhala moyo wogonjetsa tsiku ndi tsiku pochita ntchito za Khristu. Ndi pokhapokha chifuniro chathu chigonjera, pamene kumvera kwathu kuli kopitirira, pamene m’dalitso umenewu wa Kulungamitsidwa tidzakhala nawo.”⁷

Chonde onetsetsani kuti ntchito ya munthu ndiyo kupereka chifuniro chake. Moyu wa Khristu unali moyu wodzipereka nthawi ndi nthawi. Izi tizikamba mwakuya pa mutu ukubwera kutsogoloku. Kumvera kopitirira ndi zotsatira za ntchito ya kuyeretsedwa, kumene tiyankhulenso mwakuya mu ndime yotsatira.

Zikhoza kuoneka kwa ena ngati kuti chibadwa cha umunthu n’chosafunikira. Eya, nkhani ndi imeneyodi.

“Pamene moyu udzipereka okha kwa Khristu, mphamvu yatsopano imatenga ulamuliro wa mtima

watsopano. Kusintha kumachitika kumene munthu sangakwanitse pa iye yekha. Ndi ntchito yokhudza mphamvu za Umulungu, zomwe zimabweretsa mphamvu zakuya mu chikhalidwe cha umunthu. Moyo wodzipereka kwa Khristu woterewu, umakhala pokhazikikapo Iye Mwini, pamene Iye Mwini Amauchinjiriza, ndipo Amayembekezeranso kuti palibenso wina amene adzalamulire moyo woterewo koma Iye Yekha. Moyo woterewo, wosungidwa ndi mphamvu za kumwamba, sungakhudzidwe ndi machenjero a satana... Njira yokhayo yodzitetezera ku uchimo ndiyo Mphamvu Ya Yesu Khristu Okhala mu mtima mwathu mwa chikhulupiriro mu Chilungamo Chake. Pokhapokha ife titalumikizana ndi Mulungu kotheratu, sitingathe kugonjetsa maganizo onyansa a kudzikonda, kudzisamalira tokha ndi mayesero a uchimo. Inde, tikhoza kuleka zizolowezi zambiri zoyipa, mwa kanthawi tikhoza kulekana naye satana; koma popanda kulumikizana kwenikweni ndi Mulungu, podzipereka tonse kwa Iye mphindi ndi mphindi, tidzatha kugonjetsedwa.”⁸

“Nangano kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro kumatanthauzani? Ndi ntchito ya Mulungu kuyika ulemero wa munthu mu nthaka ndi kumuchitira munthuyo izo zimene iye sangathe kuchita payekha. Pamene anthu aona kulephera kwao konse, iwo adzakhala okonzeka kubvekedwa ndi Yesu Khristu.”⁹

“Nchifukwa chiyani ziri zobvuta kwambiri kukhala moyo wodzikwaniza wekha ndi wodzichepetsa? Chifukwa chake n’chakuti akhristu sanafikirebe pakufa ku dziko. Nkophweka kukhala ndi moyo titatha kufa.”¹⁰

Kumbukirani kuti njira za Mulungu si njira zathu. Njira Ya Mulungu ikhoza kuoneka ngati yolephera, komano njira Ya Mulunguyo ndi yokhayo yopita ku chipambano. Pakuti pamene tabadwadi mwatsopano –

Timakhala ndi moyo pakufa.

Mphamvu zimabwera kudzera mu ufooko.

Nkhondo timapambana podzipereka.
Pomwepo tidzadziwa kuti Akhristu amabadwa osati
kupangidwa.

**Mafunso othandiza kuchita zomwe mwaphunzira mu ndi-
mey.**

A. FUFUZANI

Kodi tanthauzo lakuya la “kubadwa mwatsopano” ndi
chiyani ndipo mungalizindikire bwanji m’moyo wanu?
Nangano “Chilungamo” mungachisunge motani?

B. PANGANI KUKHALA MOYO WANU

“Tikhoza kusiya zizolowezi zambiri zoyipa, mwa kanthawi
tikhoza kulekana naye satana; koma popanda kulumiki-
zana kwenikweni ndi Yesu, kupyolera m’kudzipereka
kwathu kwa Iye mphindi ndi mphindi, tidzagonjetsedwa.”
Pemphani ndi pemphero kuti izi zikhale zotheka m’moyo
wanu... ndipo KHALANI MOYO WOTERO!!

Popeza pempheroli layankhidwa, moyo wanga udzakhala
wotere: (Ndikusintha kotani komwe kudzaoneke m’moyo
wanga pamene Ambuye Ayankha pempho langa).

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

- 1 Banja La chi Advenitst, (The Adventist Home), Tsamba 128.
- 2 Khristu Chilungamo chathu, (Christ our Righteousness) Tsamba 90.
- 3 Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 172.
- 4 The SDA Bible Commentary, Vol. 7A, Tsamba 650. Zizindikiro za Nthawi (Signs Of The Times), June 9, 1898.
- 5 The SDA Bible Commentary, Vol 6, Tsamba 1075, Manuscripts 148, 1897.
- 6 Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), bukhu 1, Tsamba 366.
- 7 Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), bukhu 1, Tsamba 397.
- 8 Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 3324.
- 9 Khristu Chilungamo Chathu, (Christ our Righteousness), Tsamba 104.
- 10 Mauthenga kwa Achinyamata, (Messages to Young People), Tsamba 127.

6.

KUCHOKERA

Kukulungamitsidwa **KUPITA KU CHIYANI**

Ngati munthu walungamitsidwa, ndipo kumwambako zalembedwa m'mabukhu kuti "monga ngati sin'nachimwepo," zingaoneke ngati zachilendo ngati nditafuna china chirichonso choposera apo, Kupereka maganizo onga ngati amenewa ndiko kuonetsera kuti munthu wotereyo akuganizira monga ngati munthu wa zachilamulo. Pamakhalabe chikhumbokhumbo chofuna kuchita kenakake kuti ife timvedi mkati mwathumu kuti ndi zoonadi. Chiyang'aniro chapamwamba penipeni kwa munthu wolungamitsidwa ndicho kukhala mwa chikhulupiriro malo amene Mulungu, mwa Chikondi Chake Watipatsa ife monga mphatso yaulere. Komabe tiyenera kudziwa kuti pamene ife talungamitsidwa ndi nthawi yomweyonso imene ife tiyeretsedwa. Ziwiri zonsezi timazifikira mwa chikhulupiriro.

Kulungamitsidwa kumakhudzana ndi zolemba zanu m'mabuku kumwamba. Kumasintha mlandu wanu kuchokera kwakuti Chigawenga chokaphedwa, kukhalano Mfulu yopanda mulandu, ndipo zolemba zonse za m'mabuku zokhudza moyo wanu wakale zimakhala zoyeretsedwa.

Kuyeretsedwa ndiyo njira yachiyero yokonzedweratu ndi kumwamba imene Chigawenga chomasulidwacho (Chimeneno chakhala m'mbanja La Mulungu) chikhoza kuthokoza mosalekeza kwa Mulungu chifukwa cha mphatso yosaneneka yotere ya Kulungamitsidwa kwa Gwamula wotereyu. Kodi izi zimatheka motani? Pololera tsiku ndi tsiku kuti Mulungu Agwire ntchito mwa ife kuchita chifuniro Chake. Afilipi 2:13.

Mbali yathu ndiyo kulola Mulungu kugwira ntchito m'moyo wathu, kutikonzanso kuti tidzitha kubvomera kuti inde, nthawi

zonse pamene Yesu atiuza ife kuti, “Nayi Njira yomwe uyenera kuyendamo.” Chifuniro cha kumwamba cha kwa onse amene adzalowe kumwamba ndicho kukhala nacho chikhulupiriro chotheratu mwa Yesu Khristu opanda chikaiko chirichonse, kapena kunyalanyaza, ngakhale kufunsa mafunso ena aliwonse. Kuyankha kwathu pa chitsogozo chake uyenera kukhala kwa chilengedwe, monga umo duwa limatembenukira ku dzuwa.

N’zachimvekere kuti sitiyenera kukayikira kwina kulikonse popeza kulungamitsidwa kwathu (Kopatsidwa mwa ife) kapenanso kuyeretsewa kwathu (Kotengera khalidwe lathu la tsiku ndi tsiku) zonsezi ndi mphatso zochokera kwa Khristu. Ndikupyolera mu kulungamitsidwa, pamene kumvera kumapatsidwa kwa ife, nthawi yatsopano ngakhalenso moyo uli nkudza.

“Kupyolera M’Chilungamo Chake chopatsidwa kwa ife, Iwo amabvomerezeka pamaso pa Mulungu monga iwo amene akuonetsera ku dziko kuti ndi Ake a Mulungu, osunga Malamulo Ake.”¹

“Tiyenera kuphunzira Moyo wa Mlengi wathu, popeza ndi Yekhayu Amene Ali Chitsanzo Cha Ungwior kwa anthu. Tiyenera kulingalira za mtengo wapatali woperekedwa pa Gologota ndi kuonapo kuipitsitsa kwa tchimo ndi chilungamo cha Lamulo. Ndipokhapo pamene tidzathe kuphunzira ndi kulimbikitsidwa mwakuya za Nzeru Ya chipulumutso. Chidziwitso chanu cha Khalidwe La Mulungu chidzakhala chakuya; ndiponso nzeru yonse ya Chipulumutso idzasongoka m’maganizo anu, pomwepo mudzatha kukwaniritsa maitanidwe anu. Mutatha kutsimikizika kotere inu eni, mudzathano kuuza ena za kusasinthika kwa Lamulo, komwe kunaonetsedwa kupyolera mu imfa ya Yesu pamtanda, komanso kuipitsitsa kwa tchimo, ndi Chilungamo Cha Mulungu polungamitsa munthu wokhulupirira mwa Yesu, polingalira za tsogolo lake lomvera ku Malamulo a Boma La Mulungu kumwamba ndi padziko lapansi.”²

“Chipembedzo cha payekha-payekha cha ife anthu chazilara kotheratu. Chomwe tikuona ndicho kungodzi-

onetsera, kayendetsedwe ka chipembedzo, komanso chipembedzo cha pakamwa pokha; komano pakufunika china chakuya ndi cholimba kuti chilowe m'moyo wathu wa chipembedzo... Chomwe tiyenera kudziwa ndicho kudziwa Mulungu ndi Mphamvu Ya Chikondi Chake, Yoonetsedwa mwa Khristu, kupyolera mwa nzeru yakuchita nayo m'moyo wathu... kupyolera mwa kuthekera kwa Yesu, kupyolera mu Chilungamo Chake, chomwe chimapatsidwa kwa ife mwa chikhulupiro, tiyenera ife kufikira pa chiyero cha khalidwe la chikhristu.”³

Ungwiro umabweranso kudzera mu kulungamitsidwa. Ndi kupyolera m'chiyero momwe izi zimatheka. Uwu udzakhala moyo wathu, osangoti kufikira kubwera kwa Yesu kokha, komano kufikira muyaya. Chidzakhala chimwemwe chathu kuonetsera chiyamiko chathu ku mayiko onse olengedwa, kuwauza za mphatso yosaneneka ya Yesu Khristu.

Chikhulupiro chakhazikika pa kulungamitsidwa, komwe ndi mphatso yaulere yochokera kwa Mulungu. M'mene ife tilandirira mphatsoyo zagona pa chiyanjano chathu mu nkhani ya chiyero ndi kubvomereza kwathu kulolera kuti Yesu Akonzenso khalidwe lathu kuti lionetsere Khalidwe Lake. Iyi ndiyo ntchito Yake mulimonse umo Iye Achitira kukwaniritsa cholinga Chake. Mbali yathu ndiyo kungodzipereka kwa Iye.

Kodi nangano, tidziti kuyeretsedwa ndiko umboni wa kulungamitsidwa? Yesu, pa Yohane 15:5 Akuti, “Iye amene akhala mwa Ine ndi Ine mwa iye, yemweyo abala chipatso chambiri...” Chipatso cha Mzimu chidzaonekera mwa onse amene alungamitsidwadi. Agalatiya 5:22,23. Wokhulupirirayo akungoyenera kukhala mu chiyanjanochi (pokhazikika pache) mwa Khristu, pomwepo iye adzathano kubereka chipatso. Khristu ndiye Mpesa; wokhulupirira ndiye nthambi. Pokhazikika pathu monga ziwalo za banja La Mulungu, ndipo maziko a chimwemwe chathu. Sitiyenera ife kukhala ndi maganizo a pokhapokha. Pamene ife tiri nthambi za mpesa timakhala mbali imodzi ndi Iye. Kulungamitsidwa kudzafunikira nthawi zonse. Khalidwe La Khristu ndicho chobvala chomwe chidzafikira chosowa chathu chonse chokwaniritsa Lamulo Langwiro La Mulungu. Chotero, ichi chiyenera kukhazikika.

“Mdani wa munthu ndi Mulungu safuna kuti choonadi ichi (cha kulungamitsidwa mwa chikhulupiro) chimveke moonadi mwake ndi anthu onse; popeza iye amadziwa kuti ngati zitatero, mphamvu yake idzaphwanyidwa. Ngati iye angakwaniritse kulamalira maganizo, kotero kuti chikaiko ndi kusakhulupirira ndi mdima zidzawakuta iwo amene amadzitchula kuti ndi ana a Mulungu, apo ndipo iye adzatha kuwagonjetsa ndi mayesero.”⁴

“Taonani, ndapatsa inu mphamvu ya kuponda pa njoka ndi zinkhanira ndi pa mphamvu yonse ya m’dani...”
Luka 10:19.

N’chachidziwikire, kuti akhristu sanafike pozindikira kuti akhoza kukhala omasuka ku mphamvu za satana. Izi sizitanthauza kumasuka ku mayesero ake, komano mayeserowo, pamodzi ndi uchimo zidzakhala zopanda mphamvu. Iyitu ndi nkhani yabwino kwa ife tonse.

Tchimo lakhala ndi chikoka chachikulu m’banja la munthu. Tchimo liri ndi chikoka ku chibadwa chathuchi cha uchimo. Tchimo limabweretsa chisangalalo cha kanthawi kochepa. Komano poletsedwa, limapatsa chidwi. Limabweretsa mzimu wodziimira pawekha. Limapangitsa kusagwiritsa bwino ntchito kwa mphamvu ya chisankho. Komatu zonsezi nzogonjetsedwa kale m’moyo wa m’khristu amene ali wobadwanso pamene m’khristuyo ayenda ndi Ambuye m’chilungamo.

Pali mbali ina yamachenjerero ya mphamvu ya tchimo yomwe tiyenera kuidziwa: “. . . Mphamvu ya tchimo ndiyo Lamulo.” 1 Akorinto 15:56. Liwu lakuti Dunamisi (kuthekera) muchiyankhulo cha chi Helene, limaimira kuti mphamvu. Nthawi zambiri limagwiritsidwa ntchito monga mphamvu. Chinthu chirichonse cha mphamvu chinatengera ku liwu limeneli. Mphamvu zake ndi zochuluka monga mphamvu zophulitsira chirichonse. Chotero, ngati mphamvu ya tchimo ndi Lamulo, tiyeneranso kudziwa kuti izi ndi zoonza. Mulungu Sanaonetsere Lamulo Lake monga kope lolemberapo Khalidwe Lake kapenanso “mphamvu ya tchimo.” Lamulo La Mulungu La chikondi ndilo lomwe Linamupangitsa Iye kupanga munthu wokhala nako kuthekera kochimwa. Iye

Adam'patsa munthuyo mphamvu ya kusankha. Kodino tidziti apa ndipo pagona mphamvu ya tchimo? “Mayesero amagonjetsedwa pokhapokha munthu akudziwa kuti ali nako kuthekera konse kuti akhoza kuchimwa, ndipo ngakhale ali nako kuthekeraku, iyeyo n'kusankha yekha kukana kuchimwako mwa chikhulupiriro, podalira mphamvu ya Umulungu.”⁵

Nzosangalatsa kudziwa kuti mphamvu zimene Yesu Adapereka kwa akuphunzira Ake mu Luka 10:19 zinali (ulamuliro), osati kuthekera. Komano mphamvu ya m'dani mu ndime yomweyo ndiyo (kuthekera). Apano tikhoza kunena kuti Mulungu Adapereka kwa munthu ulamuliro pa kuthekera kwa satana komanso amakhala nayo mphamvu ya ulamuliro ndi kuthekera komwe pa satana m'kulumulira kwake kwa Mulunguyo. Kupyolera mwa Khristu mphamvu zonse za satana ndizophwanyidwa popeza iyeyo ndi m'dani wogonjetsedwa kale.

Akolose 1:3 akuti, “Amene Adatiombola ife ku mphamvu ya mdima, natisandulitsa ife mu ufumu wa Mwana Wake Wokondedwa.” Kuomboledwa kuchokera ku ulamuliro wa satana ndi kukhala ziwalo za ufumu wa Mulungu ndi zinthu zofana. “Pamene mukhuthula chifuniro chanu, nzeru zanu, ndi kuphunzira mwa Khristu, pomwepo mudzalandira mpumulo wa ufumu wa Mulungu.”⁶

Popeza Lamulo La Mulungu ndi kope lolemberapo Khalidwe Lake, ndipo satana akuyesetsa nthawi zonse kudetsa khalidweri, tipezano yankho pa nkhani yakuti Lamulo ndilo “mphamvu ya tchimo.”

Kupyolera m'kusamvetsetsa ndi kusagwiritsidwa bwino ntchito kwa Lamulo La Mulungu, Israeli wakaleyo adalamulidwa ndi satana kwa nthawi yaitali. Inali nzeru Ya Mulungu kuti Lamulo Lake, umo Linaperekedwera pa phiri la Sinai, likhale sukulu yophunzirirapo powabwezeretsanso anthu Ake kwa Khristu. Agalatiya 3:24. Komano satana naye anali ndi njira zake. Lamulo Lomwelo La ufulu iye adalikhotetsa ndi kuligwiritsa ntchito kuwaika anthu a Mulungu mu ukapolo. Zidatheka bwanji? Pongokhazikika pa mfundo imodzi yokha ya ntchito ya Lamulo – ntchito ya Lamulo yotsutsa tchimo. Paulo adalemba kuti, “Potero pa kuchimwa kwa munthu m'modzi chiweruza chinadza kwa onse ku chitayiko...” Aroma 5:18. Apatu ndipo pamene satana wagwiritsitsa ndi mphamvu yake pa anthu. Iye

amayesetsa kutseka maso a anthu kuti asawerengenso kumapeto kwa ndimeyi, komwe kunalembidwa mawu awaa: "...Poteronso mwa mwa chilungamo cha m' modzi kunadza mphatso yaulere ya kwa anthu onse ku chilungamo cha moyo."

Satana wakulitsa kutsutsidwa kwathu ndipo wakhazikitsa kumvera Lamulo kokha monga njira yokhayo yothana ndi bvutoli. Potero munthu wagonjetsedwa poyesetsa icho chimene iye sangathe kuchisunga payekha – mphamvu, kapena ulamuliro. Chilango ndi kutsutsika zimayendera limodzi, ndipo ndi zida zomwe satana amazigwiritsa ntchito ponamiza akhristu.

Kutsutsika ndi kulakwa pachiyambi zidakhazikitsidwa monga njira zothandiza kumuonetsera munthu kusowekera kwake, potero munthuyo athe kubwerera kwa Mulungu amene Anatuma Mwana Wake kudzathana nalo bvutoli la tchimo. Kholo lachikondi, likamalanga mwana wake wosochera, limaonetsera ulamuliro ndi kuthekera, ngakhale kuti mwanayo sangathe kulimvetsetsa khololo. Tchimo linabvumbulutsa Lamulo lomwe linalipo kuyambira kalekale ngakhale linali lomveredwa molakwika. Mwa kutsutsika, ntchito yaikulu ya Lamulo monga mphunzitsi wamkulu idabisika m;maso a wanthu.

Chilango ndicho mphamvu yankhanza pakati pa anthu a chikunja ngakhalenso zipembedzo za chikhristu. Ambiri a makolo athu amene ankagwira ntchito ya kukonzanso adazunzika ndi chilangochi. Chikhristu nacho chayesetsa kulimbana ndi bvutoli koma m' malo mwake changokwanitsa kupeza mayankho a anthu okha, amenenso amalephera kudzutsa Chikondi Cha Mulungu ndi kumvera Lamulo Lake. Davide adatseguka maso ndipo adatha kuliona Lamulo monga mphunzitsi wamkulu, kapena njira yopita kwa Khristu. Kuyankha kwake kunali kwakuti, "Ha! Ndikondadi Chilamulo Chanu; ndilingiriramo ine tsiku lonse." Masalmo 119:97.

Kuyambira pa mpanduko wa satana, iye wakhala wodana ndi Lamulo La Mulungu, poyesetsa kulisinthana kapenanso kungolipotoloza pan'gono. Njira iliyonse yomwe imayesetsa kugwiritsa ntchito kulungamitsidwa, komwe ndi kuikidwa kwa Khalidwe la Khristu pa munthu, monga ngati njira yosinthira kapena kuchotseratu Lamulo La Mulungu, ndi njira yokhayo yogwirizana ndi satana ndi kulumikizana naye mu mpanduko wake kwa Mulungu.

Chiphunzitso chakuti Lamulo liribe ntchito koma chikhulupiriro chokha, Kutsutsana ndi Lamulo La Mulungu, zonsezi ndizo yankho la umunthu lothana ndi uchimo pogwirizana ndi satana m'kuukira kwake Boma La Mulungu.

Munthu wamakono akhoza kuganiza kuti Lamulo silingathe kufira chosowa chake. Komabe munthuyo adzafunabe Mpulumutsi, amene Lamulolo Lidzampititsa kwa Iye. Choonadi n'chakuti mpofunika basi munthu kusinthiratu wathunthu, osati Lamulo. Kusinthikaku kumachitika njira ziwiri zomwe ndi zofanana, komano zosiyana m'kacitidwe kake. Choyamba, njira yokhudza zachilamulo inakwaniritsidwira munthu ndi Khristu Mwini Wake pa Gologota pamene iye Anatenga malo athu otiyenera, nalipira mtengo umene ife patokha sitikanatha kuulipira, natikhala ndi moyo.. Potero, Mbiri ya munthu imasinthika kuyambira nthawi yomwe munthuyo walandira Yesu Khristu kukhala Mpulumutsi wake, ndikudzipereka kwathunthu moyo wake kuti ulumuliridwe ndi Khristu. "Pamene anthu angaone kupelewera kwao, pamene-po adzakhala okonzeka kubvekedwa ndi Chilungamo cha Yesu."⁷ Pa Gologota ndipo pamene pamationetsera mopanda chikaiko china chirichonse za kusasinthika kwa Lamulo La Mulungu. Ngati kukadakhala kotheka kuti Lamulo La Mulungu Lisinthidwe, padalibenso chifikwa chakuti Yesu Afe pa Gologota. Tithokoze Mulungu chifukwa cha Mphatso ya Yesu ya pa Gologota, pamene Yesu anatengano ulumuliro opulumutsa amunsinga kuchokera ku dzaja lamphamvu la satana wonyengayo wamkuluyo.⁸

"Chifukwa chake tsopano iwo akukhala mwa Khrist Yesu alibe kutsutsidwa, amene ayenda osati mwa thupi, koma mwa Mzimu." Aroma 8:1. Kulungamitsidwa kumasamalira nkhani ya kutsutsidwa kwa mkhristu amene anadzipereka kwa Yesu. Yesu Mpulumutsi akuti, "Pakuti Mulungu Sanatuma Mwana Wake ku dziko lapansi kuti Akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi Iye." Yohane 3:17. Lamulo Limatsutsabe, koma satana yekha ndiye ali kalikiliki kutsutsa. Mkhristu wobadwanso (wolungamitsidwa) amadziwa kuti ngakhale satana amagwiritsa ntchito umo momwe munthu amvera mthupi mwake kuti amutsutse munthuyo, Yesu Khristu Sali ku mbali yotsutsa. "M'mene monse mtima wathu utitsutsa; chifukwa Mulungu Ali Wamkulu Woposa mitima yathu, Nazindikira zonse. Okonedwa, mtima wathu ukapanda kutitsutsa, tiri nako

kulimbika mtima kwa Mulungu.” 1 Yohane 3:20,21.

Kodi tikutha kuona kuti ndi pokhapokha ife titatha kumumvetsetsa Mulungu mu chiyanjano Chake chenicheni ndi munthu – Cha chikondi osati chotsutsa – pamene tidzakhala womukhulupirira kotheratu. “Pakuti Chilamulo cha Mzimu wa moyo mwa Khritu Yesu chandimasula ine ku lamulo la uchimo ndi la imfa.” Aroma 8:2. Lamulo la Mzimu ndilo lomwe Limatiphunzitsa ife za moyo wa mwa Yesu Khristu, umene umatimasula ife ku lamulo la uchimo ndi imfa. Ili ndi limene Paulo anamasulidwa nalo pamene analemba mu Aroma 7.

Zonena kuti lamulo la tchimo lomwe limanena kuti “... Pakuti mphotho yache ya uchimo ndi imfa...” Aroma 6:23 lili ndi mphamvu yotitsutsa m’ moyo wathu poumurizidwa ndi satana. Ndi nzeru yake kutiumiriza ife kulapa kupyolera m’kumva kwathu kotere. Kulapa kochuluka kwa akhristu kumakhala chilakolako chofuna kumasuka ku kamvedwe kotereka. Ngati tiri a chilungamo titha kuona kuti undekha ndiwo muzu wa kulapa kotereku. Komatu Mawu A Mulungu Akuti, “...Ubwino Wa Mulungu Ukubwezera kuti ulape.” Aroma 2:4. Sindiko kupyolera mkutsutsa, komano kupyolera poyan’gana kwa Khristu pa mtanda wa Gologota zomwe zimatipangitsa ife kulapa koonadi mtima, Kudziwa kuti Iye Amadana ndi tchimo komano Amakonda wochimwayo, kumatipangitsa ife kukhala mfulu. “Chifukwa chake ngati Mwana Adzakuyesani inu afulu, mudzakhala mfulu ndithu.” Yohane 8:36

Monga momwe tikuonera kuti ife ndife akapolo a tchimo, lomwe lasiya zipsera zambiri mwa ife – zomwe ziyenera kuchotsedwa – tithano kumvetsetsa m’mene Yesu Ayenera kugwira ntchito mwa ife ndi chipiriro chonse kutichotsera zizolowezi zoipazi. Ndi pokhapo pamene ife tidzathe kuona chifukwa chomwe kuyeretsewa – komwe ndi mbali yachiwiri – ndiyo njira ya Mulungu yotichotsera ife zizolowezi zoipazi, ndipo ndi ntchito ya masiku onse a moyo wathu. Sizitanthauza kuti masiku onse a moyo wathu tidzakhala wosachimwa, komano zidzakhazikitsa mwa ife khalidwe lodzipereka kotheratu ndi kulolera komwe kudzapangitse Mulungu “...Kuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe.” Afilipi 2:13.

Kulungamitsidwa kumachita ndi chibadwa chathu. Pamene tifa ku undekha, tipereka chifuniro chathu, ndi kulola

Iye kuti Alamulire moyo wathu, pamenepo khalidwe latsopano limaperekedwa kwa mkhristu amene wangobadwanso kumene. Khalidwe lotereli ndilo likhoza kumvera Lamulo La Mulungu, pamene khalidwe lakale linali lodana ndi Lamulo La Mulungu Aroma 8:7. Kuyetsedwaku kumatengano ntchito yokonzanso khalidwe la munthu ndi kuchotsa zizolowezi zonse zoipa zomwe zidabwera ndi khalidwe lakale la uchimo. Zizolowezi zoterezi ndizo zotsalira za moyo wakale wa undekha. Ndizo zimene satana wagwiritsa pa moyo wa mkhristu wobadwanso mwatsopano. Tithokoze Mulungu kuti ngakhale satana wagwiritsa pamenepa, komabe mphanvu yakeyo ikhoza kuthyoledwa kupyolera mu njira yodabwitsa yotere ya Nzeru ya Chiombolo.

Mafunso othandiza kuchita nazo zomwe mwaphunzira mu ndimeyi.

A. FUFUZANI

Kodi pali mgwirizano wotani pakati pa “Kulungamitsidwa” ndi “Kuyetsedwa”. Nanga ndi ntchito za ndani? mbali yathu ndi yotani?

Kodi satana amagwiritsa ntchito motani mavesi a pa Aroma 5:18 komanso Aroma 6:23 motisocheretsa kuti tidzibvomereza machimo athu mwa mantha? Nangano kulapa kwenikweni kumabwera motani?

B. PANGANI ICHI KUHALA MOYO WANU !!

Moyo watsopano: “Kuyetsedwa kumatenga ntchito ya kukonzanso khalidwe ndi kuchotsa zizolowezi zomwe zidabwera chifukwa cha moyo wakale wa uchimo.” Funyani ndi pemphero kuti izi zikhaledi moyo wanu... ndipo **KHALANI MOYO WOTERO !!**

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Kodi ndi kusintha kwanji komwe kudzaonekere m'moyo wanga pamene Ambuye Adzayankha pemphero langa).

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Khristu Chilungamo Chathu, (Christ Our Righteousness), Tsamba 99.
2. Khristu Chilungamo Chathu, (Christ Our Righteousness), Tsamba 35.
3. Khristu Chilungamo Chathu, (Christ Our Righteousness), Tsamba 81,82.
4. Khristu Chilungamo Chathu, (Christ Our Righteousness), Tsamba 54.
5. The SDA Bible Commentary, bukhu 5, Tsamba 1082, Mlangizi wa Achinyamata, (The Youth's Instructor), July 20, 1899.
6. Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), bukhu 1, Tsamba 110.
7. Khristu Chilungamo Chathu, (Christ Our Righteousness), Tsamba 104.
8. Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire Of Ages), Tsamba 744

7.

MAKWERERO ANAPANGIDWIRA

Kukwerapo

Kalata yachiwiri ya Petro inalemberedwa kwa gulu la anthu limene, monga iye Petro mwini, lidalandira "...chikhulupiriro cha mtengo wake, womwewo ndi ife, m'chilungamo cha Mulungu wathu ndi Mpulumutsi Yesu Khristu." 2 Petro 1:1.

Zingakhale zobvuta kunena m'chiyankhulo chomveka bwino ndi wina aliyense, kuti anthu awa anali monganso analili Petro, olungamitsidwa – omasulidwa kuchokera ku machimo awo akale – ndipo amayendano m'moyo watsopano.

Chomwecho Petro, pouziridwa ndi Mzimu, akuonetsera kwa akhristu obadwanso kumenewa njira ya Mulungu yakuti chilungamo Chake chiperekedwe kwa iwo ndi kwa ife tomwe.

Petro akunena momveka bwino ndi mwamphamvu pa mutu umenewu wa kuyeretsedwa. Iye akunenetsa kuti "...Zinthu zonse zokhudza moyo ndi umulungu..." zapatsidwa kwa ife. Akunenanso momveka bwino njira imene mphatso zoterezi zimafikira kwa okhulupirira – pokhulupirira malonjezano akuya ndi a mtengo wapatali amene amationetsera ife kuti wokhulupirira amene wabadwanso kachiwiri, akhoza kukhala wolandira nao chikhalidwe cha Mulungu.

Poonjezera apo, iye akunena kuti munthu woteroyu, apulumuka ku chibvundi chiri pa dziko lapansi. 2 Petro 1:3, 4. Chibvundi chomwe chikukambidwa apa ndicho undekha, umene umaononedwa pamene munthu afa ku khalidwe lakale mwa chikhulupiriro. Zotsatira zake ndizo zakuti Yesu amakhozano kulungamitsa wokhulupirira pamene wochimwayo afadi ku uchimo. Aroma 6:12.

Wokhulupirira woteroyu, molingana ndi Paulo, sangolun-

gamitsidwa kokha ndi mwazi wa Yesu (Imfa Yake), komano amapulumsidwa ndi moyo ya Yesu. Aroma 5:10. Kodi moyo wotero ndiwo wotani? Litamandike Dzina Lake loyera ! Uwu ndiwo moyo Wake wangwiro (Khalidwe) lomwe Anakwaniritsa pa dziko kwa zaka makumi atatu ndi theka.

Ndi khalidwe la Yesu Lomwe limaperkekedwa kwa wokhulupirira, limene limatsatira m'zolemba za moyo wakale zomwe zimalembedwa kuti, “monga ngati kuti sin'nachimwepo.” Khalidwe lotereli limakhalano gawo lake la moyo wa munthu wokhulupirirayo pameneno aphunzira kuyenda m'moyo watsopanowu, pokhulupirira Ambuye mulungu wake kuti Adzakwaniritsa zosowa zonse zokhudzana ndi moyo watsopanowu.

Chiyang'aniro chophunzira kuyenda moyo watsopanowu ndicho chodalira kotheratu khalidwe la umulungu, kuti lidzatithandiza kuphwanya zizolowezi zoyipa za khalidwe lathu lakale, zomwe tabwera nazono mu khalidwe lathu latsopanoli, komano limene lapachikidwa naye limodzi pamtanda.

“Pamene Mulungu Agwira ntchito mu mtima, ndipo munthu apereka chifuniro chake kwa Mulungu, ndi kulumikizana Naye, amagwira m'moyowo zomwe Mulungu Amagwira nazo ntchito mwa Mzimu Wake, potero pamakhala chiyanjano pakati pa zolinga za mtima ndi zomwe moyo uchita. Tchimo lirilonse liyenera kulekedwa ndikuonedwa monga chinthu chonyansa chimene chinampachikitsa Ambuye Yesu wamoyo ndi waulemerero pa mtanda, chomwecho wokhulupirirayo akuyenera kukhala ndi moyo wonka chitsogolo pochita mopitiriza ntchito za Yesu Khristu. Ndi pokhapokha tidzipereka chifuniro chatu nthawi ndi nthawi, pokhala omvera, pameneno m'dalitso wa kulungamitsidwa udzakhazikika pa ife.”¹

Panthawiyi, tiyeni tikhazike pa ganizo lakumvera. Apa ndipo pamene mkhristu amalephera. Pomwe tiyenera kukhazikika ndipo pa nkhani ya kudzipereka. Ngati ife titakhala moyo wodzipereka nthawi ndi nthawi, Mulungu Adzagwira ntchito mwa ife “...kufuna ndi kuchita komwe chifukwa cha kukoma mtima Kwake.” Afilipi 2:13.

Khalidwe ndilo limene ife tiri. Mbiri ndiyo imene anthu amaganiza za ife. Khalidwe limaonetsedwa mwa zizolowezi zathu, pamene mbiri imaonetsedwa ndi m'mene ife tiganizira. “Khalidwe limaonetsedwa osati ndi ntchito zowerengeka zabwino zokha ndi ntchito zowerengeka zokha zosakhala bwino, komano ndi chizolowezi cha mawu ndi ntchito zabwino.”²

Kukhala kwa chizolowezi ndiko kukhala momwe ife tikhalira tisakuganizirapo chirichonse. Kukhala kwathu kwa tsiku ndi tsiku kumatsogozedwa ndi maganizo athu a mkatikati. Kudzipereka kwathu ku chitsogozo cha Khristu m'moyo wathu kuyenera kukhala chikhaliidwe chatu cha tsiku ndi tsiku. Kuyenera kukhala chikhaliidwe chatu.

“Tiyenera kuyandikana ndi Mulungu kwambiri, kotero kuti m'mayesero onse odzidzimutsa, maganizo athu ayenera kutembenukira kwa Iye mwa chibadwidwe monga umo duwa litembenukira ku dzuwa.”³

Paulo akutidandaulira ponene kuti, “Mukhale nawo mtima mkati mwanu umene unalinso mwa Khristu Yesu.” Afilipi 2:5 Pomwepo chotsatira ndicho kudzipereka kotheratu monga “... Kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda.” Afilipi 2:8.

Liwu lakui “Mukhale nawo” likutipangitsa ife kuzindikira kuti mphavu yolamulira ili m'manja mwathu. “Yesu Khristu Akudikirira ndi chikhumbokhumbo chachikulu kuti Adzionetsere Yekha ku Mpingo Wake. Pamene khalidwe la Khristu Lidzaonetseredwa kotheratu mwa anthu Ake, pomwepo Iye Adzadza kudzatenga Ake a Iye Mwini.”⁴

Chiyang'aniri choterechi chingathe kufikirika kupyolera mu njira ya Kubadwanso kachiwiri pokhazikika pa mfundo ya Chilungamo chochita nacho chikhulupiriro. Chilungamo chimenechi, chopatsidwa kwa ife mwa chikhulupiriro, ndikukhalanso moyo woyeretsedwa mwa chikhulupiriro, zonsezi ndizo “zonse za pamoyo ndi chipembedzo...” 2 Petro 1:3. Mphatso zozizwitsazi zochokera kwa Mulungu zimakhala zathu pamene ife timulola Iye kutichitira zomwe ife sitingathe kuchita patokha.

Pemphero la Danieli likuyenera kukhala pemphero lathu: “Ambuye, Chilungamo n'cha Inu, koma kwa ife manyazi a nkhope yathu...” Danieli 9:7. Nkobvuta kwa munthu kubvomereza

kuti mwa iye mulibe kalikonse kabwino. Ndipokhapokha “pamene munthu aona kuperewera kwake, pamene angakhale wokonzeka kubvekedwa ndi Chilungamo Cha Khristu.”⁵ Tikamagwiritsa ntchito liwu lakuti “Nkhope ziwiri”, timadziwa zomwe wolankhulayo akutanthauza. Ndikukhulupirira kuti Danieli ankanthauza kuti, “Ambuye, kaya ndibvala nkhope ya maonekedwe otani, mapeto ake ndi kusokonekera, popeza zonse sindizo zenizeni zake.”

O, tikadalakalaka kuti Mulungu Adzionetsere Yekha mwa ife monga Alili, kuti ife tithe kunena pamodzi ndi Paulo kuti, “Pakuti Mulungu Amene Anati, kuunika kudzawala kuturuka mum’dima, ndiye Amene Anawala m’mitima yathu, kutipatsa chiwalitsiro cha chidziwitso cha ulemerero wa Mulungu pankhope pa Yesu Khristu. Koma tiri nacho chuma ichi m’zotengera za dothi, kuti ukulu wokoma wamphamvu ukhale wa Mulungu, wosachokera kwa ife.” 2 Akorinto 4:6,7.

Makwerero a chiyeretso a Petro alembedwa mu 2 Petro 1:5-7. “Muonjezero ukoma pa chikhulupiriro chanu, ndi pa ukoma, chizindikiritso; ndi pa chizindikiritso, chodziletsa; ndi pachodziletsa, chipiriro; ndi pa chipiriro, chipembedzo; ndi pachipembedzo, chikondi cha pa abale; ndi pa chikondi cha pa abale, chikondi.” Apatu Petro akutionetsera ife makwerero amene chiyeretso cha m’Baibulo chikhoza kufikiridwa.

“Chikhulupiriro, ukoma, chizindikiritso, chodziletsa, chipiriro, chipembedzo, chikondi cha pa abale, awa ndiwo makwerero omwe tingakwerepo. Ife timapulumutsidwa pamene tikwera khwerero, kupita pa khwerero linzake, kufikira titafika pamwamba pa makwerero amene takwerapo pamene Yesu Afuna kuti tifikirepo. Chotero Iye Akhala Nzeru yathu, ndi Chilungamo chathu ndi Chiyeretso chathu ndi Chiombolo chathu.”⁶

Tisanayambe kukwera makwerero amenewa tiyenera kudziwa za khalidwe la thabwa la pa khwerero lirilonse. Thabwa lirilonse loponderapo pa khwereroli likuimira khalidwe lathu. Sitingathe ife kuponda thabwa linalo lapamwamba pake, tisanakwaniritse khaliwe loimiridwa ndi thabwa lomwe tapondapo panthawiyo.

Tikhoza kunena kuti makwerero amenewa akufanizidwa ndi mtundu wa chingwe chopota chimene chiri lendelende m'mwamba. Ichi n'chifukwa chake ali makwerero a chikhulupiriro, chifukwa gwero lake liri kumwamba. Iye amene akukwera makwerero amenewa akuyambira pansu kupita m'mwamba pokwera thabwa limodzi pa kanthawi, kuonjezera ku khalidwe lake, ndipo "... Pamene munthuyu akuchita nako kuonjezera, Mulungu Amachita naye munthu wotereyu ndi nzeru yakuonkhetsa." ⁷

Thabwa lililonse pa khwereroli likuyenera kuponedwa popeza matabwa onsewa a pamakwererowa ndi odalirana lina pa linzake. Lachiwiri limadalira pa loyamba. Khalidwe lililonse lotere limankirankirabe lionkhetsedwa ndi Mulungu Mwini pokhapokha ife tikukulabe tsiku ndi tsiku mu Uzimu.

Pali chinthu chimodzinso choonjezera chomwe tiyenera kuchidziwa chokhudza makwererowa:

"Pamaso pa okhulupirira paikidwa kuthekera kodabwitsa kwakuti munthu akhoza kukhala ngati Yesu, womvera ku chifuniro chonse cha Mulungu. Komano pa iye yekha munthu sangathe kufikira chiyang'ani-rochi. Chiyero chimene Mawu a Mulungu Akufuna, chimene munthuyu ayenera kukhala nacho asanafikirepo populumutsidwa, ndicho chotsatira cha Chisomo cha Mulungu, pamene munthuyo awerama pa kumvera ku chidzudzulo ndi chiletso cha Mzimu wa Choonadi.... Mbali ya mkhristu ndiyo kupirira m'kugonjetsa cholakwika chirichonse. Nthawi zonse iye ayenera kupemphera kwa Mpulumutsi kuti Achiritsidwe ku chisalungamo chirichonse cha moyo wake wochimwawu. Munthuyu alibe payekha nzeru, kapena mphamvu zogonjetsera; izi ndi Zake Za Mulungu, ndipo Amapereka kwa iwo amene, podzichepetsa ndi kugonjera afunafuna Thandizo Lake." ⁸

Kodi mwakhoza kuona apa kuti ntchito yathu ndiyo kudziper-eka ku zokumana nazo m'moyo uno, opanda kung'ung'udza, komano kulandira zonse monga zochokera kwa Khristu, ngakhale zinazo zitakhala kuti zachokera kwa satana? Chifukwa mwinjiro wa Khristu umatibveka ife, tiyenera kuzindikira kuti palibe china

chirichonse chomwe chidzatihudza ife chopanda kuloledwa kaye ndi Iye. Aroma 8:28.

Khristu Amabvomereza kuti icho chomwe chitikhudze ife ndi chokhacho chimene chidzathandiza khalidwe lathu kufanana ndi Lake. (Zochokera mu bukhu la Thoughts from the Mount of Blessings, tsamba 71). Pobvomereza choonadi ichi tidzaphunzira kumukhulupirira mu zochitika zonse za m'moyo uno. Potero tidzakhala mwa chikhulupiro osati mwa zooneka. Umo ndi momwe Yesu Khristu Anakhalira moyo Wake padziko pano monga chitsanzo chathu.

Nachi chithunzithunzi china: “Ntchito iyi yokonzanso kuchoka ku chidetso kupita ku chiyeero ndi ntchito yochita mopitiriza. Tsiku ndi tsiku Mulungu Amagwira ntchito yomuyetsa munthu, ndipo munthu ayenera kukhala womvera kulumikizana naye Mulungu mu ntchitoyi, poikirapo mtima kukhala ndi makhalidwe abwino.”⁹ Apatu taona ntchito ya Mulungu, komanso ntchito ya munthu. Ntchito ya Mulungu ndiyo ntchito ya tsiku ndi tsiku pa munthu. Ntchito yathu ndiyo kulumikizana naye Mulungu “pokhala ndi makhalidwe abwino.”

Ngati tingafunedi kukhala ndi makhalidwe abwino, funso lomwe tiyenera kulifunsa ndilo lakuti, zitheka bwanji? Tikhoza kuyesera pogwiritsa ntchito chifuniro, pochita mbali yathu, pochita mobwerezabwerezwa zizolowezi zabwino, kapenanso tikhoza kuyesa pemphero.

Liwu ili lakuti kuyesetsa kukhala ndi chizolowezi, langogwiritsidwa ntchito chifukwa cha kuzama kwa tanthauzo lake lakuya. Ngati titayesera kusintha liwu lakuti zizolowezi, ndikugwiritsa ntchito m'malo mwake liwu lakuti “mbatata” tikhoza kumvetsetsa mosabvuta. Ngati tikubzala mbatata, timadziwa umo tichitira. Timayamba kugalauza nthaka, kenakono kuphwanya zigulumwa kuti nthaka ifewe kuti mbatatayo imere ndi kukula bwino. Nanga tikatero timatani nayo mbatatayo? Timangoisiya m'munda momwemo ndipo Mulungu Amaisamalira, kuipanga kuti imere, ikule. Ife mbali yathu ndi kungopalira, kuchotsa udzu otsamwitsa.

“Iye Ali wolakalaka kuonetsera chisomo chake. Ngati anthu Ake atachotsa zotsamwitsa, Iye Adzatsanulira madzi a chipulumutso m'mitsinje yochuluka kupyolera mu zipangizo za anthu.”¹⁰

“Palibe chinthu chimene satana amachita nacho mantha kwambiri choposa kuona anthu a Mulungu akuchotsa m’ moyo mwao zotsamwitsa zonse, ndi kulola Mulungu kutsanulira Mzimu Wake pa Mpingo Wake obvutika ndi wosalapa.”¹¹

Tapeza kale kuti sitingathe kusintha moyo wathu. “Kodi angathe M’kusi kusanduliza khungu lake? Kapena nyalugwe maanga ake? Pamenepo mungathe inunso kuchita zabwino, inu amene muzolowera kuchita zoipa.” Yeremiya 13:23. Ntchito yathu pochotsa zotsamwitsa ndi zopinga za mu khalidwe lathu ndiyo kuzizindikira mwachangu pamene taziona. Pomwepo tiyenera kupemphera kosalekeza kwa Mulungu kuti Achiritse moyo wathu wodzadza ndi uchimowu. Iye Adzachotsa zotsamwitsazi pamene ife tiri okonzeka kuletsa kuikira kumbuyo zotsamwitsa zimenezi. Tiyenera kusiyanita pakati pa tchire ndi mbewu yeniyeni.

Zipatso za Mzimu ndizo mbewu za nthete zofunika kulimidwa bwino kufikira zitazikika mizu. Pomwepo zimakhala zokhazikika kufikira tikhoza kunena pamodzi ndi Paulo kuti, “...Kuchitira umboni uthenga wabwino wa chisomo...” Machitidwe 20:24.

Ntchito yonseyi yokonzekera, pamodzi ndi kukwera makwerero a Petro, ndiyo ntchito ya chikhulupiriro. “Alipo ena amene amayeserera kukwera makwerero a moyo wopitirirawu wa chikhristu; komano pamene akuyenda chotero, amayambano kuika chikhulupiriro chawo mwa munthu, potero amachotsa maso awo pa Yesu Khristu, Amene Ali Chiyambi ndi Mapeto a chikhulupiriro chawo. Zotsatira zake zimakhala kulephera.” (Machitidwe a Atumwi, Tsamba 532.)

Timvetse apa kuti Kuyeretsedwa, monganso kulungamitsidwa, ndi ntchito ya chikhulupiriro pa ulendo wathu wonse.

“Otsatira a Yesu akuyenera kufanana ndi Iye mu zonse – mwa Chisomo Cha Mulungu kupanga makhalidwe oyanjana ndi Lamulo Lake Lachiyero. Uku ndiko kuyeretsedwa molingana ndi Baibulo. Ntchito yotere ingakwaniritsidwe pokhapokha mwa chikhulupiriro mwa Yesu, pothandizidwa ndi Mphamvu Ya Mzimu Woyera Wa Mulungu Wokhala mwa ife.”¹²

“Mwa ife tokha sitingathe kuchita kena kalikonse kabwino; komano icho chomwe ife sitingathe, chidzatheka ndi mphamvu Ya Mulungu m’oyo wa mkhristu aliyense amene ali wodzipereka ndi wokhulupirira. Ndi kupyolera mwa chikhulupiriro m’mene moyo wa uzi-mu umabadwa, potero timapatsidwa kuthekera kochita ntchito za chilungamo.”¹³

“Palibe wina koma Khristu Amene Angathe kukonzanso khalidwe limene laonongedwa ndi uchimo. Iye Anadza kudzachotsa ziwanda zimene zimalamulira chifuniro cha munthu.”¹⁴

“Ndi kupyolera mu kutengapo mbali mu Chisomo Cha Khristu pamene tchimo limatha kuonekera mu chikhalidwe chake choipa, ndikuchotsedwa mu kachisi wa moyo wa munthu.”¹⁵

Ziganizo izi zikutiuza momveka bwino kuti pokhapokha pamene titengapo mbali mu khalidwe la Khristu mu chiyeretso, pamene tidzatha kulionadi tchimo umo momwe lirili – nthenda yakupha. Ndipokhapo pomwe ife tidzatha kudana nalo. Mfundoyi tingathe kuimvetsa bwino pokhapokha titayamba kukwera makwererowa.

Mutha kuona kuti tikugwiritsa ntchito liwu lakuti tchimo, lomwe likuloza ku nthenda, osati machimo, omwe ndi zizindikiro za nthenda. Tikhozano kupeza mophweka udani wa machimo womwe umasonyeza kuti pali chikhalidwe cha chibadwa cha uchimo komwe uchimowo uchokera. Komano nthawi zambiri ife timakhazikika pa zizindikiro za nthenda, malo mwa nthenda yeneyeni. Izi ndi zimene satana amafuna ife kuti tizichita. Chifukwa ndi pokhapokha ngati ife tachotsa nthendayo, satana amadziwa kuti zizindikiro za nthenda zokhazo nzokwanira kutitanganitsa ife kulimbana komanso kugonjetsedwa nao,

Ndi mfundo yodziwika imene nthawi zambiri timailambalala yakuti munthu aliyense mu chibadwa chake cha umunthu, ali nayo nthenda yoopsa imeneyi ya tchimo. M’kuona kwa Mulungu, nthendayi ndi yoopsa mbali zonse za moyo wathu. Komabe, zizindikiro zina n’zobvomerezeka poyang’anira ubwino wa

anthu, pomwe zizindikiro zina nzosabvomerezeka chifukwa n'zomui pitsiratu munthu.

Tiyenera kumulola Mulungu kut Atibvumbulutsire khalidwe lowononga lotere, ndikutibweretsa ife pa malo pamene tidzatha kuliona tchimo monga umo Iye Aonera. Pomwepo tidzakhalano omasuka ku zikadabo zake za tchimo. N'chifukwa chiyani izi ziri zobvuta kwa munthu kuti azione? Chifukwa chakuti mitima yathuyi ndi youma ndi tchimo, yofa dzanzi, kotero kuti sititha kuliona tchimo pamene tikomana nalo. Tsoka lake ndilo lakuti pamene tikhala moyo wotere timaiwala kuti "Iye, [Khristu] Anali Mfulu ku chidetso cha tchimo, chikhaliidwe Chake Chosalala ndi chazimu chidapangitsa tchimo kukhala lowawitsa m'moyo Mwake." ¹⁶ Ntchito yaikulu nanga yomwe tiyenera kuchita, kuti tionetsere chifanizo chake mopanda banga.

Tisanayambe kukwera khwereroli la chiyeretso, tatiyeni tione ndondomeko zomwe ziri mu, (Gawo C, pa tsamba 154,155). Apa tione m'mene satana ali nayo njira yake yachinyengo ya m'mene ife tingakhalire ndi chiyero, njira yomwe satanayo amagwirit-sira ntchito pa choonadi chirichonse cha m'Baibulo. Njira ya Mulungu imayamba ndi chikhulupiriro kumalizira ndi chikondi (Chikondi cha Umulungu). Njira ya satana imayamba ndi undekha, kuchangamuka, ndipo imamalizira ndi kutengekatengeka.

Njira ya satana imabweretsa zopinga, zotchinga zomwe zimamulepheretsa mkhristu kuti asakule ndi khalidwe la Khristu. Makhaliidwe oterewa amakhala akulirakulirabe mphamvu, potero amatchinga kuti chikondi cha Umulungu chisafikirike. M'malo mwake mumakhalano mlowam'malo wokongola, wachikoka ndi wachinyengo amene amadziwika ndi matengekatengeka. Ndi mbali imeneyi yotengekatengeka imene satana wamanga nsinga anthu miyandamiyanda omwe amadzitcha okha akhristu.

Sindikufuna kupereka ganizo lakuti mu za Umulungu mulibe kutengeka kwina kulikonse. Ayi, kulimo ndithu. Komano ndi Chikondi Cha Khristu Chimene Chimatikakamiza ife. 2 Akorinto 5:15. Chikondi Cha Khristu ndicho chimatimanga ife tonse pamodzi. Izi ndizo zotsatira za Chikondi Cha Umulungu.

Kutengekatengeka, kumatengera za kuthupi, kwenikweni kwa iwo amene amvetsetsana okhaokha. Pamene mbali inayi, Chikondi Cha Khristu chimafikira ndi kukupatira ngakhale iwo wonse amene atsutsana ndi kulimbana nacho. Chimabvomera

mafuno ena aliwonse, abwino, kaya oipa, komano chimabwezera chikondi chokhachokha m'malo mwake. Iyi zedi ndi mphatso yochokera kwa Mulungu. Izi ndizo zimene Chiyeretso chimachita.

Tiyeneranso kukumbukira kuti m'khristu, pamene akulora Mulungu kukuza khalidwe Lake m'moyo wa munthuyo, mkhristuyo amakula mu chisomo (Chomwe chiri khalidwe La Mulungu), osati mwa chisomo (Khalidwe la Mulungu).¹⁷ M'mene izi zichitikira n'kobvuta kuzizindikira komano zotsatira zake zimakhala zowonekera kwa okhulupirirayo ndi kwa onse omuzungulira.

Kumbukirani kuti pamene tikukwera makwererowa, Phazi lililonse pa thabwa lililonse limayendedwa mwa chikhulupiriro monga momwe zafotokozeredwa pa chithunzi cha ndondomeko chija.

Inde, Makwerero anapangiridwa kukwerapo, ndipo ife tatsala pan'gono kutino tiyambepo. Chotero tiyeni tipemphere kuti Mulungu atibvumbulutsire zotilepheretsa zonse, ndi zotchinga zonse zomwe zidza Mulepheretse Iye kubereka mwa ife chipatso cha chilungamo. Tatiyeni tingounikira mwachangu khalidwe la chipatso chomwe tingayembekezere kwa Iye, pamene Akugwira ntchito Yake yozizwitsa mwa ife. "...Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso, chiletso..." Agalatiya 5:22.23.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwaphunzira mu ndimeyi:

A. FUFUZANI

Ndi chiyani chomwe Khristu Amalolera kuti chitikhudze, nanga chifukwa ninji?

"Kodi njira ya Mulungu Imayamba ndi chiyani ndipo imathera ndi chiyani? Kubera kwa satana kumayamba ndi kumaliza ndi chiyani?"

(Mukhoza kupeza yankho pa: Zothandizira, mbali C ndi mbali D).

B. PANGANI KUKHALA KHALIDWE LANU !!

"Tikumbukirenso kuti m'khristu, pamene akubvomereza

Mulungu kukuza khalidwe Lake mwa iye, mkhristuyo amakula mu chisomo (Khalidwe la Mulungu) osati mwa chisomo (Khalidwe La Mulungu). Izi zimakhala zobvuta kuzizindikira komano zimakhala zoonekera kwa okhulupirirayo ndi kwa onse omuzungulira.” Pemphani kuti ili likhale khalidwe lanu... ndipo KHALANI MOTERO !!

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Kusintha komwe kudzakhala m’moyo wanga pamene Ambuye Ayankha pemphero langa).

Mabuku Omwe Agwiritsidwa Ntchito:

1. Mauthenga Osankhika (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 397.
2. Mapazi Opita Kwa Khristu, (Steps To Christ), Tsamba 57, 58.
3. Mapazi Opita Kwa Khristu, (Steps To Christ), Tsamba 99,100.
4. Mafanizo A Yesu, (Christ Object Lessons), Tsamba 69
5. Khristu Chilungamo chathu,(Christ Our Righteousness), Tsamba 104, The Review and Herald, September 16, 1902.
6. Machitidwe a Atumwi, (The Acts Of The Apostles), Tsamba 530.
7. Machitidwe a Atumwi, (The Acts Of The Apostles), Tsamba 532.
8. Machitidwe a Atumwi, (The ACTS Of The Apostles), Tsamba 532.(Owonjezeredwa).
9. Machitidwe a Atumwi, (The Acts Of The Apostles), Tsamba 532.
10. Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 251 (Owonjezeredwa).
11. Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 124.
12. Mkangano Waukulu, (The Great Controversy), Tsamba 469.
13. Chokhumba Cha Mibadwo (The Desire Of Ages), Tsamba 98.
14. Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire Of Ages), Tsamba 38.
15. Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 366.
16. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7A, Tsamba 451, The Review and Herald, Nov 8, 1887.
17. Mafanizo A Yesu, (Christ Object Lessons), Tsamba 271.

8.

“Kuonjezera Ku Chikhulupiriro”

MAZIKO OLIMBA

Usanayambe kukwera Makwerero, munthu umayamba waona malo amene makwererowo ayima kapena kukhazikika! Chotero, popeza phazi loyamba la Makwererowa ndi chikhulupiriro, tiyeni tiyambe ndi mfundo yakuti Maziko ake ndiwo chikhulupiriro.

Petro akuyankhula uthenga wake kwa iwo, amenenso monga iye mwini, ayasedwa olungama mwa chikhulupiriro. Koma tikhoza kumva wina akuti, “Mwatiuza kale kuti Makwererowa ngolendewera kuchokera kumwamba, ndikuti sanakhazikike pa china chirichonse cha pansu pano.” Izi n’zoon. N’chifukwa chake tikunena kuti maziko ake ndiwo chikhulupiriro. Paulo adati, “...Koma moyo umene ndiri nawo tsopano m’thupi, ndiri nawo m’chikhulupiriro cha Mwana wa Mulungu...” Agalatiya 2:20. Tisunge m’maganzizo mwathumo kuti maziko, komanso thabwa lililonse la pa khwereroli, ndi za mwa chikhulupiriro chochokera kumwamba. Kumbukirani, “...Pakuti Mwa Iye tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda ndi kupeza m’khalidwe wathu...” Machitidwe 17: 28. “...Ndipo simukhala a inu nokha. Pakuti munagulidwa ndi mwazi...” 1 Akorinto 6: 19 -20. Mtengo umene tinagulidwa nawo ndiye mwazi wa Yesu Okhetsedwa pa mtanda, kuti Khristu akhale Woyenera mobvomerezeka ndi chilamulo kuti Akakhoze kutilungamitsa Iye Mwini, Natiombola ife kwa ife tokha. Ganizo lakuti tiyenera ife kuombedwa kwa ife tokha likhoza kukhala lobvuta kulilandira kwa ambiri a ife.

Chithunzithunzi chomwe Mulungu Akutipatsa chokhudza Israeli wakale chikutionetsa chithunzithunzi chathu chenecheni monga tiliri lero: “...Mutu wonse uli kudwala ndi mtima wonse walefuka. Kuchokera pansu pa phazi kufikira ku mutu mmene-mo mulibe changwiwo; koma mabala ndi mikwingwirima, ndi

zirona; sizinapole, ngakhale kumangidwa, ngakhale kupakidwa mafuta.” Yesaya 1: 5-6.

Kodi ife sitingathokoze kuti mu njira Yake ya Mulungu Yolungamitsira munthu, munthu wakaleyu amafa ? pomwepo timapatsidwa ife moyo watsopano mwa Khristu, monga momwe Paulo akunenera , “Chifukwa chake ngati munthu ali mwa Khristu ali cholengedwa chatsopano: (chilengedwe) zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano.” 2 Akorinto 5:17. Iyi ndi mfundo yokhazikika pa malonjezano a Mulungu. Izi, molingana ndi Petro zimatikhozetsa ife kutenga nawo mbali mu khalidwe la Umulungu.

Tiyenera kudziwa ichi nthawi zonse kuti ife timakhala anthu atsopano mwa Yesu. Pokwera makwerero amenewa a Petro, nthawi ndi nthawi tidzapeza kuti m’matupi athu muli kulimbana ndi kamphamvu kena, kofuna kulimbana ndi umulungu wa mkati mwathu pochita nkhondo ndi chitsogozo cha Mzimu pa ulendo wathu uwu wa chikhulupiriro. Nthawi zambiri tidzanena monga ngati Paulo, “Munthu wosauka ine; adzandilanditsa ndani m’thupi la imfa iyi ?” Aroma 7:24.

Nkofunikira kwa ife kukumbukira kuti nkhondo iyi ya pakati pa Khristu – Yemwe ndi Wolamulira Watsopano wa munthu uyu watsopano – ndi satana – mtsogoleri wogonjetsedwa wa munthu wakale – nkhondoyi idakamenyedwabe mowirikiza, popeza satana wakwiya. Njira yake yakale ya satanayo yolamulira moyo wathu inali yodzera mu zizolowezi zathu zoipa. Tisaiwale kuti khalidwe limaonetsedwa mkupyolera mu zizolowezi zathu.

“Wonyengayo, kusiyana kwa maonekedwe a wina aliyense, zizolowezi zomwe zimapanga khalidwe lathu – chirichonse chomwe timapanga tikakhala pakhomopathu, zidzaonekera m’aganizo athu, m’mawu athu ndi m’machitachita a chikhalidwe chomwecho.”¹

Timawerenganso motere:

“Banga limene limaonetsedwa pochita ndi zinthu zing’onozing’ono za m’moyo uno, zimafikira kukhalano zinthu zikuluzikulu...

...Potero, machitachita athu obwerezabwereza, amapanga zizolowezi, ndipo zizolowezi zimapanga

khalidwe, ndipo khalidwe limapanga matsiriziro athu a nthawi zamuyaya.”²

Ndi mfundo zimenezi zokhazikika m’ maganizo athu, tikhoza kuona kuti nkhondo yeniyeni iri pakati pa uyo amene ife eni tamupanga kulamulira maganizo athu. Potero tikuyenera kukhala ndi maganizo osadetsedwa, kuti tikhoze kuzindikira kusiyana kwa mphamvu ziwirizi zomwe zikulimbana ndi ulamuliro wa pa maganizo athu. Tsopano ,tiyenino tidzione tokha ngati zisankho zathu zambiri za mmoyo uno zinapangidwa potsatira mfundo zachilungamo, kapena pongotengeka ndi mmene ife tikumvera mthupimo pa nthawi imeneyo. Ngati tingakhale owona pa ife tokha, tikhoza kupeza kuti zisankho zambiri zakhala zikupangika pongotsatira umo m’mene tikumvera m’thupi pa nthawiyo, kuphatikizapo zisankho zokhudza moyo wathu wa Uzimu womwe. Kumva kwa m’thupi kumeneku, kumene satana wakupanga kukhala njira yake yodzeramo ndi mpita wake, kwapanga mwa ife zizolowezi zolimba kotero kuti satana sangangokhala manja ntambasale kuonerera zizolowezi zoipazi zikufa mwa ife, kopanda iyeyo kumenyapo nkhondo. Kuyankha kwathu ku chirichonse cha m’ moyo wathu kudzatengera zizolowezi zathu za mgonagona. Ngati ife titachita molingana ndi umo timvera, apo ndipo satana amatengano ulamuliro onse kenakono amatitsutsa, kutidzudzula ndi kutikhumudwitsa. Potero amayesetsa kutipanga ife kuti tikhulupirire kuti kulungamitsidwa kwathu sikwenikweni ndi kuti ifeyo tikungodzipusitsa tokha.

Mkhristu wobadwanso mwa Khristu, amene akukhala mwa chikhulupiriro, akuyenera kudziphunzitsa yekha zomwe angelo adalangiza Adamu ndi Hava kuchita pamene satana adzawayesa iwo. Apa ndipo pamene nkhondo yathuyi imaoneka yotikulira. Makolo athu oyamba analephera, komabe mwa Khristu ife tikhoza kupambana ! zingatheke bwanji? Adamu ndi Hava adauzidwa kuti akane machenjerero a satana potero adzakhala otetezedwa.³ Tiyenera ife kuzindikira pamene mdaniyo akugwira ntchito poona zizolowezi zathu, ndipo tikatero tizindikire ufooko wathu, pomwepo titembujukire kwa Khristu kufuna thandizo la kwa Iye. Tibvomereze apa kuti sitingathe kugonjetsa mochita kulimbana, kaya tiyese bwanji ! Pamene tikumana ndi maufooko athu, ndipo nthawi yomweyo titembujukira kwa Khristu, Iye

Amagwiritsa ntchito mayesero omwewo monga chida m' manja Mwake chotikonzeranso ife khalidwe lathu. "Palibe wina koma Khristu Yekha Ndiye amene angathenso kukhonza khalidwe limene laonongeka ndi tchimo. Iye Anadza kudzaononga ziwanda zimene zinali kulamulira chifuniro chathu." ⁴

Mu njira yonseyi yokwera Makwererowa, Khristu Mwi-ni amakhala kalikiliki kupanga khalidwe limeneli latsopano, pamene ife tiri otanganidwa kudzipereka ku ntchito Yake yotikonzanso. Uwu ndi udindo wa wina aliyense wa ife ku nthawi zonse. Ndi pokhapokha pamene ife, pogonjera kwa Iye, titsegula khomo kulola kuti Iye Agwiremo ntchito Yake mu chilengedwe Chake chatsopano.

Tiyenera ife nthawi ndi nthawi kuchotsa zotsamwitsa ndi zopinga zimene zimalepheretsa Iye kugwira ntchito m'moyo wathu. Ngakhale m'kudziperekaku, muli chimwemwe podzi-wa kuti, "Koma Mulungu wa mtendere Amene anabwera Naye woturuka mwa akufa M'busa wamkuru wa Nkhosa ndi mwazi wa chipangano chosatha, ndiye Ambuye Wathu Yesu; Kwa Iyeyu ukhale ulemmero ku nthawi za nthawi. Amen." Ahebri 13:20-21.

Ngakhale pamene Yesu Khristu Anali wopambana kupyolera mwa kudzipereka pamene m'maso mwa anthu zinkaoneka ngati wagonja ndi kulephera, choteronso ife tonse tiri nayo njira imodzi yokha yonka nayo ku chipambano. Makwererowa adzakhala obvuta kukwerapo, osati chifukwa chakuti ndi ophedika, kape-na okhakhala ndi ogobeka, koma chifukwa chakuti undekha udzayesetsa kuchita ntchito yomwe ndi yoyenera Mulungu Yekha kuichita, m'malo mochita ntchito yomwe ife tiyenera kuchita - ntchito ya kugonja ndi kudzipereka.

Ziripo zopinga zomwe ziyenera kuchotsedwa munthu asanayambe ulendo wokwera makwererowa. Ngati undekha sunafe kupyolera mu kulungamitsidwa, sitingathe ife kukwera makwerero amenewa a Petro, komano tidzapezeka kuti tikukwera Makwerero ena olakwika.

"Kubadwanso mwatsopano ndi chochitika chosowa mu m'badwo uno wa dziko. Ichi n'chifukwa chake pali mikwingwirima yochuluka m'mipingo yathu. Anthu miyandamiyanda, amene amadzitcha okha Akhristu ali opanda chiyero. Anabatizidwa, komano adakwiridwa

adakali amoyo. Undekha udali usadafe mwa iwo, potero iwo adali asadadzuke ku moyo watsopano wa mwa Khristu.”⁵

Paulo akunena kuti, “Pakuti ngati ife tinakhala olumikizidwa ndi iye m’chifanizidwe cha imfa Yake, choteronso tidzakhala m’chifanizidwe cha kuuka kwake.” Aroma 6:5. Paulo akupitiriza ndikuti, “...tinayanjanitsidwa ndi Mulungu mwa imfa Ya Mwana Wake makamaka ndithu popeza ife tayanjanitsidwa ndi iye, tidzapulumuka ndi Moyo Wake.” Aroma 5:10. Pamene kulungamitsidwa kumanyamula mbali yonse yokhudzana ndi zachilamulo, Kuyeretsedwa – komwe ndi kutengera khalidwe la Khristu – ndi ntchito imene kuyenereredwa kwathu kwa kumwamba kumakhazikitsidwa. Kulungamitsidwa popanda kuyeretsedwa, kulibe mphamvu ya kupulumutsa, komanso, kuyeretsedwa paokha, popanda kulungamitsidwa nkosatheka.

“Mulungu Amafuna kudzipereka kwathunthu kwa Mtima, kulungamitsidwa kusanachitike; ndipo pofuna kuti munthu alandire kulungamitsidwaku, payenera kukhala kumvera kopitirira kupyolera mu chikhulupiriro cha machitachita, chikhulupiriro choonekera m’chikondi ndi choyeretsa moyo.”⁶ Iyi ndiyo ntchito ya chiyeretso.

“Apa, choonadi chaonetsedwa pamtetete. Ubwino woterewu ndi chifundo choterechi n’chosatiyenera. Chisomo Cha Khristu ndi cholungamitsa munthu kwaulere kopanda munthuyo kukhala nako kuyeneretsedwa kulikonse. Kulungamitsidwa ndiko kukhululukidwa kotheratu kwa tchimo. Nthawi yomwe wochimwa alandira Khristu mwa chikhulupiriro, nthawi yomweyo wochimwayo amakhululukidwa. Chilungamo cha Khristu Chimapatsidwa kwa iye kukhala mbali ya moyo wake., potero sayeneranso kukayikira chisomo cha Mulungu chokhululukira.”⁷

Ngati inu simunalandire kulungamitsidwaku mwa chikhulupiriro, kudzipereka kwathunthu kwa inu mwa Khristu, ndi kulandira imfa yake pamtanda monga yanu ya inu eni, kufa ku

undekha, ndingokupemphani kuti muwerame mutu wanu tsopano, pempherani mwakachetechete, ndi kulowa mu chipambano Chake choperekedwa kwa inu.

Mafunso othandizira kuchita zomwe mwawerenga mu ndimeyi:

A. FUFUZANI

N'chifukwa chani kukhazikika pa m'mene munthu ukumvera kuli kowononga? Kodi Angelo adawauza Adamu ndi Hava kuti achite chiyani potsutsana ndi satana?
Kodi 'njira imodzi ya ku chipambano' ndiyo iti?

B. PANGANI KUKHALA MOYO WANU !!

“Mulungu Amafuna kudzipereka konse kwa Mtima, kulungamitsidwa kusanachitike; ndipo pofuna kuti munthu akhalenso ndi kulungamitsidwaku, pakuyenera kukhala kumvera kwa nthawi zonse kupyolera mu chikhulupiro chochitachita choonekera m'chikondi ndi kuyeretsa moyo.”

Funsani ndi pemphero kuti izi zikhale mbali ya moyo wanu...
ndipo.... **KHALANI MOYO WOTERO !!**

Chifkwa pemphero ili layankhidwa, moyo wanga udzakhala wotere: (Ndi kusintha kotani komwe kudzachitika m'moyo wanga pamene Ambuye Ayankha pempho langa).

Mabuku Omwe Agwiritsidwa Ntchito:

1. Maumboni, (Testimonies), Bukhu 6, Tsamba 174.
2. Mafanizo A Yesu, (Christ Object Lessons), Tsamba 356.
3. Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 53.
4. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 53.
5. The SDA Bible Commentary, Bukhu 6, Tsamba 1075, Akalata 148, 1897
6. Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 366.
7. The SDA Bible Commentary, Bukhu 6, Tsamba 1071, Zizindikiro za Nthawi, (The Signs of the Times), May, 1898.

9.

KUTAMBASULA MAZIKO A

“Chikalidwe Chabwino”

Pamene mkhristu abwera kwa Khristu odzipereka kwathunthu, mkhristuyo amalandira Khritu monga Mpulumutsi wake wompulumutsa ku machimo. Chokhumba chakeno chimakhala maganizo a moyo wamuyaya. Mwa Khristu, amamvano kutezedwa ndipo safunikanso kudandaula kuti “n’dzalowa bwanji” kumwamba. Mpumulo wake umakhala wodalitsika ndi wotsimikizika. Izi zikhoza kungokhala za kanthawi kochepa kokha, kapenanso zikhoza kukhala zamuyaya. Komabe, kwa ofunafuna choonadiyo zidzafika nthawi zimene iye adzapeze kuti moyo wa Chikhristu sindiwo moyo wamtambasale pa “mpando wa ndakhuta ndalema” komano ndi moyo wa matakadzo, woyenda tsiku ndi tsiku m’dziko ili la uchimo. Iye adzapeza kuti ndi chinthu china kukhala mkhristu pakati pa akhristu – abwenzi omuthangatira, omupempherera ndi kumulimbikitsa. Iye adzapezanso kuti ndi chinthu china kukhala moyo watsopano woterewu pa malo osiyaniranatu ndi ake a poyamba. Iye adzapeza kuti ngakhale m’nyumba mwake momwe mudzakhala mobvuta kukhalamo ndi moyo wauzimu, poyerekeza ndi ku Tchaliichi kapena ndi anzake amene anamuthandiza kudziwa za Khristu. Iye adzapezanso kuti ngakhale ntchito yake yomwe idzafunika kupanga zisankho zochititsa manyazi ngakhale kwa iye mwini, popezano wakhala Mkhristu. Adzapeza kuti mwayi wochulukuka ukumutsegukira umene akadakhocha kupanga nawo phindu lochulukuka ngati akadangotayirira pang’ono pokha m’moyo wake watsopanowo. Chinthu chofunika kuchita mu zonsezi ndiko kuganiza mwakuya. Nkobvuta kwa ife kukumbukira kuti chikhulupiriro sichidalira kuganiza mwakuya. Zimafunika Nzeru ya Kumwamba kuti tipeze

mayankho olondola. Yesu Adati, “Tiyeni tsono tiweruzane...” Yesaya 1:18. “Mwandikhulupirira Ine pa chipulumutso chanu. Kodi mungandikhulupirirensa kuti Ndikhoza kusamalira zosowa zanu za tsiku ndi tsiku? Kodi mungandilole kulamulira mbali zonse za maganizo anu?” Iye Adalonjeza kuti ngati ife titachita izi Iye Adzakwaniritsa zosowa zathu zonse, komanso kuonjezera apo, kutipatsa ife moyo wosatha kulowa mu Ufumu Wake.

Izitu sizikutanthauza kuti moyo wantambasale uja wa “Mpando wa ndakhuta ndalema” ndiwo mayankho a zonse. Ndi chopatsa chithonhozo kudziwa kuti ndikuyenera kudzipereka ndekha kwathunthu kwa Khristu, m’moyo watsopanowu wa chikhulupiriro, monganso umo ndidadzipereka kwanthunthu m’moyo wanga woyamba uja ku uchimo. Paulo akuti, “...Pakuti monga inu munapereka ziwalo zanu zikhale akapolo a chonyansa ndi a kusayeruzika kuti zichite kusayeruzika, inde, kotero tsopano perekani ziwalo zanu zikhale akapolo a chilungamo kuti zichite chiyeretso.” Aroma 6:19.

Yesu adakhala moyo wodzipereka kwathunthu wotero, komabe Adali ndi chiyang’aniro chachikulu, Wamphamvu ndi Wosamalitsa kuchita zoyenera zomwe Adayenera kuchita. Iye sadali wokwanitsidwa ndi zinthu zawamba. Chomwecho, mkhristu amene wabadwanso mwa Khristu akuyenera kuchita mbali yake yoona, ngakhale pakuoneka kuti palibe phindu lake la kwa iye yekha. Phindu lake ndi la mtengo wapatali losati lofanana ndi khalidwe la padziko. Mulungu Angathe, ndipo Adzaika munthu woteroyo m’malo a ulamuliro amene adzaonetsera Ulemerero Wake Wa Mulungu (Khalidwe) potero adzakhala monga ngati mphamvu ya nyetsi, kapena kuti maginito, yokokera anthu onse kwa Khristu.

Tanena kale kuti Khristu Amagwira ntchito yake kuyambira mkati, kenakono kunja. (Monga zalembedwa mu gawo D la zothandizira) ndipo Iye Akutsatira njira Yakeyi pogwiritsa ntchito Chiyeretso monga taphunzirira mu Makwerero a Petro. Matabwa atatu oyambirira pa Makwerero aja, akukhudzana ndi m’mene ife tiganizira. Ngati maganizo athu aperekedwa kwa Iye, sitidzakhala ndi bvuto ndi zakuthupi. “Mukhale nawo mti-ma mkati mwanu Umene Unalinso mwa Khristu Yesu.” Afilipi 2:5. Onani kuti nkhani iri apa ndiyo “Yotsegula” – kudzipereka kogonjera kuchoka ku kaganizidwe kathu ka chibadwa. Moyo

watsopanowu wa chikhulupiriro umafikira ngodya zonse za zochitika m'moyo wathu. Moyo wotere umakhulupirira Khristu ngakhale sitingadziwe m'mene Iye Adzagwirira ntchito Yake. Chikhulupiriro chenicheni sichikhazikika pa njira zomwe Iye Agwiritsa ntchito – komano pa zotsatira zomwe Iye Adalonjeza.

Komatu pali zolepheretsa ku chikhulupiriro choterechi. Kukayika ndicho chida champhamvu chodalirika cha satana. Kodi mwatha kuona kuti pamene satana achita ndi munthu wosakhulupirira amayesetsa kumuchotseratu kwa Khristu, Baibulo ndi Choonadi? Komano pamene satanayu agwira ntchito ndi mkhristu, iyeyu amagwiritsa ntchito chikayiko. Njira imeneyi adagwiritsa ntchito ponamiza Hava. Adayesetsa kuti asasemphanitse ndi zomwe Mulungu Adanena. Komano adayesetsa kubweretsa chikayiko chachikulu pa chifukwa chimene Mulungu Adanenera choletsedwacho. Atathano kubweretsa chikayikochi m'maganizo a Hava, pambuyo pakeno panabwera kukana choonadi. Komatu chikhalirenicho Havayu adali atachenjezedwa kale za choopsachi chochokera kwa mdani. Pomwepo adamva chikakamizo chothawira kwa mwamuna wake - Adamu. Adamvano ngati kuti angakhale atakumana naye m'daniyo iye adali ndi mphamvu zokwanira kumugonjetsa. Tsopano pokomana naye, mdaniyo atadzizimbayitsa, adapezeka kuti akukangana naye.¹ Palibe chinthu china chomwe chimamukondweretsa satana choposa kulowa naye mkhristu mu mkangano. “Iye amayesa anthu kuti asakhulupirire Chikondi Cha Mulungu ndi kukaikira Nzeru Yake. Nthawi zonse iye akuyesetsa kubweretsa mzimu wa kufunafuna kopanda phindu, chilakolako chofuna kufufuza zakuya za nzeru ndi Mphamvu ya Mulungu.”²

“Pali njira imodzi yokha yomwe iyenera kutengedwa, kwa iwo amene afunafunadi kukhala womasuka ku chikaiko choterechi. M'malo molimbana ndi kufunsafunsa za Mulungu, izo zomwe iwo sangathe kumvetsetsa, iwo akuyenera kungogwiritsa ntchito kuwala komwe kulipo kale, ndipo potero adzalandira kuwala koposera apo.”³

Ntchito yathu ndiyo kuyenda mwa chikhulupiriro, komwe kumafunikira kumvera, ngakhale sitingathe kudziwa “Chifukwa chiyani.”

Ahebri 11, yomwe ndi ndime yaikulu yokhudza Chikhulupiriro, imanena kuti Chikhulupiriro “ndicho,” osati “chakhala” chikhazikitso cha zinthu zoyembekezeka. Zingakhale zobvuta kwa ife kuona kusiyana kwa zinthu ziwiri izi za chikhulupiriro. Nthawi zambiri timangofuna kudziwa ngati ife tiri nachodi chikhulupirirocho. Nanga timafufuza kuti? Nthawi zambiri timafufuza za m’mene ife eni tikumvera m’thupi mwathumu! Timanena kuti, “Ndikumva ngati motere kapena motero.” Chikhulupiriro chathu chikuyenera kukhazikika pa china chodalirika choposa mamveredwe a mthupi. Poterepa ndipo pa bwalo la zamasewero la satana mdierekezi. “Chikhulupiriro sichingotanthauza kukhulupirira kokha, koma kukhulupirira kotheratu.”⁴ “ziwanda zikhulupiranso ndipo zinthunthumira” Yakobo 2:19. Kukhulupira kwa ziwanda mwachidziwikire sindiko chikhulupiriro.

Nchifukwa chiyani kumvetsetsa uku kuli kofunikira pa Makwerero aja a Petro? Ndi chifukwa chakuti, “Palibe wina amene angathe kukonzanso khalidwe lowonongeka ndi uchimo koma Khristu Yekha Ndiye.”⁵ Funso leneleni lomwe liyenera kuyankhidwa ndi aliyense wa ife ndilo lakuti, kodi tiri ololera kumlora Iye kuti Agwire ntchito Yake mwa ife, kapena ife tikungofuna mbali inayo tigwire tokha? Mtimawu umalalakala “kuthandizirapo.” Komano tiyeni timulekere Woumba mbiya Atiumbe mwa luso Lake, ifeyo tingokhala odekha m’Manja Ake. Ndi pokhapo pamene mbiya yotuluka m’Manjamo idzakhala ya mtengo wapatali !

Mafunso othandizira kuchita zomwe mwaphunzira m’ndimeyi:

A. FUFUZANI

Kodi mungadalire kupeza zifukwa mu nkondo yomenyana ndi choipa ? Chifuwa chiyani ?

Kodi Chikhulupiriro choona chakhazikika pa njira za Mulungu kapena pa malonjezano Ake ? Ndi chiyani chomwe chingalepheretse chikhulupiriro choterechi ?

B. PANGANI ICHI KUKHALA MOYO WANU

“Koma tiyenera kulola Woumba mbiya kuchita ntchito Yake

Kotheratu ndikukhala wokondwa kukhala modekha m'manja MWake. "Ndi pemphero pemphani kuti ichi chikhale mbali ya moyo wanu...ndipo " KHALANI MOYO WOTERO !

Chifukwa pempho ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndikusintha kwanji komwe kudzachitike m'moyo wanga pamene Ambuye Adzayankha pemphero langa).

MABUKU OMWE AGWIRITSIDWA NTCHITO:

1. Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 53-55.
2. Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 54-55.
3. Mkangano Waukulu, (The Great Controversy), Tsamba 528.
4. Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 389.
5. Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire Of Ages), Tsamba 38.

10.

MPHAMVU ZOPANDA MALIRE

“Chidziwitso”

Yesu Anapemphera kuti, “...Koma moyo wosatha ndi uwu, kuti akadziwe Inu Mulungu Wona Yekha, ndi Yesu Khristu Amene Munamtuma.” Yohane 17:3. Yohane akuikiranso umboni motere, “Okonedwa, tikondane wina ndi mzake: Chifukwa kuti Chikondi Chichokera kwa Mulungu... Pakuti Mulungu Ndiye Chikondi.” 1 Yohane 4:7, 8. Mkhristu wina aliyense amene anabadwanso mwatsopano mwa Khristu, adafikira pozindikira kuti ngati afuna kuonetsera Khalidwe La Mulungu, Chikondi chikuyenera kuonetsedwa m’magawo onse a moyo wake. Chikondi chotere sindicho chongoyerekeza – ngati chongobvalidwa – Komano chikuyenera kuchokera mkati, ndipo gwero lake likuyenera kukhala mwa Khristu. Mkhristu sangakuze chikondi chotere; ndi mphatso yochokera kwa Mulungu yobwera kupyolera mu kumdziwa Iye.

“Chidziwitso Cha Mulungu, chobvumbulutsidwa mwa Khristu ndicho Chidziwitso chimene onse omwe ndi opulumutsidwa ayenera kukhala nacho. Ndi chidziwitso chomwe chimakonza khalidwe. Chidziwitso chotere tikachilandira, chimathandiza kukonzanso moyo kuti ufanane ndi chifaniziro cha Mulungu. Chidzabweretsa ku moyo wonse mphamvu ya Uzimu yochokera kwa Mulungu...”¹

Chidziwitso chotere chimakula molingana ndi malo amene chikhulupiriro chifanizidwa ndi chokometsera, komanso chomanga mbali zonse ziwiri kukhala pamodzi, pokumana ndi chochi-

tika chirichonse. Kodi mwatha kuona apa kuti ndi Chidziwitso cha kwa Mulungu, chobvumbulutsidwa mwa Khristu, chomwe tiyenera kukhala nacho ndipo ndicho chimene chidzaonetsera khalidwe la Umulungu mwa munthu ? Kapena nkutheka kuti ichi ndicho chifukwa chake ife tikulimbikitsidwa kukhala ndi ola limodzi tsiku lililonse, kuwerenga ndi kuganizira mwakuya za Moyo wa Khristu, kwenikweni magawo otsirizira a Moyo Wake ?

Zochitika zoterezi zidzationetsera ife kuti Yesu, monga munthu, adaphunzira za Mulungu kuchokera kwa amayi Ake, kenakono m'mene Amakula, adaphunzira kuchokera m'chilengedwe. M'mene Adayamba kuwerenga, Adaphunzira kuchokera m'malembo Oyera. Atate Wake Adamuunikira m'kuwerenga Kwake, ndikumubvumbulutsira ntchito Yake pa dziko lino lapansi. Chidziwitso chotere sichidam'chotse m'pang'onong'ono pomwe, kukhulupirika kwake pochita ntchito zake za pakhomu mokhulupirika. Iye Adali Odalirika mu ntchito Yake Nagwira ntchito pothandizira a pabanja Pake kufikira nthawi yomwe Adayamba utumiki Wake.

Tipeza kuti M'kudalira Kwake Pa Mulungu nthawi ndi nthawi, kudam'pangitsa Iye kukhala omvera nthawi zonse, kufikira, kumapeto kwake, m'munda wa Getsemane. Kumvera Kwake kudafikira pa chidzalo pamene Adapemphera, "Atate, Mukafuna inu, chotsani chikho ichi pa Ine; koma si kufuna Kwanga ai, koma Kwanu kuchitike." Luka 22:42.

"Tikuyenera kuphunzira moyo Wa Mpulumutsi wathu, popeza Iye ndiye chitsanzo changwiro cha anthu. Tikuyenera kulingalirapo pa nsembe yoposa ya pa Gologota, ndi kuona kuipitsitsa kwa tchimo, komanso chilungamo cha Lamulo. Poto mudzapeza mutu wa Nzeru ya chipulumutso ndipo potero mudzalimbikitsidwa. Kumvetsetsa kwanu kwa chikhalidwe cha Mulungu kudzalimbikitsidwa mwakuya; potero pomvetsetsa za nzeru yonse ya chipulumutso, yoikidwa pamtetete m'maganizo anu, mudzatha kukwaniritsa maitanidwe anu. Kupyolera m'kutsimikizika mtima kwa inu eni, mudzathano kuchitira umboni pakati pa anthu za kusasinthika kwa Lamulo La Mulungu, poonetsetsewa ndi imfa ya yesu pamtanda, komanso kuipitsitsa kwa tchimo ndi

Chilungamo cha Mulungu polungamitsa wokhulupirira mwa Yesu, polingalira za tsogolo lake lomvera Malamulo a Boma la Mulungu kumwamba ndi padziko lapansi.”²

Tikawerenga mwakuya zomwe zakambidwazi, tipezamo zinthu zinayi zomwe tiyenera kuziphunzira, zochokera pa Moyo wa Khristu: (1) Nsembe Yake Yamuyaya, (2) Kuipa kwa tchimo, (3) Kulungama kwa Lamulo La Mulungu, (4) Nzeru ya Chiombolo. Ngati ife titapanga chidziwitso choterechi kukhala gwero la maphunziro athu, ndiye kuti tilonjezedwanso mphoto zake zotsatiranso zinayi : (1) Tidzalimbikitsidwa ndi kuchitiridwa ulemu, (2) Chidziwitso chakuya cha Khalidwe La Mulungu chidzakhala chathu, (3) Nzeru ya Chipulumutso idzakhala yomveka bwino, (4) Tidzathano kukwaniritsa maitanidwe a ntchito yathu. Potero tidzakhala okhoza, potsimikizika ife eni, za mfundo zitatu zikuluzikulu za nzeru Ya Mulungu Ya chipulumutso: (1) Kusasinthika kwa Lamulo La Mulungu, (2) Kuipitsitsa kwa tchimo, (3) Njira Ya Mulungu Ya Chilungamo chochita ndi Chikhulupiriro. Mfundo zimenezi zimationetsera ife Chilungamo ndi Chifundo Cha Mulungu, chomwe Iye Amafunika kuti chionekere mwa wokhulupirira wina aliyense.

Mulungu Wapereka zotiyeneretsa zonse zomwe akadatha, ndi cholinga chofuna kutilimbikitsa ife kulowa mu njira iyi. Aroma 5: 1,2 akutsimikizira wokhulupirira aliyense zokhala mu mtendere ndi Mulungu, komanso mwayi wokhala nawo mu chikhaliidwe cha Mulungu (chopatsidwa kwa ife) mu nthawi ya kuyeretsedwa (Kuyenda ndi Yesu), kukhala mfulu posatsutsidwa, komanso ndi m’dalitso woposa – Mzimu Woyera, womuthandizira munthu wotereyu kuyenda ndi Yesu. Popeza Lamulo La Mzimu ndilo “Moyo mwa Khristu Yesu.”

Yesu Mwini Wake Adati, “Koma Nkhosweyo Mzimu woyera, amene Atate Adzamtuma m’Dzina Langa, Iyeyo Adzaphunzitsa inu zonse, Nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene Ndinanena kwa inu.” Yohane 14:26. Ndi ntchito ya Mzimu Woyera kutibvumbulutsira ife tanthauzo lakuti “Moyo Mwa Yesu Khristu.”

Chidziwitso Cha Mulungu, monga Chidabvumbulutsidwira ndi Yesu Khristu, ndi chomveketseka komanso chopezekeratu kwa munthu koposa chidziwitso china chirichonse. Chalembedwa pa duwa lina lililonse, Pa mtengo wina uliwonse, miyamba

ya nyenyezi zonse, m'kuwala kwa dzuwa, kuya kwa Nyanja, ndi pa cholengedwa china chirichonse chochokera m'manja a Mulungu. Chalembedwanso mu bukhu la Iye Mwini – Baibulo Loyera. Komanso Mulungu Watuma M'modzi mwa Utatu Wa Umulungu kukhala Mlangizi wathu. Kaya tikuwerenga kupyolera m'chilengedwe chake, kapena kuwerenga kuchokera m'mawu Ake Opatulika. Cholinga Chake chachikulu ndicho kutithandiza ife kuona tanthauzo lokhala ndi “Moyo mwa Kristu.”

Pamene inu mukuwerenga bukhuli, mwina mukhoza kukhala ndi maganizo akuti mukhoza kuchedwerapo pang'ono kupeza chidziwitso chotere. Maganizo oterowo ndiwo amene amakhala chipsinjo chachikulu chofikira chiyang'aniro chathu.

Timamva ngati kuti tiribe nthawi. Timamva ngati kuti sitingathe kumvetsetsa. Timamva ngati kuti ndife osalungama – kulakalaka ngati pakadakhala wina woti tidziwerenga naye limodzi. Mwinanso tikhoza kumva kuti ngati moyo wathu utasinthika, anzathu adzatiseka ndi kutijeda ndi kutitaya. Kamvetsedwe kotereka ndi kochokera kwa satana, popeza iyeyo amadziwa bwino lomwe mphamvu ya kamveredwe ka mthupi. Ndikukumbutseni kuti chikhulupiriro, kapena m'mene umvera m'thupi mwako, ndi zinthu ziwiri zosiyana, monganso kum'mawa kusiyanyirana ndi kumadzulo. Chotero, kaya inu mukumva bwanji m'thupi lanulo, yesetsani kufunafuna chidziwitso chochokera kumwamba ndikumatulidwa kuti mulawe nawo “Moyo Wa mwa Yesu Khristu” womwe ndi wa Chikondi chopanda malire – Mphamvu Yeniyeni Ya Mulungu.

Pamene tiyenda ndi Yesu, tikumbukire kuti Iye Satitsutsa ife ngakhale ife titalakwitsa. Iye ndi Kholo lathu la kumwamba Amene nthawi zonse Amakhala tcheru kutithandiza, pokonza zolakwika zathu kuzitembenuza kukhala miyala yoponderapo, osati miyala yophunthwitsa.

Satana ndiye wotitsutsa wathu wamkulu. Mawu A Mulungu Akuti, “Pakuti Mulungu Sanatuma Mwana Wake ku dziko lapansi kuti Akaweruze dziko lapansi, koma kuti dziko lapansi likapulumsidwe ndi Iye.” Yohane 3:17.

Kumudziwa Yesu kokha kwapangitsa Agwamula ambiri kukhala Akhristu achikondi ndi okondeka. Palibe nzeru ina pa dziko lapansi kapena kumwamba imene ingachite zoterezi. O ! tikuyenera nanga kum'dziwa Iye, Amene kum'dziwa Iye ndiko moyo wosatha.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwawerenga mu ndimeyi:

A.FUFUZANI

Kodi ndi zinthu zinayi ziti zomwe muyenera kuziphunzira zokhudzana ndi moyo wa Khristu ? nanga ndi zinthu zinayi ziti zomwe ziri zotsatira pa kuwerenga kotereku, nanga ndi mfundo zitatu ziti zomwe zimaonetsera chifundo ndi chilungamo cha khalidwe la Mulungu ?

Kodi ndi zopinga ziti zimene zingakulepheretseni kuona ntchito ya mzimu Woyera, Nkhosweyo, potero zitilepheretsa kufikira chiyang'aniro chatu ?

B.PANGANI ICHI KUKHALA MOYO WANU

Iye ndi Kholo Lathu Amene Ali “Wokonzeka kutithandiza ife, posintha zolakwitsa zathu kukhala miyala yoponderapo, m'malo mokhala miyala yophunthwitsa.” Funsani ndi pemphero kuti izi zikhale zoonadi m'moyo wanu ndipo ...
KHALANI MOYO WOTERO !!

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndi Kusintha kotani kudzaonekera m'moyo wanga pamene Ambuye Ayankha pemphero langa).

Mabuku Omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Moyo wanga Lero, (My Life Today), Tsamba 293.
2. Khristu Chilungamo Chatu, (Christ Our Righteousness), Tsamba 35.

11.

ZOYAMBA ZIKHALE ZOYAMBA

“Kudziletsa A”

Chidziwitso Cha Mulungu, Chopyolera m’kuona Khalidwe la Yesu Khristu, chimatitsogolera ife ku kuitanira Yesu Khristu kuti Aonetsere mwachibadwidwe khalidwe Lake mwa ife. Pamenepa Khristu, Yemwe mwa chikhulupiriro Wakhala Akusintha maganizo athu – kuti maganizo athu ayanjane ndi Ake – chomwechonso Iye Amasintha kakhaliidwe ka moyo wathu. Ntchito yotere ikuyenera kuyamba ndi chosowa chachikulu cha munthu.

“Kudziletsa kokha ndiko maziko a Zisomo zonse zochokera kwa Mulungu, maziko a zipambano zonse zomwe tingapambane.”¹

Pamenepa tikuyenera kumvetsetsa tanthauzo la mawu akuti kudziletsa.

“Kudziletsa koonadi mtima kumatiphunzitsa ife kulekana nazo kotheratu zonse zowononga moyo wathu, ndi kugwiritsa ntchito mwa maganizo abwino posankha izo zomwe ziri zathanzi. Alipo ochepa okha amene amazindikira monga ayenera kuzindikira, kuti ndizingati mwa zizolowezi zawo zimene ziri zokhudzana ndi thanzi lawo, khalidwe lawo, kufunikira kwawo m’dziko lino, komanso Tsogolo lawo lamuyaya. Madyedwe akuyenera kumvera nthawi zonse ku chitsogozo cha mphamvu ya maganizidwe abwino ndi nzeru zabwino. Thupi likuyenera kukhala kapolo wa maganizo athu, osati maganizo kukhala kapolo wa thupi lathu.”²

“Kusadziletsa ... kukutanthauza kuchita nazo zinthu zoononga moyo wathu za mtundu wa madyedwe kapena chilakolako.”³

Nkofunika kuti tidziwe m’ maganizo mwathu kuti nkondo ya pakati pa Khristu ndi satana, ndi nkondo yolimbirana kuti ndani amene atsogolere maganizo athu. Chingakhale chachidziwikire, kuti satana angachite chirichonse chomwe angathe, ndicholinga chongofuna kufooketsa kuthekera kwa maganizo a munthu. Iye amadziwa kuti ngati atafooketsa kaganizidwe ka munthu kuti kakhale kotsikirapo koposa pa mphamvu yake yoikidwa ndi Mulungu, pamene ndipo kuti satanayo wapeza chipambano choposa pa Mulungu. Ngati maganizo sangathe kumvetsetsa zinthu za UMulungu, zingatheke bwanji kuti munthu wotero adziwe choyenera kuchita ? Zotsatira zake ndizo zakuti, chifuniro cha munthu sichingagwiritsidwe ntchito mu njira yabwino. Satana amadziwa kuti ngati chifuniro chathu sichingagwiritsidwe bwino chotere, iye adzakhala ndi mwayi waukulu. Pobweretsa zikaiko, ziyang’ aniro za abwenzi ocheza nawo, ndi zina zotero, iye satanayo angakhoze kutipangitsa ife kusapanga chisankho. Iye amachita mosamalitsa kuti ife tisazindikire kuti kukanika kupanga chisankho zikutanthauza kupanga chisankho kumene. Zikutanthauza kugwiritsa ntchito ufulu wathu wa kasankhidwe, komano komukomera satanayo.

“Idyani chakudya chakumudzi, chokonzedwa mon-gofwafwaza, kuti nthambo za ku bongo zisakhale zofooka, kapena kugwidwa dzanzi, kapena kupuwala kumene, komwe kudzapangitse inu kulephera kuona zinthu zauzimu, ndi kuona chitetezero cha Yesu ndi Mphamvu yoyeretsa ya Yesu Khristu, monga ngati yachabechabe.”⁴

“Kusadziletsa kumayambira pa magome athu a zakudya, pamene tidya zakudya zosapatsa thanzi.”⁵ Poto kudziletsa kukuyenera kukhala gwero la bvutoli, kenakono limasefukira ku kakhaliidwe konse ka moyo wathu.

Njira yotsatira mfundo zisanu ndi zitatu, inatumizidwa ndi Mulungu kwa ife zaka makumi asanu ndi awiri apitawo, kuti

zithandizire kaganizidwe kathu ndi thanzi la thupi lathu kuti zigwire ntchito bwino mokwanira. “Mpweya wabwino, kuwala kwa dzuwa, kudzikana, mpumulo, majowajowa, zakudya zabwino, madzi, komanso kukhulupirira mu mphamvu ya Mulungu – awa ndiwo mankhwala eni eni.”⁶

Kuti timve zambiri za zomwe tatchulazi tikhoza kuwerenga Baibulo komanso zolemba zochuluka zolembedwa ndi Ellen White. Ngati ife titabvomereza kuti mabuku amenewa ndi obvomerezeka, tidzakhala nacho chotitsogolera cha komwe tingathe kupeza chidziwitso choterechi.

Kafukufuku wamakono watsimikiza kuti njira zathanzi zochokera kwa Mulungu zimenezi, ndi zolondola, komanso pa mfundo ina iriyonse yokhudza njira zimenezi, pali zolemba zochuluka zedi. Mulungu Wawaunikira abambo ndi amayi, amene adalemba ndi ulamuliro wonse, komano mu chiyankhulo chomveka bwino. Ife lero tiribe chowiringula.

Komabe, tiyeni tikhazikikeno pa ufooko waukulu wa munthu – chilakolako cha chakudya. Ngati chilakolako cha chakudya chitayamba kulamulidwa ndi Khristu, ife tidzatha kukhala ogonjetsa pa tchimo lina lirilonse lowononga.

“Mphamvu yolamulira ya chilakolako cha chakudya idzaonongetsa anthu miyandamiyanda, omwe, ngati akadakhala ogonjetsa pa chilakolakochi, akadathanso kukhala nayo mphamvu yogonjetsa mayesero ena aliwone a satana.”⁷

Mtanthauziri mawu wotchedwa Webster anatanthauzira liwu limeneli lakuti kudziletsa, monga, “Chizolowezi chochita nacho pang’ono pang’ono chilakolako cha madyedwe ndi chakuthupi.” Webster akutanthauzira liwu lakuti chilakolako monga ngati “Chibaba cha mgonagona.” Ndi pokhapokha ife tingaone kulumikizana kotereku kwa chilakolako cha zakudya, pamene tidzathe kumvetsetsa tanthauzo lotere.

Hava adayesedwa mayeso kupyolera mu chilakolako cha zakudya. Chilakolako chenichenicho chidabisika mu funso lake. N’chifukwa chiyani Mulungu Adawaletsa kudya chipatso cha mtengowo? Lidali funso lobisika lotere, loonetsedwa mu chikhalidwe chake ndi maonekedwe ake, zimene zinampangitsa

satana kutengerapo mwayi. “Eya, kodi Adati Mulungu musadye za mtengo wa m’mundamu?” Hava adatengeka pamene adamva chinjokacho chikuyankhula maganizo ake a Havayo. Nanga ndi angati lero amene ali nacho chilakolako chofuna kudziwa kuti “N’chifukwa chiyani” pa njira za Mulungu. “Zinsinsi N’zake za Yehova Mulungu: Koma zobvumbulutsidwa n’zathu ndi ana athu ku mibadwo mibadwo..” Deuteronomo 29:29. Kodi tidzayamba liti kukhala okwanitsidwa kukhulupirira zomwe Mulungu Wane-na, ndikusiya kufunsa “Chifukwa” pokhapokha Mwini Wake Atatibvumbulutsira?

Chilakolako cha Hava chidaonetseredwanso mu njira zina. Chinjokacho chidapitirizabe kuyankhula ndi mawu a chikoka, ot-amanda maonekedwe ake okongola, zomwe zidasangalatsa Hava.

Pamene chilakolako chinadyetseredwa pan’gono chotere, linali khwerero limodzi lokha lomupanga Hava kukayikira m’ma-ganizo ake popeza adazolowera liwu limene lidabvumbulutsa “zokoma” zotere. Iye adayankhano funso lochenjera la chinjok-acho,... “Zipatso za mitengo ya m’mundamu tidye; koma zipatso za mtengo umene uli mkati mwa munda Mulungu adati musadye umenewo, musakhudze umenewo mungadzafe.” Genesis 3:2,3. Yankho la chinjokacho linali lachangu ndi lotsimikiza, “...kufa simudzafai.” Genesis 3:4. Kusemphanitsa kwa Mawu A Mulun-gu kumeneku kudatsimikizika ndi chikaiko, “chifukwa Adziwa Mulungu kuti tsiku limene mukadya umenewo adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhala ngati Mulungu, wakudziwa zabwino ndi zoipa.” Genesis 3:5.

“Iye [satana] akuyesetsa nthawi zonse kubweretsa kamzimu kosafunikira kofuna kuonetsetsa, komanso chikhumbokhumbo chofuna kufukula mwakuya zinsinsi za Nzeru ndi Mphamvu Ya Mulungu. Mu kufunafuna kwao kuti apeze icho chimene Mulungu Chamukomera kuwabisira, anthu miyandamiyanda satha kuona choona-di chimene Iye Wachibvumbulutsa, chimene chiri cho-funikira ku chipulumutso cha munthu.”⁸

Chikaiko chinapezano m’maganizo a Hava, mbuto yokha-lamo. Komano satana ayenera kulimbikitsa chikaiko choterechi ndi m’mene munthu amvera m’thupi mwake. Tangoyang’anani makwerero amene satana afuna ife anthu tikwerepo.

Iyeno adatengerapo mwayi pa zolankhula za Hava, ndipo adatenga chipatsocho nachiiika m’manja mwa Hava. (Onani m’mene mamvekedwe amaonongera chidziwitso.) chinjokacho chidamkumbutsa Hava mawu ake omwe, “Musakhudze uwu kuti mungafe.” Satana adati: “Si icho nanga chiri m’manja mwa-ko, ndipo sunafe. Sungafe angakhale utadya.” Hava sadaonepo choopsa chirichonse, potero adatsimikizika kudya. Maganizo ake adakumbukira mawu a satana akuti chipatsocho chidzampatsa nzeru, potero iye adadya. Zotsatira zakeno ndizo kamvedwe kake. (Tisaiwale kuti mamvekedwe a m’thupi ndiwo njira zimene satana amagwiritsira ntchito.) Hava sadaonepo kena kalikonse kosonyeza kusakondwa kwa Mulungu. Iyeyo adangoona kutsekemera komwe kudalowerera mthupi monse. Iye adaganiza kui umu ndi m’mene anthu okhala kumwamba amamvera m’thupi mwawo.

Kodi inunso mudayamba mwamvapo kutsekemera kwa tchimo koyenderera m’thupi monse mutangomaliza kuchita tchimo? Kumbukirani kuti mphamvu ya satana idakalipobe.

Hava, atadzazidwa ndi mamveredwe a m’thupi mwake, adakhalano chida chomwe Adamu adagwera. Kupyolera m’mamveredwe, satana adakapitirizabe kuononga ndi kuphwasula chidziwitso cha Mulungu chopatsidwa kwa anthu. “Chifukwa chake mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena, chitani zonse ku Ulemerero wa Mulungu.” 1 Akorinto 10:31.

Kudziletsa kudzatsatana ndi chidziwitso m’moyo wathu ngati tiri ololera kuthana nalo bvuto la chilakolako cha chakudya. Mw ife tokha sitingathe, komano tiri naye Wina pambali pathu Amene Ali Wamphamvu yopulumutsa. Pamene tikomana ndi kulephera kwathu, pomwepo tisankha mwa chifuniro chathu kugwiritsa Malembowa, ngakhale titalephera kwa nthawi zochulukana, Mulungu Adzagonjetsa zilakolako zathu. Chipambano chidzakhathu. Pomwepo tidzaika “zoyamba kukhala zoyamba.”

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwaphunzira mu ndimeyi:

A. FUFUZANI

Kodi ndi nkhondo yanji yomwe ikukhudzana ndi “Kudziletsa” ?

Bwerezani magawo a machenjero amene mdierekezi amagwiritsa ntchito kutipusitsa ife.

B. PANGANI KUKHALA MOYO WANU !!

“Ngati titapezana ndi kulephera kwathu, ndipo mwa ku-sankha kwathu tigwiritsa ntchito malembowa, ngakhale titalephera kwa nthawi zochuluka, Mulungu Adzatigonjetsera zilakolako zathu. Chipambano chidzakhala chathu.”

Funsani ndi pemphero kuti izi zikhale zenizeni m’oyo wanu... ndipo **KHALANI MOYO WOTERO !!**

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndikusintha kwanji komwe kudzachitika m’oyo mwanga pamene Ambuye Ayankha pemphero langa).

Mabuku Omwe Agwiritsidwa Ntchito:

1. Kudziletsa, (Temperance), Tsamba 201.
2. Kudziletsa, (Temperance), Tsamba 138. (Owonjezedwa)
3. Kudziletsa, (Temperance), Tsamba 137.
4. Maumboni, (Testimonies, Bukhu 2, Tsamba 46. Weren-ganinso Bukhu la Malangizo a Madyedwe ndi Zakudya, (Counsels on Diet and Foods), Tsamba 55, ndi Maumboni, (Testimonies), Bukhu 6, Tsamba 327.
5. Maumboni, (Testimonies), Bukhu 3, Tsamba 487.
6. Utumiki wa machiritso, (Ministry of Healing), Tsamba 127.
7. Kudziletsa, (Temperance), Tsamba 16.
8. Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 54,55.

12.

Chipiriro

– NTCHITO YANGWIRO YA MULUNGU

Pamene tafikapa, m’kukwera kwathu kwa Makwerero - Chiyeretso – n’kofunika kukumbukira kuti iyi ndi ntchito ya chikhulupiriro. Ndi pokhapokha pamene ife tichita mbali yathu – kuzindikira zopangitsa kupinga ndi kulepheretsa, ndikuzindikira kuti sitingathe kuzichotsa mwa ife tokha – pokhapo ndi pamene ife tidzathe kugwiritsa ntchito mphamvu ya chisankho chathu ndi kukhala omasuka ku zotsamwitsa zoterezi. Ngati titafikira poteropo, ndipo pamene Mulungu Adzachita Ntchito Yake Mwa ife. Iye sadzaumiriza chifuniro chathu, koma Adzadikira ulamuliro wathu wobvomereza kuti Iye Atichotsere zoterezi. Tapeza kuti ngati ntchitoyi ingachitike, ndiye kuti ndi Mulungu Yekha amene Angaichite. Kumbukirani kuti pa ife tokha “tiribe nzeru ngakhale mphamvu zogonjetsera” uchimo. ¹ Izi tizidziwe m’maganzizo mwathu pamene tikukwera khwerero lina lililonse.

Petro akunena kuti, “...ndi pa chodziletsa chipiriro...” 2 Petro 1:6. “Chipatso cha mtengo wapatali cha chiyeretso ndicho chisomo cha kudzichepetsa.”² Tikayang’ana mwakuya mu Mtanthauzira mawu wa Webster’s Collegiate, tipezamo ubale weniweni wa pakati pa kudziletsa ndi chifatso.

Mopanda chikayiko, Mulungu Adakuza khalidwe la chifatsoli mwa Mose kwathunthu kuposa munthu wina aliynse. Ngakhale izi zinali chomwecho, mwa Moseyo, kulakwitsa kumodzi kokha, ngakhale kuti iye anakhululukidwa, kunalepheretsa Mulungu kukwaniritsa ziyang’aniro Zake pa moyo wa Mose pa dziko lino. Apatu tikutha kuona kulukana kwangwiro pakati pa Chilungamo ndi Chifundo cha Mulungu. “Kudziyeretsa kwenikweni... kutanthauza kufa tsiku ndi tsiku ku undekha ndi kufanizidwa tsiku ndi tsiku ku chifuniro Cha Mulungu .”³

Magwero a chiyero akhazikika pa muzu wa bvuto la khwero limeneli la Chipiriro, popeza chipsinjo chachikulu ndicho kunyada. Tikudziwa za kujijirika kwa Petro – munthu wongolankhula ndi kuchita asanaganizire.

“Tchimo lomwe linapangitsa Petro kugwa ndiponso limene linawatsekereza Afarisi kulumikizana ndi Mulungu, likupangitsa anthu miyandamiyanda kuonongeka lero. Palibe chinthu china chomunyansa Mulungu ngakhalenso choopsesetsa kwa munthu, choposa kunyada ndi kudzialira wekha. Mwa machimo onse, kunyada ndiko kopanda chiyembekezo ndi kosachiritsika.”⁴

Kunyada ndi kudzialira kumachititsa maganizo a munthu kukhala osiyaniranatu ndi mtima wodzichepetsa ndi wodzipereka. Ichi ndicho chifukwa chake pamene tiyesa kudzilamulira tokha, natilephera, timadzayesetsanso koposera muyeso ngati titapeza mwayi wina. Kuyesetsa konse kwa umunthu kuti akhale ndi chipiriro sikungathe kubweretsa chipatso cha chipiriro. Mwina chikoka chokha chikhoza kubweretsa chidwi cha chipiriro – anthu amalonda amagwiritsa njira yomweyi yokopa chidwi cha anthu. Ogula akhoza kupusitsidwa ndi chikoka choterechi, pakuti zomwe anthu amaona kumsewu sindizo zomwe munthu aliri akakhala kwawo.

Bvuto lathu likuoneka kuti kunyada kumakhala potsogolera pa izo zomwe ziri zofunikira. Kunyada kukhoza kubvala maonekedwe ofatsa, ophunzitsika, odekha ngakhalenso a chipiriro.

“Ena a ife tiri ndi mitima yothamanga ndipo mwachibadwa timachita zinthu mwa phuma; komano tidziwe kuti palibe munthu amene sangathe kuphunzira kukhala wodekha ndi wopirira. Chipiriro ndi mbewu yomwe imakula mwachangu ngati itasamalidwa bwino.”⁵

Kupalira ndiko njira imene imachotsa zonse zotsamwitsa makulidwe ofunika a mbewu. Bvuto kwa ambiri a ife sindilo kutengulira. Bvuto ndi kulephera kubvomereza kuchotsa zomwe ziyenera kuchotsedwa mu khalidwe lathu, ndi kulolera kupita nazo kwa Mulungu kuti Atichotsere. Ngati chipiriro chingakule

mwa ife mwachangu, pakufunikira kudziunikira tokha ndi kulolera mfundo zeni zenizo. “Padali pamalo pamene Petro anadziyesa yekha kuti ali wamphamvu, pamene Petroyo anasonyeza ufooko wake; ndipo ndipokhapokha iyeyo anazindikira kufooka kwake kumene Petroyo anazindikira kufunika kwa Yesu”.⁶

Chipiriro chikhoza kubvala chobvala china chomwe tichiyang’ane.

“Alipo ambiri amene podzudzulidwa amachiona ngati cha mtengo wapatali pamene alandira chidzudzulocho popanda kukwiyapo; komano ndi ochepa otani nanga amene amatenga chidzudzulo ali ndi chimwemwe mu mtima, nawadalitsa iwo amene awapulumsa kuchoka ku phompho.”⁷

Chachidziwikire kuti chipiriro chimafikira madera amene sitiwaganizira. Chimafunika kubweza moto, osafuna kubwezera choipa. Chipiriro chimafunikira kumuona wina aliyense monga aliri ndi zonse monganso ziriri.

Werengani Ahebri 11, ndikuonapo mboni zochuluka kuyambira pa Abele kufikira kwa Samueli, ndikufikira khamu lalikulu la amuna ndi kazi amene, kupyolera mwa Khristu, anagonjetsa satana ndi khamu lake la angelo akugwa. Ndiyeno muonenso chithunzi cha inu eni mu ndime 12 pamene Paulo akuti, ... “Titaye cholemetsa chirichonse, ndi tchimoli limangotizinga...” – Kutanthauza chotitchinga. Tichotse udzu onse otsamwitsa ndipo tikumbe kukonzetsera nthaka yolimba. Paulo akupitiriza ndikuti, “...ndi tchimo limangotizinga...” Ahebri 12:1. Apa tiri ndi zizolowezi zathu zakale zomwe satana amazigwiritsa ntchito nthawi ndi nthawi.

“Undekha ndi kunyada zidzatipangitsa ife kupanga chisankho choona kuti ziwirizi ziri zoipa. Sitingathe ife mwa ife tokha kugonjetsa zilakolako ndi zizolowezi zomwe zimafuna kulumulira moyowu. Ifeyo sitingathe kugonjetsa m’dani wamkuluyo amene watigwira ife mu ukapolo.” Mulungu Yekha Ndiye Amene Angathe kutipatsa ife chigonjetso... Koma Sangagwire ntchito mwa ife popanda chilolezo chathu.”⁸

Titatha kuchita zonsezi, pomwepo tikhoza kulankhula pa-

modzi ndi Paulo, "...ndipo tithamange mwachipiriro makaniwo adatiikirira ndi kupenyenera Woyamba ndi Womaliza wa chikhulupiriro chathu, Yesu..." Ahebri 12:1, 2.

Yakobo anali m'modzi wa ana a 'bingu'. Iye, pamodzi ndi m'bale wake Yohane, akadatha kuitana moto kuti utsike kuchokera kumwamba kunyeketsa iwo amene sadamlandire Yesu Khristu ndi akuphunzira Ake polowa mu Mzinda. Yesu adasintha zonsezi ndikumuphunzitsa Yakobo kufunikira kwa ntchito ime-neyi ya chipiriro, kotero kuti Yakobo anathano kulemba motere: "...Koma chipiriro chikhale nayo ntchito yake yangwiro, kuti mukakhale angwiro ndi opanda cirema, osasowa kanthu konse." Yakobo 1:4.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwaphunzira mu ndimeyi:

A. FUFUZANI

Kodi ndi mfundo ziwiri ziti zomwe zimalepheretsa chipiriro? Tingachite nawo bwanji mtsutso wa anthu pogwiritsa chipiriro?

B. PANGANI ICHI KUKHALA MOYO WANU !!

"Koma chipiriro chikhale nayo ntchito yake yangwiro, kuti mukakhale angwiro ndi opanda chirema, osasowa kanthu konse," (Yakobo 1:4) Funsani ndi pemphero kuti ichi chikhale moyo wanu ndipo.... KHALANI MOYO WOTERE !!

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Kusintha kotani komwe kudzachitika m'moyo mwanga pamene Ambuye Ayankha pemphero langa.)

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Machitachita a Atumwi, (The Acts of the Apostles), Tsamba 532.
2. Moyo Wanga Lero, (My Life Today), Tsamba 253.
3. Moyo Wanga Lero, (My Life Today), Tsamba 248.
4. Mafanizo A Yesu, (Christ Object Lessons), Tsamba 154.
5. Moyo Wanga Lero, (My Life Today), Tsamba 97.
6. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire Of Ages), TSamba 382.
7. Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 667.
8. Thoughts From The Mount Of Blessings, Tsamba 142.

13.

Palibe **MOAL OIMA**

Phunziro lakuti “kutchuka kwenikweni kumatengera ubwino woonadi”¹ lakhala nthawi zonse lobvuta kuliphunzira. Ngakhale Nebukadinezara, mfumu yaikulu yonyada ya kalelo adaphunzira phunziroli mu njira yobvuta. N’zachibadwa, kuti pamene tikuyesetsa kuchita zolungama, timamva ngati kuti tafikirapo pa umulungu kupyolera mkuchita zinthu zabwino.

“Chifukwa chimene anthu ambiri mu mbadwo uno wa dziko sakukula moonjezera m’oyo wawo wa uzimu, ndi chifukwa chakuti amatanthauzira Chifuniro cha Mulungu kuti ndicho chomwe iwo ayenera kuchita. Pot-satira zifuniro za iwo eni, iwo amadinamiza okha kuti akufanizidwa ndi Chifuniro Cha Mulungu. Oterewa alibe nkhondo yolimbana ndi undekha. Aliponso ena omwe mwakanthawi kochepe amaoneka ngati akupambana mu nkhondo yawo yolimbana ndi zilakolako zawo ndi moyo wawo wa mtambasale. Oterewa nkutheka kuti sakudziwapo kanthu kenakalikonse, komano amatopa mkuyesetsa kwawo, pofa tsiku ndi tsiku, mwa ntchito yawo yosalekeza. Ulesi umawayandikira, komanso amadana ndi kufa ku undekha; potero amatseka maso awo olemera ndi tulo, ndikugwa ku mphamvu ya mayesero m’ malo mokana mayeserowo.”²

Pali magulu awiri amene anenedwa mu ndime imene yangothayi. Gulu loyamba ndilo lomwe tingalitchule kuti Okhulupirira mololera. Gulu limeneli liribe bvuto ndi nkhani ya kufa ku un-

dekha. Ku gulu limeneli kumaoneka kophweka kufufuta chiyero, kuchichotsa ku mphatso ya Mulungu ya chilungamo chochita ndi chikhulupiriro, kulekana ndi kutsatira kuitana kwa Mlengi kwa-kuti, "...Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, natenge mtanda wake, nanditsate Ine." Mateyu 16:24.

Gulu lachiwiri ndilo gulu la okhulupirira okanika amene amakhala otopa chifukwa mizu yawo ndiyosazikika mwa Khristu. Iwo sanaphunzire chimwemwe chokana undekha ndi kulolera Khristu kunyamula katundu wawo. Iwo sanadziwebe kuti Goli Lake liri lofewa ndi katundu Wake wo pepuka.

Chiyeretso, monga ntchito ya tsiku ndi tsiku, chimafikira pansi ndi pansi mwakuya m'moyo wathu, ndipo chifunika kudzipereka kwathunthu nthawi zonse. Izi zimakhala zobvuta kuchita kwa mtima umene uli onyada kuti ungapeze chimwewe chotere.³

"Yohane ndi Yudasi akuimirira iwo amene ali otsatira a Yesu... aliyense anali nako kufooka ndi kulephera mu khalidwe lake, komanso yense mwa iwo anali nawo mwayi wofikira Chisomo Cha Mulungu Chosintha khalidwe la munthu...M'modzi mwa awiriwa, posankha kufa ku undekha tsiku ndi tsiku ndi kugonjetsa tchimo, anayeretsedwa mwa choonadi; winayo, pokana mphamvu yachisomo cha kusintha, ndi kukhazikika pa zilakolako za umbombo, adakodwa mu msampha wa satana."⁴

Popeza moyo womwe tikhalawu ndi wofunika kupanga zisankho tsiku ndi tsiku, chomwecho zikutanthauza kuti lime-neli ndilo dera lomwe kufa ku undekha kuyenera kuyambira. Monga Yesu, Yemwe Ali Chitsanzo chathu, chisankho chathu mopanda kukakamizidwa chikuyenera kukhala chakuti, "Osati kufuna kwanga koma kufuna kwana kuchitidwe." Pemphero lotereli lisangokhala longolankhula kokha, koma lochita. Likufunikira kulolera – monga Mulungu Atsogolera – kusintha, kuleka, kapenanso kuchita ntchito ina iliyonse kapena chifuniro china chirichonse ngakhale chikhale chokondedwa motani. Chikufunikira kuzolowerana ndi chifuniro cha Mulungu chobvumbulutsidwa ndi Umulungu; komanso tiyenera kumvetsera ku liwu la kayaziyazi la chikumbumtima chathu pamenenso tikuona

chitsogozo Chake. ⁵

Potsatira njir izi, Chisomo Cha Mulungu “Chidzakopa maganizo athu kuganizira za kumwamba ndi kupanga chizolowezi choganizira nthawi zonse za zinthu zachiyero.”⁶ Kufanana ndi Umulungu sizitanthauza kuchita zomwe Yesu Anachita, koma zitanthauza kukhala moyo monga Yesu Anakhalira. Tikuyenera kumvetsetsa malangizo a Paulo a kakhaliwe ka m’chiyero monga kwalembedwa mu Akolose 3:3,4. “Pakuti munafa, ndipo moyo wanu wabisika pamodzi ndi Khristu mwa Mulungu. Pamene Khristu Adzaoneka, ndiye moyo wathu, pamenepo inunso mudzawonekera pamodzi ndi iye mu ulemerero.” Kodi ndi ulemerero wanji womwe Paulo akunena apawu? “Kwa iwo amene Mulungu anafuna kuwazindikiritsa ichi chimene chiri chuma cha ulemerero wa chinsinsi pakati pa amitundu, ndiye Khristu mwa inu chiyembekezo cha ulemerero.” Akolose 1:27.

Mwayi waukulu wotere nanga kuti ife tingathe kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu m’kuonetsera Khalidwe lake ku dziko losakhulupirali. “Palibe makhalidwe kapena mphamvu zimene zinaonetsedwa ndi Yesu zimene anthu sangathe kukhala nazo mwa chikhulupiriro mwa Iye. Umunthu Wake Wangwiro ndiwo umene otsatira Ake onse akuyenera kukhala nawo, ngati iwo angafune kugonjera kwa Mulungu monga Iye Adachitira.”⁷

Uwu ndiwo Umulungu weniweni, osati kuyesetsa kukhala wabwino kapena kuchita zinthu zabwino, koma kufa ku undekha tsiku ndi tsiku – kukhulupirira mwa Mulungu moona mtima. “Mwananga, undipatse mtima wako, Maso ako akondwere ndi njira Zanga.” Miyambo 23:26. Tidzazizwa pa zimene Mulungu Adzachita m’moyo wathu ngati ife titasiya kuyesetsa, m’ malo mwake ndikuyambano kufa ku undekha – kuyamba kumvera Mulungu monga Yesu Anachitira.

Pali chochinga chimodzi chomwe tiyenera kukomana nacho pamene tikuyamba khwerero lotereli – chochinga chimenechi ndicho kufewerera. Iyi ndi njira imodzi yomwe satana amaigwiritsa ntchito kumulepheretsa Mkristu kupanga chipambano cha uzimu chimene Mulungu amafuna mwa munthuyo. Moyo wa Yesu Khristu pa dziko lino lapansi sunaonetse kufewerera kwa mtundu wina uliwonse pa nthawi ina iriyonse. Iye nthawi zonse Anali Odzipereka kuchita Cifuniro Cha Atate Wake. Mawu Ake Adati, “Kuchita chikondwero Chanu kundikonda, Mulungu

Wanga...” Masalmo 40:8 akutionetsera ife khalidwe lenileni lofanana ndi lobvomerezeka pamaso pa Mulungu. Kumvera konyinyirika sindiko kumvera ayi.

“Pamene ziyang’aniro za Mulungu zimaoneka ngati zotsamwitsa chifukwa zikulimbana ndi zifuniro zathu, pamenepo ndiye kuti tidziwe kuti moyo woterowo sindiwo moyo wa Mkhristu. Kumvera kwenikweni ndi ntchito yoyambira mkati mwa munthu. Kumachokera ku magwero a chikondi cha chilungamo, chomwe ndi chikondi cha Lamulo la Mulungu. Chofunikira cha chilungamo chonse ndicho kumvera Mpulumutsi wathu.”⁸

Ophunzira a kalewo, Makolo athu a nthawi ya kukonzanso, ngakhale anthu a Mulungu ku mibadwo yonse akhala akukomana ndi yesero limeneli la kwa satana mdierekezi lowayesa iwo kufewerera pa chikhulupiriro chawo mwa Mulungu. Ndikupyolera mu izo zimene ife timazona ngati mphamvu zathu, zimene satana amapezapo ufooko wathu. Tiyeni tiyang’anenso mbali ina ya Mtumwi Petro.

“Inali nthawi imene iye Petro anadziyesa yekha kuti ali wamphamvu pamene iye anaonetsa ufooko wake; Ndi pokhapokha pamene iyeyo anazindikira kufooka kwake pameneno adaona kufunika kodalira pa Khristu. Iye akadaphunziriratu phunziro limene Yesu Adafuna kumuphunzitsiratu nthawi ija ya panyanja, iye sakadalephera pamene yesero lalikuku lidamufikira.”⁹

Tsopano tikhoza kumvetsetsa bwino mawu a Khristu kwa Paulo mu 2 Akorinto 12:9, “...Chisomo Changa Chikukwanira; pakuti mphamvu Yanga ithedwa mu ufooko...” Chomwecho, pamene Paulo akupereka yankho mu vesi lotsatiralo, “Pakuti pamene ndifooka, pamenepo ndiri wamphamvu.” Ayi, palibe malo oyima apa. Thabwa la khwerero ili langotitsegula maso kuona ngalande za kutsogolo, pamene Yesu Wokhala mwa ife Akhala Mfungulo yotithandiza ife kufanana ndi Mulungu.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwawerenga mu ndimeyi:

A. FUFUZANI

Apa, takamba za magulu awiri a anthu, kodi nkutheka kuti mwadziona nokha kukhala mu gulu limodzi mwa maguluwa?

Lekani kuyesetsa kapena kukhala wabwino. Tiyenera tsiku ndi tsiku tife ku undekha. Komabe ngakhale nkutero, pali cholepheretsa: Ndi chiti?

B. PANGANI KUKHALA KHALIDWE LANU !!

“Tikutha kuona kuti njira yokhayo ya ku Umulungu ndiyo kufa ku undekha. Ayi, palibe malo oyima apa.” Funsani ndi pemphero kuti izi zikhale moyo wanu. ... Ndipo KHALANI MOYO WOTERO !!

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndi kusintha kotani komwe kudzachitika m'moyo wanga pamene Ambuye ayankha pemphero langa).

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Aneneri ndi Mafumu, (Prophets and Kings), Tsamba 521.
2. Machitachita a Atumwi, (The acts of The Apostles), Tsamba 565.
3. Khristu Chilungamo Chathu, (Christ our Righteousness), Tsamba 33,34.
4. Machitachita a Atumwi, (The Act of The Apostles), Tsamba 558,559.
5. Mauthenga kwa achinyamata, (Messages to Young People), Tsamba 156.
6. Maumboni, (Testimonies), Bukhu 2, Tsamba 478,479.
7. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 664.
8. Mafanizo A Yesu, (Christ's Object Lessons), Tsamba 97.
9. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 382 Loonjezera

14.

Chiyanani, **PALIBENSO MPIKISANO?**

Kodi zinayamba zakuonekerani ngati zachilendo kuti mu chil-inganizo cha Mulungu tikuyenera kuzindikira kuti mkupyolera mu Umulungu okha tikhoza kukhala nacho chikondano cha pa abale? Ngati titalandira mfundo imeneyi yochokera m’Baibulo, ndiye kuti tayang’anizana nalo maso ndi maso bvuto. Kodi m’bale wanga ndi ndani? Yesu akuyankha funso limeneli mu Luka 8:21, “...Koma Iye anayankha, nati kwa iwo, Amai wanga ndi abale anga ndiwo amene akumva mau a Mulungu, nawachita.” Ndi zachidziwikire apa, kuti Yesu sanaikire malire a ubale kwa iwo okha amene amvera kwathunthu Mawu ke, komano anatambasulira kwa iwonso amene amalakalaka kumchera. Mateyu 12:49 akutiuzwa kuti pamene Ankalankhula mawu amenewa ankaloza ndi chala Akuphunzira Ake, amene anali kutali pochita Mawu Ake. Bvuto lalikulu pakati pa wina aliyense wa iwo linali mpikisano.

Mzimu umene umalimbikitsa maganizo a mpikisano ndi mzimu woweruza. Mzimu wa mpikisano ndi mzimu woweruza, zonse ndi zochokera kwa satana ndipo zimangokwaniritsa chifuniro chake. Nangano tingatani kuti tikhale omasuka ku zipsinjo zoterezi? Yesu akutipatsa ife yankho lake. Moyo Wake Unali chionetsero changwiwo cha umo m’mene ife tingathe kukhalira m’chiyanjano pamodzi ndi abale ndi alongo athu. Pa mutu wachitatu tidaona zolemba zochokera m’bukhu la “Thoughts from the Mount of Blessing, pa tsamba 71. Tingobwerezanso zomwe tinalamba, chifukwa zitipatsa ife yankho la m’mene moyo wa yesu Udadzaziridwa ndi chikondi chimenechi cha pa abale, ngakhale kufikira kwa iwo amene anamnyoza Iye. ¹

“Ulemerero Wa Atate Unam’zinga Khristu, ndipo palibe chinthu china chirichonse chomwe chinam’gwera Iye, choposa icho chimene Chikondi cha Mulungu Chinabvomereza, kuti dziko lidalitsike nacho. Apa ndipo pamene panagona chithonhozo Chake, ndipo chikhozanso kukhala chathu. Iye amene adzazidwa ndi Mzimu Wa khristu akhala mwa Khristu. Chipsinjo chotumizidwa kwa iye chimayamba chagwera kaye pa Mpulumutsi, amene amakhala atamzinga kale ndi Ulemerero Wake. Chirichonse chobwera kwa iye chimachokera kwa Khristu. Iye salimbana yekha kugonjetsa choipa, popeza Khritu ndiye Mtetezi wake. Palibe china chirichonse chimene chingamkhudze iye pokhapokha chitaloledwa ndi Ambuye, ndipo, “Tidziwa kuti amene akonda Mulungu, zinthu zonse zithandizana kuwachitira ubwino. Aroma 8:28.”²

Pamene Yesu Ankalandira zonse zochitika kwa Iye m’moyo Wake monga ngati zochokera m’dzanja La Atate Wake, ngakhale zinazo zinali zochokera kwa satana, Iye Adali ndi mtendere weniweni. Iye Adali Okhoza kulandira chitonzo choipitsitsa chomwe chikadatha kugwera munthu wina aliyense, m’maganzizo ngakhale ku thupi, komabe anali odekha mtima kwa munthu amene chipsinjocho chabwera ndi iye. Kudali kuchibvomera kotereku, kumene Yesu anatha kukhululukira onse omuchitira zoipa. Iye Ankatha kuona ndi diso lopyola la umunthu, naona satana monga mdani weniweni wogwiritsa nthito anthuwo. Izi zidampangitsa Iye kumvetsetsa ngakhale kwa omuzunza, nawachitirabe chifundo. Iye Adawachitira chifundo m’malo modzimvera chifundo Yekha. Nthawi zonse Anali kuwakhulukira otsatira ake chifukwa cha kusadziwa kwao. Ankadziwa kuti satana ankawachititsa khungu.

Ife tikuuzidwa kuti gwero la chithonhozo Chake likhozanso kukhala gwero lathu. Kodi mukutha kuona zomwe zikadakhocha kuchitika m’banja la Mulungu ngati abale ake a Yesu akadamakhalira ndi mfundo izo zomwe Iye amagwiritsa nthito adakali pa dziko lino lapansi? Chikondi cha pa abale sichingatifikire ife koposera apa. Ifetu sitingaziumirize tokha kukhala achifundo ndi achikondi. Iyi ndi nkhani yochokera mkati – mu mtima. Njira

ya Yesu ndi njira yokhayo imene mtima wathu ungabvomere mosayang'ana mbali, chifukwa ndi pokhapo pamene maso athu sadzayang'ana kwa anthu ngakhale ku nkhaza zawo.

Mayeso enieni akupezeka mu “Zinthu zonse”, munga mwa Aroma 8:28. Ife tiri okonzeka kugwiritsa ntchito njira ya Yesu m'moyo wathu ku zinthu zina, komano kodi ndi mu zinthu zonse? Eya, palibe kusiyantsa. Iye ndiye Mbuye Wa zonse kapena ayi.

Mulungu Ali osamalitsa kutiteteza ife, kotero kuti Iye Adzatha kutembenuza choipa chirichonse chochokera kwa satana chobwera kwa ife, kuchipanga kukhala dalitso, ngati ife titabvomera “Zinthu zonse” kukhala phunziro lotitsogolera m'moyo wathu.

“Mayesero a moyo uno ndiwo antchito Ake a Mulungu otithandiza kuchotsa zinyansi ndi zokhuthala za mu khalidwe lathu loipali. Kutema kwao, kupinda kwao ndi kugoba kwao, kuwaula kwao, komanso kuwalitsa kwao kumakhala njira yowawa; ndichinthu chowawa kuikidwa pansu pa mphero. Komano mwanamphero anaikidwira kutithandiza ife kukhazikika pa malo athu kumwamba. Mlengi Wathu Sangataye nthawi yake kusula chinthu chopanda mtengo pamaso pake. Ndi miyala yokhayo ya mtengo wapatali pamaso Pake imene Iye Amaisula mofanana ndi okhala a m'nyumba Yake ya Chifumu.”³

Nachi chifukwa china chokwanira kuti tikhulupirire, tibvomereze ndi kuchita nawo Malembo m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Ngati mawu awa akuti “Mu zinthu zonse” akutanthauza zabwino ndi zoipa za m'moyo uno, ndiye kuti mawu a Paulo omwe alembedwa mu 1 Atesalonika 5:18, “M'zonse yamikani; pakuti ichi ndi chifuniro cha mulungu cha kwa inu, mwa Khristu Yesu.” Adzakhala ochita nawo m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Yesu anakhala moyo Wotere, ndipo ife ngati tingafune kukhala opambana m'moyo wathu wa Chikhristu, tikuyenera kutsatira chitsanzo chake. Izi sizitanthauza kuti tikuyenera kukondwera ndi chirichonse chotichitikira, komano mu zonse tidzakhala oyamika kwa Mulungu – inde ngakhale kukondwera. Yesu Sadakondwere ndi anthu amene ankakhala ndi moyo ngati wa ziwanda pomuzunza, komano Adadziwa kuti dziko lidzadalit-

sidwa kupyolera m'mazunzo oterowo. Ifenso sitidzakondwera nthawi zonse ndi "Zinthu zonse" zotigwera, komano tikhoza kukhala moyo wa mayamiko!

Tikhoza kumuthokoza Iye potha kuona mwa ife chinthu chakuti Akhoza kugwira nacho ntchito. Ife ndi zida zimene, titatha kuwalitsidwa, tidzatha kuima mu nyumba Yake ya chifumu, ndipo mwala uliwonse udzakhala pa malo ake ake ndikukhala mokwanitsidwa. Mpikisano wonse udzatheratu, popezano mzimu wa kuweruza, wonyada ndi umbombo udzachotsedweratu pamodzi ndi mwini tchimo.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwaphunzira mu ndimeyi:

A. FUFUZANI

Mungachotse bwanji mzimu wa mpikisano ?

Zinkatheka bwanji Yesu kuwamvera chisoni m'malo modzimvera chisoni Yekha?

B. KHALANI MOYO WOTERO !!

"Ife ndife zipangizo zimene, titatha kuwalitsidwa, tidzakhoza kuyeneretsedwa kukhala m'nyumba Yake ya chifumu, ndipo mwala uliwonse udzakhala pa malo ake nudzakhala okwanitsidwa. Mpikisano wonse udzachokeratu, popeza mzimu wa kuweruza, kunyada, ndi umbombo udzachokeratu pamodzi ndi mwini tchimo." Funsani ndi pemphero kuti izi zikhale zenizeni m'moyo wanu. . .ndipo KHALANI MOYO WOTERO !!

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndi kusintha kwanji komwe kudzaoneka m'moyo wanga pamene Ambuye Ayankha pempho langa).

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 87.
2. Thoughts from the Mount of Blessing, Tsamba 71.
3. Thoughts from the Mount of Blessing, Tsamba 10.

15.

Chikondi

CHOPANDA MALIRE

...Ndi pachikondi cha pa abale, chikondi. (2 Petro 1:7). Chikonzetsero cha Mulungu sichinasinthe. Iye Adzam’bwezera munthu pa malo pamene chikondi chakuya cha Mulungu chosapingidwa chidzapitirira kuyenderera kumfikira munthuyo. Ichi chidzaposa momwe Adamu adaliri nthawi yomwe adangopangidwa kumene kuchokera m’manja a Mulungu. Chidali chikondi chotere chimene Yesu Adapempherera mu pemphereo Lake lomaliza kwa Akuphunzira Ake asanapite m’ munda wa Getsemane, “...Kuti Chikondi chimene Munandikonda nacho Chikhale mwa iwo, ndi Ine mwa iwo.” Yohane 17:26. Tangoganizirani, ngati mungathe kutero, Chikondi Cha mulungu Chikuyenda ngati mtsinje kudzera mu ngalande za anthu.

Chiyang’aniro cha chiyeretso ndicho kuonetsera Chikondi chotere mwa munthu. Sichikwaniritsidwa poyesetsa kukhala okonda, komano pakufa ku undekha, ndi ku zinthu zomwe zimalepheretsa kapena kutsamwitsa Mulungu kuchita ntchito Yake m’ moyo mwathu.

Mu njira yonseyi, kufikira pamwamba pa Makwerero amene tikuphunzirawa, njira yake ndi yofanana. Khwerero lomaliza ndilo kulawa Mphamvu Yoposa zonse kumwamba kapene padziko – Imene ili Chikondi Cha Mulungu. Cholepheretsa chachikulu ndicho chozimbaitsa chomwe chimabwera ndi satana polimbana ndi mphamvu Ya Mulungu – kutengeka kwa anthu. Nthawi zonse padzakhala kutengeka kwa anthu pokhudzana ndi pamene pali chikondi cha Mulungu, komano uku ndi kutengeka chabe, osati Chikondi Cha Mulungu.

“Mpingo ndiwo chida choikika ndi Mulungu pa chipulumutso cha munthu. Mpingo unakhazikitsidwa kuti utumikire Mulungu, ndipo ntchito Yake yaikulu ndiyo kutengera Uthenga Wabwino ku dziko lonse... Mpingo ndiwo nkhekwe ya chuma ndi chisomo cha Yesu Khristu: ndipo kupyolera mwa mpingo mudzaonetseredwa ‘Kuti mu Eklesia Azindikiritse tsopano kwa akulu ndi Maulamuliro m’zakumwamba Nzeru ya mitundumitundu Ya Mulungu.’ (Aefeso 3:10). Chionetsero chathunthu ndi chomaliala cha Chikondi Cha Mulungu”.¹

Ngati izi zingachitike m’masiku ano a kumapeto kwa mbiri ya dziko, ndiye kuti tikuyenera ife kudziwa kuti Kodi Chikondi Chimenechi ndicho chiti, komanso m’mene chingaonetseredwe ndi anthu.

Chikondi Cha Mulungu ndi Lamulo lokhazikika lomwe limayendetsa kumwamba komanso mayiko onse, kupatulapo dziko lapansi lokha. Ndi Lamulo la kuchita ntchito, lomwe ndi mbali ya moyo. Chikondi cha Mulungu Chiri ngati msewu wokhala ndi mbali ziwiri zolekanitsidwa ndi mzere woyera pakati pake: Chikondi Cha Mulungu Chimayenda mbali zonse ziwiri za msewu umenewu kuti ife tisakhale ndi chowiringula – Koyamba, pamene Mulungu Anadekha ndi kutenga nthawi yaitali pomudandaulira lusifala, m’malo mongomuonongeratu. Chifundo choterechi cholinga chake chinali chakuti zolengedwa Zake zonse zithe kumvetsetsa kuti Chikondi Cha Mulungudi N’chotani – kupatsa kwa aliyense mwayi wogwiritsa chifuniro chawo (Mphamvu ya kusankha) mwanzeru. Mu chisankho chawo chomaliza, gawo limodzi mwa magawu atatu a angelo okhala kumwamba, adasankha kuukira Mulungu.

Kuwawidwa mtima Kwa Mulungu potaya khamu lalikulu lotere la angelo, kutsatana ndi kusokonezedwa m’maganzizo kwa Angelo omvera otsalira kumwambako, komanso zolengedwa zina zokhala m’mayiko ena, zidapangitsa Mulungu kukhazikitsa Nzeru Yake yozizwa ya Chiombolo cha munthu. Chikondi Cha Mulungu Chimaonekera kwathunthu pamene ife timvetsa kuti “Kuyambira pachiyambi Mulungu Atate pamodzi ndi Yesu Khristu Adadziwiratu za kuukira kwa satana komanso za kugwa kwa munthu kupyolera mu mphamvu ya kunamizidwa ya m’dani.”²

Ngakhale nchachidziwikire kuti Mulungu Sanakonzeretu za mpatuko woterewu, Iye, mu Umulungu Wake Adaoneratu pat-sogolo za mpatuko oterewu, ndipo Adakonzeratu njira yoikiratu Chikondi Chake kwamuyaya m'mitima ya zolengedwa Zake.

Nzeru Yake ya Chipulumutsoyi iri yakuya zedi koteru kuti adaikhazikitsa pa kubadwa kwa Yesu mu umunthu. Yesu Khristu, Mwana Wa Mulungu, Adakhala munthu, kuti mtundu wa anthu pamodzi ndi chilengedwe chonse cha Mulungu ukhale ndi Chitsanzo Changwirowo Chowatsogolera ku nthawi zamuyaya pamene Chikondi Choterechi Cha Mulungu Chidzatsikira mwa iwo ndi kubwereranso kwa Mulungu. Ichi ndicho chisonyezo chachiwiri cha Chikondi Cha Mulungu.

Pameneno nzeru yotere ikuperekalamulo lobvomerezeka la chipulumutso cha munthu, likuperekanso chitsanzo chakuti mkhristu aliyense akuyenera kuchitsatira, potero chikondi Cha Mulungu Chidzayenda mwa iye. Yesu Adati, “Pakuti Ndinatsika kumwamba; osati Ndichite Chifuniro Changa, koma Chifuniro Cha Iye Amene Anandituma Ine.” Yohane 6:38. Paulo anati, “Ndinapachikidwa ndi Khristu; koma ndiri ndi moyo; wosat- inso ine ayi, koma Khritu ali ndi Moyo mwa ine; koma moyo umene ndiri nawo m'thupi, ndiri nawo m'chikhulupiriro cha Mwana Wa Mulungu, Amene Anandikonda, Nadzipereka Yekha chifukwa cha ine.” Agalatiya 2:20. “...Koma iwo a Khristu Yesu adapachika thupi, ndi zokhumba zache, ndi zilakolako zache.” Agalatiya 5:24.

Palibenso njira ina imene ingapangitse chikondi cha Mulungu kufikira kwa anthu. Pofuna kuti munthu akhale ngalande yotengeramo Chikondi cha Mulungu, undekha ukuyenera kupachikidwa. Maonekedwe ena alionse a umunthu amene atsalira mwa dala, adzaononga chithunzithunzi ndi kulepheretsa mpingo wa Mulungu kuonetsera ku maiko onse “Chikondi chodzadza ndi Chomalizira cha Mulungu.”

Chiyeretso chidzagwira ntchito yake mokwanira m'moyo wathu pamene ife tinena ndi mtima wonse mu zokumana nazo za m'oyo uno kuti, “Osati chifuniro changa koma Kufuna Kwanu Kuchitidwe.” Ichi ndichodi, Chikondi chopanda malire.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwaphunzira mu ndimeyi:

A. FUFUZANI:

“Chiyang’aniro cha chiyeretso ndicho kuonetseranso Chikondi Choterechi mwa munthu.” Kodi chimalepheretsa ndi chiyani?

Masulirani mawu awa: Chikondi Cha Umulungu.

B. PANGANI ICHI KUKHALA MOYO WANU !!

“Chiyeretso chidzakwaniritsa ntchito Yake m’miyoyo yathu pamene tidzanena moonana mtima mu zochitika zonse za m’moyo uno kuti, ‘Osati chifuniro changa koma Kufuna Kwanu Kuchitidwe.’ Funsani izi ndi pemphero kuti zikhale zoonadi m’moyo wanu ... ndipo **KHALANI MOYO WOTERO !!**

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, moyo wanga udzakhalawotere: (Ndi kusintha kotani komwe kudzaonekera m’moyo wanga pamene Ambuye Adzayankha pemphero langa).

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Machitachita a Atumwi, (The Acts of The Apotles), Tsamba 9 (Owonjezedwa).
2. Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 22.

16.

KODI YESU

Anayesedwa

MONGA IFE?

“Pakuti sitiri naye mkulu wa ansembe wosatha kumva chifundo ndi zofooka zathu, koma Wayesedwa m’zonse monga momwe ife, koma wopanda tchimo.” Aheberi 4:15. Lemba ili la M’baibulo lakhala, ndipo lidakali, gwero la makangano opanda phindu ochuluka, okhudza umunthu wa Khristu. Alipo ena amene amanena kuti Yesu Anayesedwa mofanana ndendende ndi umo ayesedwera munthu, kuti Akwaniritse zomwe lembali likunena. Izi zimapherezedwa mopanda kulingalirapo zomwe Mulungu Adabvumbulutsira ku Mpingo Wake zokhudza chiphunzitsochi.

Ngati Yesu Adayesedwa kuba, kunena bodza, kulumbira, kukhala ndi maganizo onyansa, ndiye kuti Adagonjetsa potsatira imodzi mwa njira zotsatirazi: (1) pogonjetsa yesero lachibadwa logwera ku uchimo, kapena (2) pozindikira kuti payekha Saka-dakhoza kugonjetsa, potero kutembenukira kwa Atate Wake. Mu njira zonsezi tikutha kuona kuti Akadayenera kukhala nalo danga lakuti satana alowererepo pomuchimwitsa Iye. M’malo mwake tikuona Yesu akuti, “Sindidzalankhulanso zambiri ndi inu, pakuti mkulu wa dziko lapansi adza; ndipo alibe kanthu mwa ine.” Yohane 14:30. Apatu nkuti Yesu ali ku mapeto a Moyo Wake pa dziko lino la pansi. Apa nkuti satana ataunguzaunguza gawo lirilonse la moyo Wake wa Khristu koma osapeza kalikonse kofuna kumukopera Iye.

“Ngakhale ndi ganizo limodzi lomwe Yesu Khristu Adalibe lakuti akakopeke ndi mayesero a satana mdier-ekezi. Satana nthawi zonse amapeza m’mitima ya anthu penapake pamene iye angapezepo danga – chilakolako

china chofuna tchimo chimapezeka, chimeneno satanayo amaonetserapo mphamvu yake.”¹

Kumbukirani kutitu Anali monga munthu pamene Yesu khristu Ankagonjetsa mayesero onsewa. “ Padalibe ganizo ndi limodzi lomwe kapena mamvedwe a mthupi aliwonse omvetserera ku mayesero.”² “Tchimo lina lirilonse, kusokonezeka kwina kulikonse, chilakolako china chirichonse chodetsa chobwera ndi tchimo chidali chozunza mzimu Wake.”³ “Musadzaganize m’jira ina iriyonse kapena kupangitsa ena kuganiza motero kuti maganizo a uchimo kapena chisokonekero china chirichonse chidamufikira Yesu Khristu, kapena kuti Iyeyo mu njira ina iriyonse adaganizirapo za chibvundi.”⁴ “Monga Wosachimwayo, Chikhalidwe Chake Chidali chodana ndi uchimo.”⁵

Lemba lathu lomwe tikuchita nalo likuti, “[Iye] Anayesedwa mu ngodya zonse monga ife...” ndipotu izi ndi zoona. Kuti tipeze yankho ku funso lakuti “nzotheka bwanji?” tiyeni tione ku zolemba zotsatirazi zokhudza Mbuye Wathu.

“Inali ntchito yobvuta zedi kwa Kalonga Wa Mten-dere kukwaniritsa njira ya chipulumutso cha munthu pobvekedwa umunthu ku Umulungu Wake. Iye Adali ndi ulemu onse m’ mabwalo a kumwamba ndipo Anali Mwini Wa mphamvu zonse. Zinali zobvuta kwambiri kwa Iye kuti Atsike kufikira pa mlingo wa umunthu, monga momwe zikhalira zobvuta kwa munthu kuti afikire pa mlingo wa khalidwe la Umulungu.”⁶

“ Pophimba Ulemerero Wake, nakhala monga mwana wa mtundu wa anthu akugwa, kudali ngati chilango chokhwimitsitsa chimene Kalonga wa Mtendere Adachita.”⁷ Apanso ndipo pamene tonsefe timakhala ndi zobvuta zathu. Ndi bvuto lalikulu kwa ife kuti tilolere Khalidwe la Umulungu la Khristu kuti lionekere mwa ife.

Tatiyeni tiunguze mwakuya zomwe lembali likuti uza. Zidali zobvutitsitsa kuti Yesu Khristu Abveke umunthu wathu ku Umulungu Wake. Chifukwa chiyani? “Yesu Sanaonetsera maonekedwe ena aliwonse, kapena kuonetsera mphamvu zina zirizonse

zimene anthu sangathe paokha kukhala nazo mwa chikhulupiro mwa Iye. Umunthu Wake Wangwiro ndiwo umene omtsatira Ake onse akuyenera kukhala nawo, ngati angafune kumvera Mulungu monga Iye Adachitira.”⁸ Yesu Adati, “Sindikhoza kuchita kanthu mwa Ine ndekha...” Yohane 5:30.

N’chachidziwikire kuti pamene Yesu Khristu “Adasiya korona Wake wa Chifumu ndi Mwinjiro Wake,”⁹ Iye Adadzitengera Yekha khalidwe la umunthu “monga momwe Mulungu Adamulengera munthuyo.” “Yesu Khristu Adabwera pano pa dziko, Atabvala umunthu Naima monga woimirira m’ malo mwa munthu, pofuna kuonetsera mu mkangano waukulu ndi satana kuti munthu, m’mene alili ndi monga m’mene Mulungu adamulengera, ngati atalumikizana ndi Atate ndi Mwana, nzotheka munthu otereyo kumvera Malamulo a Mulungu.”¹⁰ “Iye Adayamba pamene Adamu woyamba adayamba.”¹¹ Yesu Khristu, monga Adamu wachiwiri Adayenera kupambana pamalo pamene Adamu woyamba adalephera, pogwiritsa mphamvu yomweyomweyo iyo idapatsidwa kwa Adamu woyambayo pachiyambi. “Pamene Adamu adapezedwa ndi mdierekezi m’ munda wa Edene iye adalibe banga lina lililonse la tchimo... Yesu Khristu, m’chipululu cha mayesero, Adayima mmalo mwa Adamu kukomana nalo yesero lomwe Adamuyo adalephera kugonjetsa.”¹²

Palibe umboni m’ mawu a Mulungu wakuti chibadwa cha munthu wochimwa chikhoza kumvera Mulungu ! Uthenga wa Mulungu wopita kwa munthu ndiwo wakuti munthuyo ali ndi chibadwa cha uchimo chimene chiri chopanda chiyembekezo.

“Ana amabadwa mu uchimo. Tchimo lawalekanitsa iwo kuchokera kwa Mulungu wawo. Yesu anapereka moyo Wake kuti alunzanitse ugufu odukawo kwa Mulungu. Monga zidaliri ndi Adamu woyamba, anthu onse chilango chawo ndicho kutsutsika ndi chilango cha imfa.”¹³

“Popezano chisamaliro cha thupi chidana (udani) ndi Mulungu : pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu pakuti sichikhoza kutero.” Aroma 8:7 (owonjezedwa) Yesu Khristu Sanayeserepo kuonetsera kwa wina aliyense kuti chibadwa cha uchimo chikhoza kukhala chibadwa chosachimwa. Uthenga

Wake nthawi zonse udali wakuti, "...Uyenera kubadwa mwaso-pano." Yohane 3:7. "Ngati mbewu ya tirigu siigwa m'thaka niifa ikhala payokha iyo..." Yohane 12: 24. "...Kodi mukhoza kumwera chikho nditi Ndidzamwere Ine ? ndi kubatizidwa ubatizo ndibatizidwa nawo ?...Mateyu 20:22.

Ngati Khristu Anali ndichibadwa chosachimwa nangano zinatheka bwanji Iye kuyesedwa monga ine ndiyesedwera? Kodi mayesero ndi chiyani? "Mayesero amagonjetsedwa pamene munthu ali ndi chilakolako chachikulu chofuna kuchita tchimo, ndipo podziwa kuti iye akhoza kuchimwa, munthuyo payekha nasankha kusachimwa mwa chikhulupiriro, podalira mphamvu ya Umulungu."¹⁴ Mayesero amakhalapo pokhapokha pali "chikoka chachikulu chofuna kuchita tchimo." "Koma munthu aliyense ayesedwa pamene chilakolako cha iye mwini chimkokera nichimnyenga." Yakobo 1:14. Zikanatheka bwanji kuti Yesu Kristu Ayasedwe kuchita tchimo pamene "Chikhalidwe Chake cha Chiyero chidapangitsa uchimo kukhala owawa kwa Iye?"¹⁵ Yesu Khristu ankadana ndi tchimo ndi udani weniweni. Mzimu Wake, wokhala mwa munthu ndi wokhawo womwe Ungamuthandize munthu kudana ndi tchimo, zomwe mkhristu wina aliyense wobadwanso mwa Khristu ayenera kuchita.

Yesu Khristu kuti Ayasedwe monga ife tiyesedwera, zikadatanthauza kuti bwenzi Wayamba kaye kukhala ndi chilakolako chofuna kuchita choipa, komano Iye adakhulupirira kotheratu mwa Atate Wake. Nangano poterepa satana akadapeza bwanji danga? Satana adadziwa, ngakhale kuyambira nthawi yomwe Yesu Akali mwana, kuti kudali kungotaya nthawi chabe kuyesera kumuyesa Yesu kuti Abwezere. Ngakhale pozunzidwa, kuchitiridwa zoipa, kukwiyitsidwa, kuyambidwa dala, ngakhale kuchita chirichonse choipa, zonsezi mwa Iye munalibe.

"Mwa zowawa zonse zomwe anthu amakomana nazo, panalibe china chirichonse chimene Yesu Khristu Sanakomane nacho. Analipo ene amene ankamunyodogola chifukwa cha kubadwa kwake, ngakhalenso mu ubwana Wake Iye Adapilira iwo amene ankamuyang'ana momutonza ndi kukamba manong'onong'o omujeda. Iye akadakhocha kubwezera anthu oterewa ndi mawu akukwiya kapena kuyang'ana mwa nsontho, ngakhale

kuwabwezera anthu otere ndi choipa, Iyetu Akadatero Sakadakhala chitsanzo chathu changwiro. Potero Akadalephera kukwaniritsa nzeru ya chipulumutso.”¹⁶

Satana amadziwa kuti n’kobvuta kwa munthu kukhala padziko lino ngati mkhristu wobadwanso, amene nthawi zonse angapange moyo wake wobadwa mu uchimowu kupacikidwa pamtanda tsiku ndi tsiku. Iye amadziwa kuti zimatengera kufa tsiku ndi tsiku ku undekha (1 Akorinto 15:31) – ngakhalenso kupachika mosalekeza zizolowezi za chibadwa cha uchimo. 2 Akorinto 4:10-12. Potero anasinthana njira yomuyesera Khristu, pomuyesa kuti Yesuyo aonetsere chikhaliidwe chake chimene Adachileka pamene ankabwera ku dziko lino lapansi. Kuonetsera Chikhaliwe Chake cha Umulungu kukadatanthauza kuononga nzeru ya chipulumutso, popeza zimayenera kutengera kuti Yesu Agwiritse ntchito izo zokhazo zopezeka ndi munthu.

Sipadapezekepo munthu wina wosachimwa kufikir nthawi yokhayo imene Yesu Khristu Adabadwa mwa Maria. Kuchokeranso nthawi imene Yesu Adabadwa, sipanapezekenso munthu wina wosachimwa. Machitachita a satana pochita ndi makanda ochimwa, ana, achinyamata kapenanso akuluakulu kukadakhala kopanda ntchito pochita ndi umunthu osachimwa. Satanayo adayesetsa m’mene akadathera kumuumiriza Yesu Khristu kuti Aonetsere Umulungu Wake. Podziwa kuti bvuto lalikulu la Yesu Khristu pa dziko lino lapansi lidali lolandiridwa monga Mesiya (Wodzozedwayo), satana adayesetsa kupyolera mu chikhumbo chotere, navesetsa kumuyesa Yesu Khristu kuti Achoke M’manja Mwa atate Ake ndi kuyambano kugwiritsa ntchito Umulungu Wake womwe Iye Adayamba kaye Wausiya. Kuyambira mu ubwana Wake kukafikira pa Gologota, satana adayesetsa kuti apezerepo danga pa yesero lotereli. Mayesero a satanayo adanka akulira kulirabe kufikira pamtanda pamene satana adati, “Ngati Iwe uli khritu Tsika pamtandapo kuti tikhulupirire.” Yesu Khristu podziwa kuti Akadakhosha kuyankha nthawi ina iriyonse ndi kupangitsa omuzunzawo kuti amubvomereze monga Mbuye ndi Mfumu, Adakana kutero. Iye Adasiya Moyo Wake wa kanthawi kameneko, ndiponso nthawi ya kutsogolo M’manja a Atate Wake.

“Potero, pamene Yesu Khristu ankanyozedwa, Adakomana ndi yesero lalikulu lofuna kuonetsera khalidwe

Lake la Umulungu. Mwa liwu lokha, mwa kuyang'ana kokha, Akadatha kupangitsa onse omuzunzawo kubvomereza kuti ndiye Mbuye wa mafumu ndi maulamuliro, ansebe, ngakhalenso kachisi amene. Komano Iye Adasankha kugwiritsa chomwe Adasankha pachiyambi, ndicho kufanizidwa ndi umunthu."¹⁷

Yesero lalikulu nanga ! Palibe munthu angakhoze kuyesedwa monga iye adayesedwera !

Adayesedwa bwanji monga ife? Mkhristu wobadwanso mwatsopano akuyenera kufa ku chikhalidwe chake chakale cha uchimo. "Koma iwo a Khristu Yesu adapachika thupi ndi zokhumba zake ndi zilakolako zake." Agalatiya 5:24. Izitu zakambidwa mobwerezabwereza m' mau a Mulungu. Undekha ndiwo gwero la tchimo lonse.¹⁸ Pa chiweruziro, machimo onse adzaikidwa pansu pa mutu wakuti undekha.¹⁹ "Nangano chizindikiro cha mtima watsopano ndi chiyani? Ndicho moyo wosinthika. Zikufunika kufa ora lililonse, tsiku lililonse ku undekha ndi kunyada."²⁰ Zikadasonyeza undekha ngati Yesu Khristu Akadasankha kuchita zinthu mwa zokhumba Zake.

Tangoganizani mwakuya, ndipo mupeza kuti tchimo lililonse gwero lake ndilo undekha ! ndicho chifukwa chake chakuti pamene satana amuika m'mayesero Mkhristu wobadwanso mwa Khristu kuti achimwe, khalidwe lake lakale lija, lomwe iye adalipachika limakhalabe likumuumiriza kuti achimwe. Kodi izi zimatheka bwanji pamene tikudziwa kale kuti khalidwe lakale lija linapachikidwa ? Apatu ndipo pamene pamaonetseredwa m'mene satana agwirira ntchito yake. Satana amatengerapo mwayi kuti mkhristu wobadwanso mwatsopano, amene ali ndi khalidwe latsopano, nalungamitsidwa, salandira khalidwe latsopano munjira yomweyo. Khalidwe lake likuyenera kukulitsidwa. Izi zinali zoona kwa Adamu ndipo zidakali chomwecho ndi mtundu wonse wa anthu. Mulungu Adalenga Adamu wangwiro, komano zinadalira Adamuyo kukuza khalidwe lake kuti likhale langwiro, limeneno Adamuyo adalephera kutero. Apa ndipo pamene Yesu Khristu Adapambana, pamene Adamu adalephera. Poto Yesu Khristu Amayika pa mkhristu wobadwanso, khalidwe Lake losachimwalo. Khalidwe lotereli limaperekedwa kwa mkhristu amene amabvomereza Khristu ndikulolera kuti Yesu Khristuyo

Agwire ntchito ya kuyeretsa mwa iye, yomwe imatanthauza kuti Mulungu Agwire ntchito yakusintha khalidwe la munthu woteroyo kuti likhale lobvomerezeka mwa chilamulo pokhala wolungamitsidwa.

Nangano zimenezi zikugwirizana bwanji ndi m'mene satana amatiyesera ife? Tatiyeni titaona kuti tikamati khalidwe tikuntanthauzani. “Khalidwe limaonetseredwa, osati mwa ntchito zabwino za apa ndi apo, kapenanso kufuntha kwa apa ndi apo, komano mwa mau ndi ntchito zachizolowezi.”²¹ Chizolowezi ndicho chomwe chimapanga khalidwe. Chotero, pamene tikhala ndi chibadwa cha uchimo mwa ife, ndi kulora kuti chitilamulire, chizolowezi chomwe tipangacho chimaonetsera khalidwe lauchimolo.

Zizolowezi kapena khalidwe silingotha pompopompo; n'chifukwa chake “palibe chinthu chochedwa chiyero cha pompopompo.”²² Ndi zizolowezi zakale zokhala za mgonagona mu moyo wa mkhistu wobadwansoyu, ngakhale tikudziwa kuti zidakakonzedwa ndi Khristu, tithano kuona umo m'mene satana amatchera msampha wake. Amadziwa kuti alibe mphamvu yobweretsanso chibadwa chatu chakale kukhalanso chotakataka, ngakhalenso Yesu Khristu sangachifukule. Poto njira yokhayo yomwe satana angagwiritse ntchito ndiyo zizolowezi. Iye amatchera msampha, kudzera mwa anthu kapena mu zochitika, n'cholinga chakuti ife tigwiritse ntchito chibadwa chatu pokwiya kapena kubwezera. Akaterono satanayo amatidzudzula ife kuti chibadwa chatu chakale chija sichinafebe mwa ife. Mu njira imeneyi chofuna cha satana ndicho kutikhumudwitsa ife kuti tidziona ngati kuti sizikutheka, ndipo tingosiya kukhulupirira Yesu Khristu. Poto kumakhalanso ngati tadzutsanso khalidwe lathu lakale lija. Zikatero ndiye kuti satanayo akhozanso kutilamulira.

Kodi mukutha kuona kuti satanayu akumuyesa mkhristu mu njira yomweyomweyo yomwe adamuyesera nayo Yesu Khristu? Mu zitsanzo zonsezi satanayo akugwiritsa ntchito njira yakuti munthu afune kubwezera kapena kuonetsa mphamvu zake za chibadwidwe. Kusiyanana kwake ndikwakuti chibadwa chatu nchochimwa kale ndi kale, poto sitingachionetsera, pamene chikhaliwe cha Khristu Chidali cha Umulungu chotero akadalakalaka kuchionetsera. Mu zonse chofunikira ndicho kudalira ku mphamvu ya Mulungu – Yesu Khristu kudalira kwa Mulungu

Atate, ndipo ife kudalira kwa Yesu Khristu. Kudzipereka kwa Yesu Khristu Kudamtengera Iye kukapachikidwa pa Mtanda ndi kuoneka ngati wagonjetsedwa, mkuona kwa umunthu. Komano kudzipereka kwathu kwa Mulungu kudzatitengera ife ku moyo wosatha ndi kukhala mu mtendere ndi Mulungu.

Undekha, omwe ndiwo muzu, ndiwo pachimake pa nkondo yonseyi. Komano pali kusiyana kwakukulu pakati pa mayesero a Yesu Khristu ndi mayesero athu. Ngati ife titalephera, "...Ndipo akachimwa wina, Nkhoswe tiri Nayo kwa Tate, ndiye Yesu Khristu Wolungama." 1 Yohane 2:1. Ngati Yesu Akadachimwa, ndiye kuti kudali kutayika kwa muyaya ! Nzeru yonse ya chipulumutso ikadalephereka ndipo satana akadapambana.

Indedi, "...[Iye] Wayesedwa m'zonse monga momwe ife, koma Wopanda uchimo." Ahebri 4:15.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwawerenga mu ndimeyi:

A. FUFUZANI

"Yesu Anayesedwa mu zonse monga ife tiri?" Kodi yesero Lake linali lotani? (Muoneni Iye m'chipululu, komanso pa mtanda...) Ngati ife "okhulupirira olungamitsidwa", ndi mayesero anji omwe timakomana nawo ?

Kodi ntchito ya Chiyeretso pokonza khalidwe la mkhristu "wobadwanso" ndi chiyani? Nanga ndi dera liti lomwe linasiidwa loti satana akhoza kumugwetsa munthu?

B. PANGANI KUKHALA MOYO WANU

"Kudzipereka kwathu kumatitengera ife ku moyo wosatha ndi mtendere ndi Mulungu." Pemphani ndi pemphero kuti umenewu ukhale moyo wanu...ndipo **KHALANI MOYO WOTERO !!**

Popeza pemphero langa layankhidwa, moyo wanga udzakhala wotere: (Ndi kusintha kwanji komwe kudzaoneka m'moyo wanga pamene Ambuye ayankha pemphero langa).

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

1. The Review and Herald, November 8, 1887
2. Maumboni, (Testimonies), Bukhu 5, Tsamba 422
3. Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 111
4. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1128, 1129, Kalata 8, 1895 (Yowonjezedwa).
5. Maumboni, (Testimonies), Bukhu 2, Tsamba 202.
6. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7, Tsamba 930, The Review and Herald April 1, 1875, (Lowonjezedwa).
7. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1081, Kalata 19, 1901 (Yoonjezedwa).
8. Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 664 (Lowonjezedwa)
9. The Review and Herald, June 15, 1905.
10. Zizindikiro za Nthawi, (Signs of The Times), June 9, 1898. (Zowonjezedwa)
11. Namkungwi wa Achinyamata, (The Youth's Instructor) June 2, 1898. (Owonjezedwa)
12. The Review and Herald, July 28, 1874.
13. Mtsogozi wa ana (Child Guidance), Tsamba 475.
14. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1082, Namkungwi wa achinyamata, (The Youth's Instructor), July 20, 1899.
15. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7A, Tsamba 451, The Review and Herald, November 8, 1887.
16. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 88.
17. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire Of Ages), Tsamba 700, (Loonjezedwa).
18. Mtsogozi wa Ana, (Child Guidance), Tsamba 294.
19. Chuma Cha Maumboni, (Testimony Treasures) Bukhu 1, Tsamba 518.
20. Namkungwi wa Achinyamata, (The Youth's Instructor), September 26, 1901.
21. Mapazi Opita Kwa Khristu, (Steps To Christ), Tsamba 57, 58.
22. Moyo wa Chiyero, (The Sanctified Life), Tsamba 10.

17.

UNDITSATE *Ine*

“Pomwepo Yesu anati kwa Akuphunzira ake, ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, natenge mtanda wake, nanditsane Ine.” Mateyu 16:24.

“Yesu anafotokoza kwa Ophunzira Ake kuti Moyo Wake wodzikaniza Yekha unali chitsanzo chakuti iwo atengere. Podziitanira kwa iye yekha Ophunzira Ake pamodzi ndi anthu ena omwe anali pafupi, Iye anati, ‘Ngati munthu afuna kutsatira Ine, adzikanize yekha, natenge mtanda wake tsiku ndi tsiku, nanditsate Ine.’ Mtanda unkadziwika bwino ndi mphamvu ya chi Roma. Mtanda udali chida chozunza ndi kupha anthu mwankhanza. Zigawenga zokalangidwa zimayenera kunyamula zokha mtanda wawo kupita ku malo komwe zikapachikidwe. Poziika zigawengazo mtandawo pa mapewa awo zigawengazo zinkalimbalinga kufikira atazimangirira ku mtandawo kuti ziduduluze zokha mtandawo. Komano Yesu Akuuza omutsatira kuti akuyenera kutenga ndi kusenza okha mtanda wawo pomutsatira Iye. Kwa ophunzira Ake, mawu oterewa, ngakhale sanathe kuwamvetsa kwenikweni tanthauzo lake, komabe anadziwa kuti akutanthauza kudzipereka kwao mogonja ndi mwa manyazi. – Kuzipereka ndi kugonja kufikira imfa chifuwa cha Yesu Khristu. Mawu a Yesu Khristu Sakadaposerera apa.”¹

Mutha kuona kuti Luka adaonjezera mawu akuti, “Tsiku ndi tsiku” . Mtanthauzira mawu wa Webster, akutanthauzira

liwu limeneli lakuti kudzikaniza monga “Kugonja” kapena “Kulekeratu.” Pamene tizindikira tanthauzo limeneli la kugonja kuti likufikira mpaka imfa, limakhala ndi tanthauzo latsopano, kwenikweni tikaonjezerapo liwu lakuti “Tsiku ndi tsiku.” Paulo adati, “Ndifa tsiku ndi tsiku.” 1 Akorinto 15:31, ndipo akupitirizanso kulemba kuti, “Nthawi zonse tiri kusenzasenza m’thupi kufa Kwake kwa Yesu, kuti Moyonso Wa Yesu uoneke m’thupi mwathu. Pakuti ife amene tiri ndi moyo tipereka ku imfa thawi zonse, chifukwa cha Yesu, kuti moyonso wa Yesu Uoneke m’thupi lathu lakufa. Chotero imfa ichita mwa ife, koma moyo mwa inu.” 2 Akorinto 4:10 -12.

N’chachidziwikire kuti pali njira imodzi yokha yowonetsera chithunzi cha Yesu, ndiko osati kuyesa, koma kufa. Popeza izi zalembedwa m’Baibulo, satana walimbana nazo kwa nthawi yaitali. Iye wakhazikika kwambiri pa mawu okha a Yesu akuti “kudzikaniza.” Satana wayesetsa kutipanga ife kuganiza kuti kudzikaniza, n’chimodzimodzi ndi kudzikana wekha. Posemphanitsa mauwa, matanthauzo akenso akukhala osemphana.

Kudzikana wekha kukhoza kukhala mbali imodzi yothandiza pa kukonza khalidwe lathu. Komano kusafanizidwe ndi kudzikani-za wekha, komwe ndiko kupachika undekha. Pamene Yesu Khristu akhala pa mpando wa mtima wathu, undekha umachotsedwa; ndipo pamene undekha ukhala pamando wa mtima wathu, Yesu Khristu Amachotsedwa. Chisankho china chirichonse chomwe tingapange chikuyenera kugwiritsa ntchito njira yomwe Yesu Khristu Anagwiritsa, “Osati chifuniro Changa koma kufuna Kwanu Kuchitidwe.” Mpulumutsi Wathu anatsatira njira imeneyi kwathunthu kotero kuti Anatha kunena kuti, “...Mawu Amene Ndinena kwa inu sindilankhula kwa Ine Ndekha; koma Atate Wokhala mwa Ine Achita ntchito Zake.” Yohane 14:10.

Chinali chinsinsi chotere chimene Paulo anaphunzira, naphunzitsanso kwa Timoteo kuti chikhale maziko a moyo wathu mwa Khristu ku nthawi zonse. Iye adati, “Okhulupirika mauwa: Pakuti ngati tidamwalira ndi Iye, tidzakhalanso moyo ndi Iye.” 2 Timoteo 2:11.

Yesu Sanangonena kokha kuti tidzikanize tokha, komanso Anati titenge mtanda wathu. Ndizozizwitsa kuona kuti Yesu Khristu akugwiritsa ntchito Mtanda monga chida cholunzanitsira wokhulupirira, kwa Iye Mwini.

“Goli ndi Mtanda ndi zizindikiro zoyimira chinthu chimodzi – kutaya chifuniro chathu kwa Mulungu. Kunyamula Goli kumalumikiza munthu wakugwa ku chiyanjano ndi Mwana Wokonedwa Wa Mulungu. Kusenza Mtanda kumachotsa undekha m’ moyo mwathu ndi kutiika ife pa malo pamene tingathe kusenza Goli La Yesu. Ife sitingathe kutsatira Yesu popanda kubvala Goli Lake, kapena kusenza mtanda ndi kumutsatira nawo Iye.”²

“Sitingathe ife kusungabe undekha mkati mwathu, tiganizira kuti tidzalowa nawo mu Ufumu wa Mulungu. Ngati ife tidzafike pa chidzalo cha chihero, zidzadalira kulekana nawo undekha ndi kulandira mtima wonga wa Yesu Khristu.”³

“Chifukwa chimene anthu ambiri pa dziko lino satha kukula m’ moyo wao wa Uzimu ndicho chakuti amanthauzira chifuniro cha Mulungu ngati kuti ndicho kufuna zomwe iwo afuna kuchita. Anthu oterewa, potsatira zokhumba zawo, amadzinamiza okha kuti akuchita chifuniro cha Mulungu. Anthu oterewa salimbana ndi undekha. Aliponso ena amene kwa kanthawi kochepe amaoneka ngati akupambana mu nkondo yawo yolimbana ndi undekha ndi chilakolako chodzikondweretsa okha. Inde, amaonekadi ngati akukwanitsa nkondoyi pa okha, komano posakhalitsa amatopa m’ kuyesetsa kwao kofa tsiku ndi tsiku ndi katundu wolemera chotereyu. Ulesi umayamba kuitana, kufa ku undekha kuja kumakhalano chonyansa, kenakono amatseka maso awo nagwa ku mphamvu ya mayesero m’ malo mogonjetsa mayesowo.”⁴

Mawu a Yesu Otsindika onena kuti, “Unditsate Ine”, ndi osatheka pokhapokha titakwaniritsa zomwe lembali likunena. Yesu Khristu Sankatanthauza kwa Ophunzira Ake ndi kwa Ot-satira ake kuti adzichita monga Iye Ankachitira, koma kuti iwo adzikhala moyo wofanana ndi Moyo Wake.

Atate Mulungu Adachita kupyolera mwa Yesu Khristu, Zomwe Mulunguyo Adamtumira Yesu kudzachita pa dziko lino.

Izi zinali zotheka chifukwa Yesu Khristu Adasankha mphindi iliyonse ya Moyo Wake, kukhala monga ngati dongo m’manja a Atate Wake. M’ malo Ake onse omwe Iye Adakhala, kugonjera kotereku kunabweretsa chiyembekezo cha mtendere ku dziko lapansi lomwe linali mu mpungwepungwe wa chisokonekero chifukwa cha kuukira kwa lusifala amene anasanduka kukhala satana. Ifenso, m’ malo athu omwe tikukhala, kudzipereka kotereku kwa Yesu Khristu kudzatipatsa ife chiyembekezo chatu cha chipulumutso. Ndi mwayi wathu kukhala padziko lino moyo umene Yesu Khristu angaugwiritse ntchito ngati chikoka cha maginito chowauza anthu onse za nzeru Ya Mulungu Yopulumutsira munthu. Njira imeneyi ndiyo yokhayo imene ingawakonzetsere anthu kukhala moyo wamuyaya m’ malo angwiro a kwawo kwa opulumutsidwa.

“Kumvera kotheratu ku Mawu a Yesu Khristu ndiko kudzichepetsa kwenikweni kofunika, kumenenso kuli kugonja ku undekha kwenikweni.”⁵ “Kugonja ku undekha ndiko thunthu lenileni la chiphunzitso cha Yesu Khristu.”⁶ Ndi pokhapokha ife tiona kufunikira kwa kukhulupirira Yesu Khristu kwathunthu, ngakhale zina zonse zingaoneke ngati zosatheka, pameneno tidzaona kufunikira kwa mawu a Yesu khristu a kwa Nikodemo akuti, “Ukabadwenso.”

M’ kubadwa kwathu kwa umunthu mu dziko lino lapansi ife tinalibe chisankho china chirichonse, koma mu nkhani iyi yobabwanso kachiwiri mu uzimu yadalira pa chisankho chatu chaufulu, chopanda kumirizidwa, chomwe chingakhale cha ufulu pakusankha kwathu kufa ku undekha ndi kulola Yesu Khristu kukhala m’ moyo mwathu.

Mateyu akutseka Uthenga wake wabwino polemba mawu a Yesu Khristu, “...Mphamvu zonse [ulamuliro, nyonga] zapatidwa kwa Ine kumwamba ndi pa dziko lapansi.” Mateyu 28:18. Uko ndiko kunali kyankha kwa Mulungu Atate kwa Mwana Wake chifukwa cha moyo wodzipereka kotheratu nthawi yomwe Adali pa dziko lino nakhala mu thupi la umunthu.

Yesu Khristu Anayesedwa kutsatira njira zachidule. Mu chipululu, nthawi yomwe ankayamba utumiki Wake, satana adayesetsa kumuonetsera njira yachidule. Atatha kumuonetsera

maufumu onse a dziko lino ndi maulemerero awo, satana anati, "...Zonse ndikupatsani inu, ngati mudzagwa pansi ndi kundigwadirira ine." Mateyu 4:9. Njira yachidule nanga ! Komano posankha kukhulupirira ndi kudalira Mulungu, ngakhale idali njira ya mtanda, komanso kulolera kufa, Iye Adalandira kuchokera kwa Atate Wake mphamvu zonse kumwamba ndi dziko lapansi. Tisaiwale kuti Yesu Khristu Anapanga chisankho chimenechi Adakali m'thupi la umunthu monga ife tiri, popanda mphamvu ina iriyonse yapadera imene ife tiribe.

"Yesu Khristu Sanaonetsere makhalidwe, kapena kuonetsera mphamvu zimene anthu sangathe kukhala nazo mwa chikhulupiriro mwa Iye. Umunthu Wake wangwiwo ndiwo umene otsatira Ake onse akuyenera kukhala nawo ngati iwo atakhala omvera kotheratu kwa Mulungu monga Iye Adachitira."⁷

Njira yachinyengo yachidule yeniyeni yomwe satana adamuonetsera Yesu idali kumayambiro kwa mayesero a m'chipululu.

"Iye [satana] anayetsa kumupanga Yesu kukhulupirira kuti Mulungu Sankafuna kuti Iye Adutse njira yodzikaniza Yekha ndi yozunzika yomwe inali patsogolo Pake; komano kuti satanayo watumidwa kuchokera kumwamba kudzamuuzwa Yesuyo uthenga wakuti chomwe Mulungu Ankangofuna ndicho kusonyeza kulolera kwake kokhako basi."

"satana adamuuzwa Yesu Khristu kuti Adangoyenera kungoponda kokha mu njira ya mwazi, osati kuchita kuyenda njira yonse mpaka kumapeto. Satanayo adamuuzanso Yesu kuti iye satanayo adali mgelo amene anagwira dzanja la Abrahamu pamene Abrahamuyo adakweza mpeni kufuna kupha Isake, chomwecho iye satanayo wabweranso kudzapulumutsa moyo wa Yesu Khristu; komanso kuti sikudali kofunika kuti Yesu Khristuyo Achite kuzunzika ndi njala ndi imfa yowawa; komano kuti iye satanayo adzamuthandizako gawo lina la nzeru imeneyi ya chipulumutso."⁸

Satana wakhala akufikira mwana aliyense wa Adamu, kuyambira pachiyambi ndi uthenga ngati omwewu, "Yesu Khristu

anakufera, kotero sikoyenera kuti iwenso ufe.” Zimamveka ngati zabwino chifukwa mkatimo muli ngati ka choonadi. Indedi Yesu Khristu anafa kutipulumutsa ife ku mphotho ya uchimo imene ili imfa ya muyaya. Komanso, Yesu Khristuyo anakhala moyo wodzikhuthula kotheratu ku undekha monga ngati chitsanzo cha momwe ife tiyenera kukhalira. Satana adzayesetsa kubweretsa njira ina iriyonse yachidule kwa mkhristu amene akulimbana ndi uchimo, koma tidziwe kuti njira yokhayo yopita ku ufumu wa Mulungu ndiyo yotsatira Yesu Khristu.

Mafunso okuthandizani kuchita zomwe mwawerenga m’ndimeyi:

A. FUFUZANI

“Kudzikaniza wekha” ndi “Kufa ku undekha”: Siyanitsani ziganizo ziwirizi. Kodi n’chifukwa chiyani “Kudzikaniza wekha” kuli kwa mtengo wapatali m’moyo wathu wa chikhristu?

Ndi mphamvu yanji imene Yesu Khristu Anadandaulira kuti ndi yofunikira pa chipambano chathu? Ndi njira ziti zachidule zomwe satana adamuonetsera Yesu Khristu?

B. KHALANI MOYO WOTERO !!

“satana adzayesetsa kubweretsa njira zonse zachidule kwa mkhristu amene akulimbana ndi uchimo, koma njira yokhayo yopita ku Ufumu wa Mulungu ndiyo kutsatira Yesu Khristu.” Pemphani ndi pemphero kuti izi zikhale moyo wanu... ndipo **KHALANI MOYO WOTERO !!**

Chifukwa pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndikusintha kwanji komwe kudzachitika m’moyo wanga pamene Ambuye ayankha pemphero langa).

Mabuku Omwe agwiritsidwa ntchito mu ndimeyi:

1. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 416 -417.
2. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1090 -1091, The Review and Herald, October 23, 1900. (Owonjezeredwa).
3. Thoughts from the Mount of Blessing, Tsamba 143, (Oonjezeredwa)
4. Machitachita a Atumwi, (The Acts of The Apostles), Tsamba 565.
5. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 535.
6. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 523.
7. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 644. (Oonjezeredwa)
8. Mauthenga Osankhika, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 273.

18.

KHALANI MWA Ine

Ndime yakhumi ndi chitatu ya yohane ikutionetsera ife Mgonero Wa ambuye Umene Yesu Khristu Anadya usiku omaliza Asanapachikidwe. Pa Mgonero umenewu, m' modzi wa Ophunzira wake anayenera kuchoka, osadzayendanso ndi anzake. Yudasi adzampereka Mbuye wake poganiza kuti akuthandizira kukweza ufumu wa Mulungu padziko. Mwa nthawi zonse, Petro anafunsa funso limene onse ankaliganizira: “Mupita kuti Ambuye nanga n'chifukwa chiyani sitinganke Nanu?” Chomwecho panabwera kudzipereka kwathunthu, “Ndidzataya moyo wanga chifukwa cha Inu.” Yohane 13:37. Komatu usiku omwewo Petro ndi Akuphunzira ena adzapanga chisankho china.

Marko 14:30 -31 akuti, “Ndipo Yesu Ananena naye, ndithu ndinena ndi iwe, kuti lero, usiku uno, tambala asanalire kawiri, udzandikana ine katatu. Koma iye analimbitsa mawu chilimbitsire kuti, Ngakhale ndidzafa nanu, sindidzakana inu. Ndipo onsewo anatero.” (Mawu owonjezedwa.)

Yesu anadziwa kuti kuyankha kwa Ophunzirawa kunali koono mtima, komano thupi ndilo linali lofooka. Kulephera kwa iwo eni kudzakhala chida chachikulu cha satana chowakhumudwitsira. Pofuna kuwakonzetsera chokumana nachochi, Yesu Adawauza uthenga wabwino wopezeka mu Yohane 14.

Kumapeto kwa uthenga umenewu Yesu Ananena mawu akuti, “Nyamukani tizimuka kuchokera kuno.” Yesu adadziwa komwe ankapita. Ophunzira Ake ankangolalakalaka kukhala Naye pafupi, chomwecho adamtsatira. Unali usiku, ndipo mosakaikira, m' misewu yonse munali pikitipikiti ndi anthu popeza inali nthawi ya nyengo ya Paska. Mu nyengo yonga ngati imeneyi, m' mbali

monse mwa mapiri munali tizisumbu ta mahema okhalamo anthu, pakuti mu mzindamo munalibe malo okwanira aliyense wobwera pa nyengo ya Paska yotereyi.

Yesu ndi Ophunzira ake anachoka m'chipinda cha pamwamba napita ku msewu. Iye Adawatsogolera, Napita onse ku malo Ake a chizolowezi amene Adawakonda – Phiri la Azitona. Iye sikuti ankapita kumeneku pa nthawi iyi, koma Adangotengerapo mwayi Ataona mpesa wakupsa, kuti Apereke phunziro lofunikira kwa Ophunzira Ake Okondedwawa.

Mwezi unali kuwalira pa mpesawo pamene Yesu Anayima Nauyang'anitsitsa. Zidapangitsanso kuti Ophunzira aliyense ayang'anitsitse mpesawo. Kenakono Mawu A Yesu anamveka mwamphamvu mu kayaziyazi wa usikuwo, ' Ine Ndine Mpesa weniweni, ndipo Atate Wanga Ndiye Wam'munda." Yohane 15:1. Ndikutha kumumva Petro akutembenukira kwa Yohane ndikumufunsa kuti, "Kodi wamva zomwe Ambuye Wanena? Sindikumvetsa, popeza aliyense akudziwa kuti Israeli ndiye Mpesa!" Ndikuthanso kumuona Yohane akuyankha kuti, "Inenso sindikutha kumvetsa, komabe tiyeko timvetsere. Mwina Atifotokozerwa bwino." Pomwepo Yesu Adapitiriza kuphunzitsa phunziro Lake.

"Nthambi iriyonse ya mwa Ine yosabala chipatso [Atate Wanga] Aichotsa; ndi iri yonse yakubala chipatso Aisadza, kuti ikabale chipatso chochuluka." Yohane 15:2.

Mawu akuti "Mpesa", "Nthambi", "Wam'munda", "aisadza", ndi ena otero, anali mawu odziwika bwino, popeza minda ya mpesa inali yochuluka m'deralo. Ophunzirawo adamvetsetsa bwino lomwe kuti kusadza kunkachitika ndi mpeni wosadzira. Mosakaikira, uthenga uwu wakuti nthambi yosabala chipatso idzachotsedwa, koma ngati ibala chipatso idzangosadzidwa unali uthenga womveka bwino ndithu, ngakhale unali uthenga wosagwirizana ndi momwe iwo eni ankaganizira. Ayuda sadayenera chilango chotero! Iwo anali ana a Israeli –ana a Abrahamu ! kwa zaka zochuluka iwo adali mu Mpesa, kufikira, m'maganizo mwao, anali Mpesa umene.

Yesu Adayesera kuwalimbikitsa Ophunzirawa powauza kuti, "Mwakhala okonzeka tsopano inu chifukwa cha mawu amene Ndalankhula ndi inu." Yohane 15:3. Mawu amenewa tikhoza kuwamvetsetsa bwino tikawerenga mavesi ena monga, "Mawu

a Khristu akhalitse mwa inu chichulukire ...” Akolose 3:16. “Mwa ichi mutabvula chinyanso chonse ndi chisefukiro cha choipa, landirani ndi chifatso mawu ookedwa mwa inu, okhoza kupulumutsa moyo wanu. Khalani akuchita Mawu, osati akumva okha, ndi kudziyenga nokha.” Yakobo 1:21-22. Chomwe Yesu ankanena ndicho chakuti, “Inu mwayeretsedwa kale kupyolera m’kukhulupirira mawu omwe Ndalankhula kwa inu.”

Katundu weniweni yemwe anali mu mtima mwa Yesu Khristu walembedwa mu vesi lotsatirali: “Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa inu...” Yohane 15:4. N’chachidziwikire kuti Ambuye Yesu ankayang’ana kutsogolo za mayesero Ake ndi kupachikidwa, kumene ngakhale Ophunzira Ake omwe adzamukane. Anawasindikizira mfundo zimene iwo anali asanazionepo. “... Monga nthambi siingathe kubala chipatso payokha ngati siikhala mwa mpesa; motero mulibe inunso ngati simukhala mwa Ine.” Yohane 15:4. Izi ndizoono ngakhale lero lino; sitingathe kuchita kanthu kalikonse pokhapokha titakhala mwa Iye. Ngakhale zinthu zina zingaoneke zosatheka ndi zosokonekera, uthenga wake ndi omwewobe: “Khalani mwa Ine; khulupirani Ine.”

Uthengawu wa Mpesa ndi nthambi zake ukhoza kumveka bwino tikaufanizira ndi bukhu la Aroma 11. Mu ndime imeneyi ikutiuzwa za mtengo wa azitona m’ malo mwa mpesa. Zonsezi zikuimira Israeli, potero zinali kupatsidwa ulemu onse ndi Ayuda. Mtengo wakuthengo wa azitona unali kuimirira athu achikunja, ndipo mtengo wabwino wa azitona unali kuimirira Israeli.

Namphatika ndiyo njira yamakono ya ulimi imene mtengo wakuthengo umaphatikizidwa ndi mtengo wabwino, potero nusanduka kukhala mtengo wabwino. Njira imeneyi ya namphatika imatiphunzitsa ife chinsinsi chokhala moyo wa Chikhristu. Monga zinthu zina zirizonse zofunikira, ife tikuyenera kuikapo mtima pofukula kuti tipezemo choonadi.

Pamene Aroma 11:24 akunena za mtengo wa azitona wakuthengo ndi mtengo wa azitona wabwino, Paulo akunena za ufumu wa satana ndi ufumu wa Mulungu. Njira yokhayo imene nthambi yochokera kwa satana ndi ufumu wake ingakhalire nthambi ya mwa Yesu Khristu ndi ufumu Wake ndi kupyolera mu njira yokhayo ya namphatika.

Wam’munda (Yesu Khristu) akunka afunafuna nthambi (ife) zomwe zilakalaka kukhala mbali ya ufumu Wake. Yesu Khristu

Akuti, “Inu simunandisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala chipatso...” Yohane 15:16. Yesu Khristu, mwa Chikondi Chake Chosaneneka, Akuitana anthu onse, koma ndi ochepa okha amene amabvomera kuitana kotere.

Yesu Khristu asanayambe kuchita kena kalikonse kuphatika nthambizi kwa Iye Yekha, Akuyenera kukonzetsera mtengo wabwino wa azitona kuti uthe kulandira mtengo wakuthengo wa azitona. Paulo akuti zoterezi ndi zosemphana ndi chilengedwe. Nanga titi bwanji? Kodi nanga njira zambiri za munthu sindizo zosephana kumene ndi za Yesu Khristu? “Pakuti Maganizo anga Sali maganizo anu, ngakhale Njira Zanga Siziri Njira zanu, Ati Yehova.” Yesaya 55:8.

Munthu amatenga nthambi yabwino naiphatika ku phesi lakuthengo kapena muzu wakuthengo, potero amatha kumeretsa chipatso chabwino. Mulungu Amatenga nthambi ya kuthengo, Naiphatika ku muzu woonongeka, Nakhoza kutulutsapo chipatso chokometsetsa. Munthu sangathe kuchita mofanana ndi m’mene Mulungu Achitira. Nzeru yonse ya chipulumutso ikutanthauza Mulungu kuchita mu njira yomwe Adziwa Iye Mwini m’miyoyo ya anthu, ndipo munthuyo nam’atsa Mulunguyo mwa ufulu onse.

Ngati munthuyo atayesera kuchita ntchito yake mofanizira Mulungu, ndiye kuti zotsatira zake zikhoza kukhala zipatso zakuthengo zochuluka. Phunziro ili litiphunzitse ife kuti ntchito yathu yokha yomwe tiyenera kugwira ndiyo kudzipereka ndi kukhulupirira Mlengi wathu. “Ngati inu muli ofuna ndi omvera, mudzadya zabwino za dziko.” Yesaya 1:19. Kufunako ndiko kwathu; kumverako, Iye Amakwaniritsa mwa munthu aliyense okhulupirira.

Mulungu adakonza Mtengo wabwino wa Azitona kuti ulandire nthambi zakuthengo pa Gologota. Koma ife timati, “Nangano omwe adachokera kuyambira nthawi ya Adamu kufikira pa Gologota?” Kumbukirani kuti Yesu Khristu ndiye “... Mwana Wa Nkhosa Wophedwa kuyambira makhazikidwe a dziko lapansi.” Chibvumbulutso 13:8. Nthambi ina iriyonse ya kuthengo kuyambira nthawi ya Adamu kufikira nthawi yomwe Yesu Khristu Adzabweranso ikuyenera kuphatikizidwa pa Gologota.

“Nyali yochokera pa mtanda imaonetsera chikondi cha Mulungu. Chikondi Chake Chimatikokera ife Kwa

Iye. Ngati ife sitingalimbelimbe ku chikondi choterechi, tidzatsogozedwa kufikira pansu pa mtanda polapa machimo athu amene anampachikitsa Mpulumutsi. Pomwepo Mzimu Wa Mulungu, mwa chikhulupiriro, Udzatipatsa ife moyo watsopano. Maganizo athu ndi zilakolako zathu zidzakhala zomvera chifuniro cha Yesu Khristu. Mtima wathu, maganizo athu adzalengedwanso mwatsopano mu chifaniziro cha Iye Amene Achita mwa ife kukhazikitsa zonse kwa Iye Yekha.”¹

Tsopano popeza takokeredwa pa Gologota, tiyeni tione momwe Wam’ munda Achitira namphatika Wake. Monga Mlimi wa zipatso, Mwinimunda amatenga nangoleka wake, nadula nthambi yololerayo naichotseratu kuchoka ku nthambi yake yoyambirira yomwe inkapereka moyo. Ntchito yotereyi imakhala yowawa ndipo imachitidwa ndi Mwinimunda. Mbali yathu yokha ndiyo kulakalaka ndi kulolera kuti Iye Achite ntchito Yake mwa ife. Tiyenera kuyesetsa kusawiringula zam’mene Iye Achitira ntchito Yake.

Mtengo wabwino wa Azitona uyenera kuvulazidwa kumene, n’cholinga chakuti uthe kulandira nthambi yophatikidwa nayo. Bala loterelo linapyozedwa pa Gologota. Potero, nthambi yatsopanoyo ikuyenera kulowa mu bala la pa Gologotalo. “... Yense amene abvomereza Ine polandira nsembe Yanga ya kwa ochimwa, adzabvomerezedwa monga otenga nawo mbali mu ulemerero ndi chimwemwe cha owomboledwa.”²

Paulo adati, “Ndinapachikidwa ndi Khristu...” Agalatiya 2:20. Paulo akunenanso kuti, “...Koma iwo a Khristu Yesu adapachika thupi [chikhalidwe chao chakale] ndi zokhumba zake ndi zilakolako zake.” Agalatiya 5:24. Pamene nthambi idulidwa kuchokera ku mtengo wake wakale, zikutanthauza kuti yachotsedweratu ku gwero la moyo wake woyamba wakale. Komano Wam’ munda salekeza pomwepo nauleka kuti ufe paokha. Iyeyo Amatengano nthambi yopwetekedwayo naiika mosamalitsa mu mtengo wa Azitona wopwetekedwawo. Atatero amaukutano ndi phula (Mwinjiro Wake wa Chilungamo). Phula lomatidwa polumikizirapo limathandiza kuletsa nthenda iliyonse kapena tizilombo tilitonse toononga tomwe tingalepheretse makulidwe atsopano.

“Ulemerero Wa Atate Udamkuta Yesu, potero padalibe china chirichonse Chidam’gwera Iye koma chokhacho chimene Nzeru Ya Mulungu Idabvomereza kuti chikhoza kukhala mdalitso ku dziko. Apa ndipo padagona magwero a chithonhozo Chake, poteronso akhoza kukhala magwero a chithonhozo chatu. Iye amene adzadzidwa ndi Mzimu Wa Khristu akhala mwa Khristu. Chipsinjo cholunjika kwa iye chimayamba chagwera Mpulumutsi, Amene Amakhala Atamuzungulira iye ndi Ulemerero Wake. Chirichonse chobwera kwa iye, chimachokera kwa Khristu. Iye safunikanso kulimbana ndi choipa, popeza Khristu ndiye Linga lake. Palibe chomwe chingam’khudze, pokhapokha chitabvomerezedwa ndi Ambuye, chomweco, “zinthu zonse” zololedwa ndi Ambuyezo, “zithandizana kuwachitira ubwino amene akonda Mulungu.” Aroma 8:28.³

Komatu Mwinimunda Sanathane nayobe ntchito Yakeyo. Atatero Amatengano lamba lamphamvu namangiriza limodzi nthambi yatsopanoyo ku mtengo wobvulazidwawo. Mzere ndi mzere umakulungidwa kufira mphepo ndi ndi anamondwe a m’moyo uno sangathenso kulekanitsa nthambi yotereyo. Potero nthambiyo imakhalano imodzi ndi Mtengo wa Azitonawo (Kapena kuti Mpesa).

“Kulumikizana kwa nthambi ndi Mpesa, Yesu Adati kukuimira ubale womwe ife ndi Iye tikuyenera kukhala nawo. Namphatika wa ntheteyo, (nthambi) amaphatikizidwa ku Mpesa wamoyo, luzi kwa luzi, mtsempha kwa mtsempha kufikira atakula molimba monga Mpesa. Moyo wa Mpesa umakhalano moyo wa nthambi.”⁴

Ngakhale zitafika poteropobe, Mwinimunda Sanathane nayobe nthambi yoteroyo, pakuti cholinga Chake ndicho chakuti nthambi yoteroyo ifikire pobala zipatso. “...Koma chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifundo, kukoma mtima, chikhulupiriro, chifatso chiletso...” Agalatiya 5: 22-23. Tikafika apa, tikubwereranso ku chobvala cha

ukwati, Mwinjiro Wa Chilungamo Cha Yesu Khristu, chomwe ndicho Khalidwe Lake, mwinjiro womwe tonsefe tikuyenera kuubvala ngati tikufuna kukhala okonzeka pa kubwera Kwake.

Pofuna kuti chipatso chimenechi chionekere, pakufunika kusadza nthambi. Iyinso ndiyo ntchito ina ya Mwinimunda. Nthawi zambiri padzapezeka tinthambi tongodzimerera toyenera kusadzidwa pofuna kubwezera nyonga ku nthambi. Masamba osafunikira amapereka chiyembekezo cholakwika ndipo nthawi zambiri amangotsamwitsa kakulidwe ka chipatsocho.

Chinthu chimodzi chomwe Mwinimunda amayang'anitsitsa ndicho makulidwe obweretsa chiopsezo ku nthambi zonse - omwe ndiwo kukhwinyata. Bvuto lomwe limakhalapo ndi kukhwinyata ndilo lakuti pamene nthambi yokhwinyatayo ilendewera niikhudza nthaka, imayambano kukhala ndi magwero awiri otengako mphamvu zake. Koma Yesu Khristu akuti, "Palibe munthu angathe kukhala kapolo wa Ambuye awiri..." Mateyu 6:24.

Ngoleka ukuyenera kudula nthambi zokhwinyatazi, n'cholinga chakuti nthambi ikhale ndi moyo kuchokera ku gwero limodzi lokha. Mosamalitsa, Wam'munda amanyamula nthambi zowera-mazo, nazikoloweka ku akalunguse, kumene zingatheno kupuma mpweya wabwino ndi kuombedwa dzuwa la Chikondi Cha Mulungu. Khalidwe lililonse lachibadwa lofuna kuchita tchimo limadulidwa mu mchitidwe woterewu wotchedwa Kuyeretse-dwa. Ntchito imeneyi ndiyo ya Mwinimunda. Nthambi iriyonse ikuyenera kumvera ndi kulolera Mwinimunda kuchita ntchito Yake imene Iye Mwini Akudziwa kuti ndi ya ubwino wathu.

Pokhapokha ife tikhala mwa Iye ndipo pamene tidzayenda mu ungwiro, pakuti ungwiro umenewo ndiwo wa Iye, osati wathu. Kuyamika kotani nanga komwe tiyenera kukhala nako, podziwa kuti Iye Amatilola ife kubvekedwa ndi Mwinjiro Wake wa Chilungamo.

Mafunso othandiza kuchita zomwe mwaphunzira mu ndimeyi:

A. FUNAFUNANI

Namphatika: Kutenga nthambi yabwino ndi kuiphatika ku mtengo wakuthengo kapena muzu wakuthengo, potero kuturutsa chipatso chabwino. Kodi zoterezi n'chimodzimodzi kuphatika khalidwe la Yesu Khristu mwa ife ? Nanga ndi phunziro lanji lomwe tikupezamo?

Tsatirani ndondomeko za namphatika.

B. PANGANI ICHI KUKHALA MOYO WANU !!

“Nthambi ikuyenera kukhala ndi kulolera Mwinimunda kuchita ntchito Yake monga umo Adziwira Mwini mwa ife.” Funsani ndi pemphero kuti uwu ukhale moyo wanu... ndipo KHALANI MOYO WOTERO !!

Popeza pemphero ili layankhidwa, uwu udzakhala moyo wanga: (Ndi kusintha kwanji komwe kudzaoneka m'moyo wanga pamene Ambuye Ayankha pemphero langa.)

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito mu ndimeyi:

1. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 176.
2. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 357.
3. Thoughts from the Mount of Blessing, Tsamba 71.
4. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 675.

MAWU OWONJEZERA A:

GAWO LOYAMBA

Khalidwe

LA KHRISTU

Chikhalidwe cha Umunthu wa Khristu chikutanthauza zonse kwa ife, ndipo phunziroli likufunika kuliyang'ana mwakuya.

“Pamene tikuliyang'ana phunziroli, tichita bwino kumvera Mawu Amene Analankhulidwa ndi Yesu Khristu kwa Mose pa chitsamba choyaka moto, ‘Bvula Nsapato zako, pakuti malo amene uli iwewa ndi opatulika.’ Tikuyenera kuphunzira phunziroli ndi kudzichepetsa konse kwa munthu wophunzira kumene. Ndiponso phunziro la Kubadwa kwa Yesu khristu monga munthu, ndi phunziro la phindu, limene lidzabweretsa mphotho yaikulu kwa iye amene afufuza za nkhaniyi, amene akumba mwakuya ku choonadi chobisika.”¹

Mu Ahebri 2:16 timawerenga kuti, “Pakuti ndithu Salandira angelo, koma alandira mbewu ya abrahamu.” Kuliunika lembali mwakuya kukhoza kupangitsa wina kupeputsa kuti ngati khristu analandira mbewu ya Abrahamu, Iyeyo Sakanakhala Adamu wachiwiri. Komabe, mtundu wonse wa anthu uli ndi chiyambi chawo mwa Adamu, osati mwa Angelo. Paulo, amene ndikhulupirira kuti ndi yemwe analemba mabuku a Aroma ndi Ahebri, akutipatsa ife chifukwa china chimene tinganenere kuti Khristu Anali Adamu Wachiwiri. Aroma 9:6 akuti, “...Pakuti onse ochokera kwa Israeli siali Israeli.” Mu ndime 7 akuti, “...Mwa Isake mbewu yako idzaitanidwa.” Ana a Abrahamu, kape-na kuti mbewu yake, anayenera kukhala ana a lonjezano. Mu ndime 8 tikuwerenga motere, “...Ana a thupi sakhala iwo ana

a Mulungu ai: koma ana a lonjezo awerengedwa mbewu yake.” Yesu Khristu anali Mwana wa lonjezano, Mwana Wa Mulungu. Iyeyu akadayenera kukhala, mongofunikira kutero, mbewu ya Abrahamu, popeza anabadwa osati mwa chifuniro cha thupi. Yohane 1:13. Pali magwero owiri okha a munthu, awa ndiwo, kubadwa mwa chifuniro cha thupi, kapena kubadwa kochokera kwa Mulungu. Adamu adachokera kwa Mulungu, monganso Adamu wachiwiri, Yesu Khristu.

“Yesu Khristu Sanangotenga umunthu mwa nkhambakamwa chabe; koma anautenga umunthuwo mwa ntheradi. Iye anali nacho chibadwa cha umunthu. Monga ana ali otenga nawo thupi ndi mwazi, momwemonso Iye anatenga nawo mbali. Anali mwana wa Mariya; anali mbewu ya Davide molingana ndi banja la umunthu.”²

Indedi, Yesu anali munthu, monganso m’mene analili Adamu, amene Iye Adamlenga. Ku uzimu, Iye adali mbewu ya Abrahamu, ndiponso ku thupi, mbewu ya Davide.

Mu Aroma 8:3 Paulo akukamba mwatchutchuchu, “... Mulungu Anatuma Mwana Wake Wa Iye Yekha m’chifanizo cha thupi...” Ponena za lembo limeneli, Bukhu la Mthirandemanga limati, “Monga chifanizo cha njoka zoononga chinakwezedwa kuti iwo achiritsidwe, chomwechonso Iye, ‘Wokhala mchifanizidwe cha thupi la uchimo’ anayenera kukhala Momboli wawo.”³ Yesu anapangidwa m’chifaniziro cha abale Ake. Munthu anapangidwa m’chifaniziro cha Mulungu, komano sanali Mulungu.

Kubadwa mu thupi, molingana ndi Yesu pamene Ananena ndi Nikodimo, ndi kumene kudapangitsiratu kubadwa mwat-sopano kukhala kofunika. Yohane 3:1-6. Nchachidziwikire kuti pali bvuto ndi chibadwa choyamba cha munthu. “Khristu akutchulidwa kuti Adamu Wachiwiri. Mu Ungwiro ndi M’chiyero, polumikizana ndi Mulungu ndi kukonedwa ndi Mulungu, *Iye adayambira pomwe Adamu woyamba adayamba*. Mololera, anadutsa nthaka pamene Adamu adalephera, Napulumutsa kulephera kwa Adamu.”⁴ Apa Mulungu Alibe mulandu polenga munthu ndi *chibadwa cha umunthu chosachimwa*, popezano munali mu chibadwa cha umunthu choterechi m’mene munthu adagonjetsedwera. Funso linali lakuti: Kodi Mulungu Adal-

akwitsa popanga munthu? Kapena munthuyo adadzigwetsa yekha? Palibe nthawi imene Mulungu Adanenapo kuti munthu wauchimo wakugwa akhoza kugonjetsa satana. Zoterozo zikadakhala zotheke, ngati chomwe munthu akadafuna, chikadakhala chitsanzo chakuti munthu atsatire, osati Mpulumutsi amene pa phiri la Gologota "...Anatenga ulamuliro Wokhala Nkhoswe ya munthu pamaso pa Atate."⁵ Yesu Adayenera kupulumutsa ku-lephera kwa Adamu, chomwecho Anadzutsa anthu onse amene adzalandira nzeru Yake ya chipulumutso, *Powapatsa chilungamo Chake* ndi kuwapatsa *chibadwa chatsopano* chimene Mulungu Akhoza kugwira nacho ntchito, pakuti khalidwe latsopanolu sili-dana ndi Mulungu. Izitu ndizo zomwe kubadwanso mwatsopano kumatanthauza.

"Pamene Iye analibe banga lirilonse la uchimo, *chikhalidwe Chake cha Umungu* chidapangitsa kukhudzana ndi uchimo kukhala chinthu chowawitsa kwa Iye."⁶ Ngati Khalidwe la Khristu linali la chiyero, n'chachidziwikire kuti silikanakhala la uchimo. Zikadamangotchulidwa zokhazo za chikhalidwe Chake Chokhacho Cha umunthu choyeretsedwa. Pofuna kuti Khristu ayambe pamene Adamu adayambira, zidafunikira kuti Khristuyo Akhale ndi khalidwe longwa ngati lomwelo lidali ndi Adamu pamene ankayamba moyo wake pano pa dziko. "Khristu Adabwera pano pa dziko lapansi, Nabvala umunthu, Nakhala Woyimirira munthu, pofuna kusonyeza mu mkangano ndi satana kuti munthu, *monga momwe Mulungu Adamlengera*, pamene alumukizana ndi Mulungu atate ndi Mulungu Mwana, adali okhoza kumvera Malamulo onse a Mulungu."⁷ Yesu Khristu Adayenera kuyesedwa mu chikhalidwe cha "Monga Mulungu Adamlengera," chimene Adamu adalengeredwa nacho. Adamu woyambayo adalephera mayesowo, koma Adamu wachiwiriya Adakhoza, ndipo "Chikhalidwe Chake Chachiyero" Chidayeretsedwa.

Mbali ya mayeserozi idali mbali ya kukonza chikhalidwe imene Iye Adayenera kukwaniritsa m'malo mwa munthu. Imfa Yake, potero, Idampatsa mphamvu yopereka Khalidwe Lake kwa

iwo amene adzamkhulupirira namlandira Iye monga Mbuye ndi Mpulumutsi.

Ngati Yesu Adali ndi khalidwe la uchimo lochita kutengera, zikadatheka bwangi kukhala ndi khalidwe langwiwo? Paulo akuti-
uza ife mwa chimvekere kuti “...Chisamaliro cha thupi chidana
ndi Mulungu: pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu pakuti
sichikhoza kutero.” Aroma 8:7. “Ubongo wa munthu ndilo Likulu
la thupi.”⁸ Tiyenerano kufufuza ngati bongo, kapena maganizo
ndiwonso chibadwa cha munthu. Pa nkhanayi pali kusamvetsesa-
na kochuluka, komano mawu a Mzimu wa Chinenero atithandize.

“Chipembedzo changwiwo chimachokera pa chifuniro
cha munthu. Chifuniro ndicho chiongolero pa chibadwa
cha munthu, chomwe chimatsogolera zina zonse mwa
munthu. Chifuniro sindicho mayeso kapena kupende-
kera, komano ndicho mphamvu yeniyeni ya kusankha,
yomwe imagwira ntchito mwa ana a anthu kuti athe
kumvera Mulungu kapena kusamvera.”⁹

Sitingakaike ponena kuti zisankho zimapangidwa mu bongo,
womwe ndi Likulu la thupi la munthu. Tapeza kuti chifuniro ndi-
cho mphamvu yotsogolera, kapena kuti mphamvu yosankha yom-
we imapangitsa munthu kumvera kapena kusamvera. Tapezanso
kuti chifuniro ndicho mphamvu yotsogolera mu chibadwa cha
munthu. Ngati ife tibvomereza mphamvu imeneyi yotsogolera,
kapena kuti mphamvu yosankha kuifananiza ndi bongo kapena
maganizo, omwe ndi Likulu la thupi la munthu, pamenepo ndiye
kuti tapeza yankho lathu. Ubongo ndiwonso kwao kwa chibadwa
cha munthu. Popeza mtima ndi maganizo ndi zinthu zofanana,
tikhozano Kunena kuti pamene tilandira mtima watsopano, ndiye
kuti talandiranso maganizo atsopano, khalidwe latsopano ndi
chifuniro chatsopano.

Pokhudza za chisamaliro chathupi, Paulo akulemba motere:
“Pakuti chisamaliro cha thupi chiri imfa; koma chisamaliro cha
Mzimu chiri moyo ndi mtendere.” Aroma 8:6. Kapena ndicho
chifukwa chake Davide adanena m’bukhu la Masalmo 51:10
kuti, “Mundilengere mtima woyera Mulungu; Mukonze Mzimu
wokhazikika m’kati mwanga,” komanso Paulo adawalangiza an-
thu a ku Filipia, “Mukhale nawo mtima mkati mwanu umenenso
unali mwa Yesu Khristu Yesu.” Afilipi 2:5.

Inde, tikhoza kunena kuti Yesu Anali nawo mwayi waukulu woposa munthu wochimwa, komano osati woposa mkhristu wobadwanso kachiwiri.

“Kupyolera mu chipambano cha Yesu Khristu, mwayi umene Yesu Khristu Anali nawo, wapatsidwanso kwa munthu; pakuti munthuyo akhoza kukhala wolandira nawo mphamvu yoposa iye mwini munthuyo, yomuthandiza kukhala wotenga nawo khalidwe la Umulungu, Lomupangitsa iye kugonjetsa chibvundi chomwe chiri m’dzikoli kupyolera ku zilakolako.”¹⁰

Chibadwa ndicho chomwe chimaonetsera khalidwe lot-satira. Chibadwa cha uchimo kapena cha zilakolako za thupi, chimaberekanso khalidwe la uchimo ndi la chilakolako cha thupi. Sichingaturutsenso zina zoposera apo. “Ganizo lonena kuti nkofunika kungokuza kokha ubwino wokhawo womwe uli mwa munthu mwa chibadwa, ndi chinyengo choopsa zedi.”¹¹

Tsopano tikhozano kuona chifukwa chimene kubadwanso mwatsopano kuli kofunikira kwambiri m’moyo uliwonse wa munthu. Komabe, Yesu Sanafunikire kuti abadwensu kachiwiri popeza Iye Anali “Chachiyerocho” kapena kuti Mwana Wa Mulungu kuyambira pachiyambi. Luka 1:35. *Ife timakhala* ana aamuna ndi aakazi a Mulungu kupyolera mu *kubadwanso mwatsopano*. Ife sitinatengepo mbali pa kubadwa kwathu koyamba, komano tikuyenera kutengapo mbali mu chirichonse pa nkhani ya kubadwanso kwachiwiri. “Chobadwa m’thupi chikhala thupi, ndipo chobadwa mwa Mzimu, chikhala Mzimu.” Yohane 3:6.

Khalidwe lobvomerezeka ndi Mulungu lingakwaniritsidwe mu chikhalidwe chathu chopanda uchimo. Yesu, Adamu Wachiwiriyo Anabadwa ndi chibadwa chimenechi chosachimwa. Ifenso tikuyenera kubadwa mu chikhalidwe chimenechi chosachimwa.

Ngati chisamaliro cha thupi “chidana ndi Mulungu...” Aroma 8:7, ndipo Lamulo La Mulungu ndilo Chionetsero Cha Khalidwe Lake, ndiye kuti ife tiri ndi bvuto ponena kuti Yesu Khristu Adatengera khalidwe la uchimo.

Pamene Yesu Khristu Adadzitengera Yekha machimo a dziko lapansi, sindiye kuti zidamupanga Iyeyo kukhala Wochimwa, popeza Iye Adachita izi monga Wokhala m’malo mwa ife. Mu

njira imeneyi Adatenga chibadwa chathu chauchimo. Iye Adatenga mafooko athu onse, komanso zotengera zathu za kuchibadwa, za kuthupi ndi m'maganizo momwe. Iye Adadzitengera izi ncholinga chakuti, "Adakali Wosachimwa ndi Wokwezedwa mwa chibadwa, Iye Adabvomera kubvala Mwinjiro wa umunthu kuti Afanane palimodzi ndi mtundu wa anthu wakugwa."¹² Mtanthauzira mawu wa Webster, akutanthauzira liwu limeneli lakuti Mwinjiro, monga "chobvala chosonyeza khalidwe." Tikhoza kunena kuti khalidwe looneka ndi maso.

Kodi n'chifukwa chiyani izi ziri zofunikira kuti tizimvetsetse? Nzeru ya Mulungu ya chipulumutso imafuna munthu kukhala ndi khalidwe langwiro komano munthuyo sangathe kufikirapo.

"Zidali zotheka kwa Adamu, asadagwe, kuti akhale ndi khalidwe lachilungamo pomvera Lamulo La Mulungu. Koma iye adalephera kutero ndipo chifukwa cha tchimo lake, chikhalidwe chathu n'chakugwa ndipo sitingazilungamitse tokha. Popezano ndife akugwa chotero ndi opanda chihero, sitingathe kumvera Lamulo La Mulungu Langwiro. Ife tiribe chilungamo cha ife eni chomwe tingakwaniritse Lamulo La Mulungu. Komano, Yesu Khristu Anatipangira ife njira yopulumukirapo... Iye Adakhala moyo wopanda tchimo. Iye Adatifera ife, ndipo, Akudzipereka kwa ife, kusenza machimo athu ndi kutipatsa ife Chilungamo Chake... Khalidwe La Khristu likuimira m'malo mwa khalidwe lanu, ndipo inu muli obvomerezeka pamaso pa Mulungu ngati kuti simunachimwepo ndi kale lonse."¹³

Iyi ndiyo ntchito ya kulungamitsidwa, yomwe ndi mphatso yaulere kwa onse amene alandira njira yotereyi ya mulungu.

Zonsezi sizikanatheka ngati Yesu Khristu Akadakhala kuti Sadatenge chibadwa cha uchimo. Koma tithokoze Mulungu kuti izidi zidatheka, potero tidziwa kuti "Ndi udani ku tchimo, umene ungapezeke *mu khalidwe lokhalo la uchimo*, Yesu Khristu Adaonetsera kwa ochimwa chikondi chimene Ubwino wokha wa Umulungu ukhoza kufikirapo."¹⁴

"Umunthu wa Yesu Khristu Udafikira pachidzalo cha *chibvundi cha umunthu*, ndipo chidadzionetsera

chokha ndi maufooko ndi zifuniro za munthu wakugwa, pamene mbali inayi *Umulungu Wake Udagwiritsa pa Moyo wamuyaya*. Ntchito Yake yosenza mphulupulu za anthu siidampatse munthuyo ufulu wopitiriza kuphwanya Lamulo La Mulungu, lomwe Lidampanga munthuyo kukhala wamangawa ku Chilamulo, chimene Yesu Mwini Wake Adalipira kale mangawa woterowo mwa kuzunzika kwake. Mayesero ndi kuzunzika kwa Yesu Khristu cholinga chake chidali kumuonetsera munthu kuchimwa kwake kwakukulu poswa Lamulo La Mulungu ndi kumutengera munthuyo ku kulapa kupyolera mu kumvera Lamulolo ndiponso kumvera kwa kumulandira Ambuye Mulungu. *Chilungamo Chake Iye Adzachipereka kwa munthu*, potero kumukuza munthuyo mu ungwiro womvera Lamulo La Mulungu, kotero kuti kuyesetsa kwake kosunga Lamulo La Mulungu kukhale kobvomerezeka. Ntchito ya Yesu Khristu Idali *Yolumikiza munthu kwa Mulungu wake kupyolera mu chibadwa Chake cha umunthu, komanso kulumikiza Mulungu kwa munthu kupyolera mu Khalidwe Lake La Umulungu.*¹⁵

Dziwani izi: Kudali kupyolera mu umunthu wa Yesu Khristu omwe udapangitsa kuti munthu ayanjanitsidwense ndi Mulungu. Aroma 8:7 akutiiza kuti, "...Chifukwa chisamaliro cha thupi [chibadwa] chidana ndi Mulungu: pakuti sichigonja ku chilamulo cha Mulungu, pakuti sichikhoza kutero." *Kuyanjanitsidwa kotereku, nkosatheka kupyolera mu umunthu okha*. Bvuto ndilo lakuti, munthu nthawi zonse wakhala akuyesetsa kuthana nalo bvutoli payekha *pomutenga Yesu Khristu ndi kumutsitsa kufikira pa chibadwa chochimwa cha umunthu*, m'malo mwakuti munthuyo *alole Yesu Khristu kumutenga munthuyo pomudzutisa kuchokera ku chibadwa chake chakugwa ndi chauchimo kupyolera mu chilungamitso Chake chobvekedwa pa munthuyo chomulora iye kuima pamaso pa Atate Mulungu wokhala ndi chibadwa chatsopano* chomwe Mulungu Angathe kugwira nacho ntchito. Chibadwa chatsopanocho sichidana ndi Mulungu. Komabe ngakhale izi ziri chomwecho, khalidwe latsopanolo la munthuyo likuyenera kusalazidwa, ndipo iyi ndiyo ntchito yomwe chiyeretso chimachita. Sitingathe kukhulupirira kwenikweni zomwe chibadwa cha uchimo chidachita mwa munthu.

“Zotsatira zake za kudya za mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa zimaonekera m’ moyo wa munthu wina aliyense. Mwa munthu aliyense muli chikoka chofuna kuchita tchimo, chikoka chomwe popanda kuchiteteza, munthuyo sangathe kuchigonjetsa. Polimbana nacho chikoka choterechi, kuti munthu afikire pa mbendera yofunikirayo, munthuyo akufunikira kukhala ndi mphamvu imodzi yokha. Mphamvuyo ndiyo Yesu Khristu.”¹⁶

“*Cholowa cha ana ndicho cha uchimo.* Tchimo la-walekanitsa iwo ndi Mulungu. Yesu Adapereka Moyo Wake kuti Akalunzanitse ugufu wodukawo kwa Mulungu. Pokhudza za Adamu woyambayo, palibe chomwe anthu angapezemo komano kutsutsika ndi chilango cha imfa.”¹⁷

Pofuna kuti Yesu Khristu Alunzanitse ugufu wodukawo (Umene ukusonkhanitsa pamodzi mtundu wonse wa anthu), padafunika kuti Iye Yesuyo Akhale ndi *Chibadwa chosiyaniranatu ndi icho chomwe ife timabadwa nacho.*

“Munthu sangathe kuyeretsa munthu mzake. *Chibadwa chake chakugwa ndi chauchimo* chingampagitse iye kukhala nsembe yosabvomerezeka, nsembe yopanda mtengo yochepera ngakhale poyerekeza ndi m’mene anali *Adamu asadagwe.* Mulungu Adapanga munthu kukhala wangwiro, komano munthuyo atachimwa panalibenso nsembe ina yobvomerezeka kwa Mulungu m’ malo mwake, pokhapokha nsembe yoperekedwayo *ikhale ya mtengo wapatali koposa munthu monga m’mene iyeyo adaliri asadagwe m’chiyero ndi mu ungwiro.*”¹⁸

Chikhalidwe cha munthu wakugwa ndicho chibadwa chakugwa cha uchimo. Ichi ndicho chomwe chimapatsiridwa kuchokera ku m’badwo umodzi kufikira ku m’badwo unzake. Ndi *chibadwa chimenechi* chimene chikadampanga Yesu kukhala nsembe yosabvomerezeka, Akadakhala kuti Iye Yesuyo *Adadzitengera chibadwa cha uchimo.*

Nsembe iliyonse yosankhidwa idayenera kukhala yopanda chirenga chirichonse. “M’masiku a ana a Israeli nsembe zobwera

kwa mkulu wa nsembe ziidali kuphadzulidwa mpaka kumsana, pofuna kuonetsetsa kuti *zidalibe banga*.¹⁹ Yesu Khristu akuyenera kukhala Wopanda chirema ndi Wopanda banga. 1 Petro 1:19. Mtanthauziramawu wa Webster akutanthauzira liwu limeneli lakuti chirema monga “Kupindika komwe kumaononga *maonekedwe okoma*.” Apa n’zachidziwikire m’mene chibadwa chauchimo chakugwa, chikadakhala kuti chatengedwa ndi Yesu Khristu, chikadampangitsa iye kukhala nsembe yosabvomereze-ka. Poto nsembe yoteroyo ikadakanidwa ndi Mulungu Atate. Komano *Iye Adabvomerezedwa ndi Atate, Nsembe Yake Idabvomerezedwa ndi kulandiridwa – monga yopanda chirema kapen chipsera*.

“Kubadwa mu umunthu kwa Yesu Khristu, kwakhala ndipo kudzakhala nthawi zonse kwa chinsinsi. Zobvumbulutsidwazo ndizo zathu ndi ana athu, komano munthu wina aliyense achenjezedwe za nkhani yomupanga Yesu Khristu *kukhala ndendende m’mene ife tiriri; popeza izi sizingatheke*.”²⁰

Tikuyenera kudziwa kuti chibawa cha uchimo sitingathe kuchilamula, kapena kuchikonza ngakhale kuchisintha mu njira ina iriyonse. Chipangano chakale ndi chatsopano chomwe chimatiuza ife izi.

Yesaya 64:6 “Pakuti ife tonse takhala ngati wina amene ali osakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri ngati chobvala chodetsedwa...”

Yobu 14:4 “Adzaturutsa choyera m’chinthu chodetsa ndani? N’nena ndi ‘modzi yense.’”

Masalmo 51:10 “Mundilengere mtima woyera Mulungu; Mukonze Mtima wokhazikika mkati mwanga.”

Ezekieli 36:26 – 27 “Ndipo Ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga mkati mwanu mzimu watsopano; ndipo ndidzachotsa mtima wa mwala mthupi, ndi kukupatsani mtima wa mnofu.”

Yohane 12:24 “Indetu, Indetu, Ndinena ndi inu, ngati mbewu ya tirigu siigwa m’nthaka nifa, ikhala pa yokha iyo: koma ngati ifa, ibala chipatso chambiri.”

2 Akorinto 5:17 “Chifukwa chake ngati munthu ali wa Khristu, ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano.”

Agalatiya 5:24 “Koma iwo a Khristu Yesu Adapachika thupi, ndi zokhumba zake, ndi zilakolako zake.”

“Moyo wa Mkhritu sindiwo moyo wosula kapena wongowonjezera pa moyo wakale, komano ndi *moyo wa chibadwa chatsopano. Umafunika kufa ku tchimo ndi ku undekha ndi kuyambiranso moyo wina watsopano. Kusintha kotereku kumatheka pokhapokha pothandizidwa ndi ntchito ya Mzimu Woyera.*”²¹

Ngati tingamutenge Yesu kukhala ndi *chibadwa cha uchimo* ndiye kuti Iyeyo adayenera kulandira nawo kusinthika kotereku. Komatu satana sanapezemo mwa Iye ngakhale danga ndi limodzi lomwe(kapena chizolowezi) la uchimo pamene akadakhocha kumuchimwitsirapo Naye. *Izi sizikanakhala zotheka ngati Yesu Khristu Akadadzitengera chibadwa cha uchimo.*

“Pamene Yesu Khristu Adawerama mutu Wake Namwalira, Adanyamula nsanamira za ufumu wa satana kutsika nazo padziko. *Adamuthimitsiratu satana mu njira yomweyo yomwe satanayo adapezera chipambano chake mu Edeni. Mdaniyo adagonjetsedwa ndi Yesu Khristu mu chibadwa Chake Cha Umunthu.*”²²

Mu chibadwa Chake cha umunthu, Yesu Khritu Adamugonjetsa satana. *Zoterezi, chibadwa cha ku umunthu sichingathe kuchita.* (Chibadwa cha uchimo) chikuyenera kufa ndikukhala watsopano, ndipo munthu akuyenera kukhala wotenga nawo mbali mu chikhalidwe chaumulungu cha Khristu, asanayambe kukhala moyo wachigonjetso.

“Khalani wosamalitsa ,kusamalitsa kwenikweni pokamba za chibadwa cha Yesu Khristu. Tisamuonetsere Iye pamaso pa anthu kukhala monga ngati munthu wokhala nawo mafooko [kuthekera] a uchimo. Iye ndiye Adamu wachiwiri. *Adamu woyamba adalengedwa monga munthu wachiyero, wopanda tchimo, wopanda*

banga lirilonse pa iye; iye adalidi m'chifaniziro cha Mulungu. Komatu iye akadakhoza kugwa, ndipo adagwadi kupyolera mu kuswa Lamulo. Chifukwa cha tchimo mbewu yake inabadwa ndi chibadwa cha kusamvera. Koma Yesu Anali Mwana Yekhayo Wobadwa Yekha [Wosiyana] Wa Mulungu. Iye Adadzitengera Yekha chibadwa cha umunthu, nayedwa mu njira zonse monga munthu ayesedwera. Iye Akadakhoza kuchimwa; Iye Akadakhoza kugwa, komano Mwa Iye Munalibe ngakhale m'kamphindi kamodzi komwe ufooko wakuchita tchimo.”²³

Khristu ndiye Mwana Yekhayo amene Anabadwapo wopanda chibadwa chauchimo. Mu njira iyi, Iyedi ndiwolekana ndi wina aliyense. Onani izi: Munthu *anachita kutengera khalidwe lake la uchimo*. Yesu Khristu Adadzitengera chibadwa cha umunthu. “Mulungu Akulakalaka kutichiritsa, ndi kitimasula. Komano popeza izi zifunika kusinthika kwenikweni, *kukonzanso kwa chikhalidwe chathu chonse*, ife tikuyenera kudzipereka athunthu kwa Iye.”²⁴ Popeza ichi ndicho chiyang’aniro Chake, tikhozano kumvetsetsa chifukwa chimene, “*Monga Yesu Anali mu chibadwa cha umunthu, chomwechonso Mulungu Akufuna omutsatira ake kukhala motero.*”²⁵ Kodi ndiye kuti m’mene ziririmu tinene kuti otsatira Ake adzizunzika ndi khalidwe lauchimo lakugwali? *Nangano panali ubale wanji pakati pa Yesu Khristu ndi chibadwa chathu chauchimo chakugwachi?*

“Iye Adadzitengera pa Iye Yekha Wosachimwayo, khalidwe lathu la Uchimo, kuti Akhoze kuthandiza iwo amene ayesedwa.”²⁶

Pali kusiyana pakati pa icho chimene Yesu Khristu Adadzitengera pa Yekha, *mochita kutengera*, ndi izo zomwe Iye Mwini Adachita kutenga mwa kudzipereka kwake ndi cholinga chofuna kumubwezeranso munthu kwa Mulungu wake. Iye Adadzichepetsa Yekha kufikira panalibenso malo ena odzichepetsera kuposera pamene Adafikapo. Iye Adamva mochita kukomana nazo maso ndi maso izo zomwe munthu wofooketsetsa angathe kukomana nazo. Maufooko athu onse, zilema zathu zonse za

mtundu wina uliwonse, Iye Adali wololera kutisenzera. Koma tikumbukire kuti Yesu Khristu nthawi zonse *Ankadana nalo tchimo*. Ngati Yesu Khristu Akadachita kubadwa nalo tchimo ndiye kuti pakadakhala *magawaniko osaneneka* pakati pa *zikhalidwe ziwiri zoterozi*, m'malo mokhala mtendere weniweni. Kodi ndizo zomwe Mulungu Amafuna ana Ake kukhala nazo?

“Yesu Khristu Sakadachita kanthu kena kalikonse mu Utumiki Wake wa padziko lino lapansi populumutsa munthu wakugwa pakadapanda Umulungu kulumikizana ndi umunthu. Kuchepekedwa kwa munthu sikungathe kufotokoza mwakuya chinsinsi choterechi – kulunzantsidwa kwa zibadwa ziwirizi, Umulungu ndi umunthu. Ndizosaneneka. Zotsatira zake ndizo kungodabwa ndi kukhala chete. Komano tikuona kuti munthu ali nawo mwayi wotenga nawo mbali kukhala ndi khalidwe lime-neli la Umulungu, ndipo mu njira yokhayi iye akhoza kutengapo mbali mu chinsinsi choterechi.”²⁷

Kupyolera mu kubadwa mwatsopano, munthu ali woma-sulidwa kuchokera ku chibadwa chake chakale mwa imfa ndi kulandira chibadwa chatsopano pobadwanso. Ndi m'kupyolera mu chibadwa chatsopano choterechi pamene ife tikhoza kukhala wotenga nawo mbali mu khalidwe la Uzimu. Kuchokera m'kubadwa Kwake kufikira ku imfa Yake panali chiyanjano changwiro cha zikhalidwe ziwirizi m'moyo wa Yesu Khristu.

*China chirichonse chimene munthu amachitengera ngati chifukwa chochimwirapo, Yesu Adatisenzera – kuchitidwa nkhanza, kusunguluma, umphawi, kusamvetsetsedwa, kukanidwa, kumenyedwa, kumva ululu, kutonzedwa m'maganizo, kulephera mu ziyang'aniro za m'moyo uno, kuperekedwa ndi abwenzi, kuchitiridwa chiwembu ndi anansi Ake omwe, ngakhale kuoneka ngati Mulungu Amene Wamutaya. Kodino tingadabwe pamene Mulungu Akutipatsa langizo lotere lakuti, “Sitiyenera kukhala ndi chikaiko pokhudza nkhani ya ungwiro wopanda tchimo wa chibadwa cha umunthu cha Yesu Khristu.”*²⁸

“Nthawi yeniyeniyeni imene umunthu udalumikizana ndi Umulungu, siyofunikira ife kuti tiidziwe.”²⁹ Ndiloleni

ndiperekepo maganizo ena amene angathe kutithandiza kumvetsetsa za nkhaniyi.

“satana ndi mpingo wake wonse – popeza satanayo amati ndi wacipembedzo – adayesetsa kuti Yesu Khristu Alephere kukwaniritsa Uphungu wa Kumwamba. Yesu Khristu Atangobatizidwa, Adawerama mphepete mwa mtsinje wa Yordano; ndipo *sipadakhalenso nthawi yofanana ndi imeneyi pamene Kumwamba Kudamvera pemphero lotere lochokera Pakamwa pake. Yesu Khristu Adatenga chibadwa chathu pa Iye Yekha*. Ulemerero Wa Mulungu, Wotsika monga nkunda yowala ngati golide, Udatara pa Iye, pomwepo padamveka Mawu ochokera ku ulemerero Wa Mulungu, “Uyu Ndiye Mwana wanga Wokonedwa, Mwa Iyeyu Ndikondwera.”³⁰

Nzosadabwitsa kuti n’kale lomwe kumwamba Sikudamvepo Pempho lotere lochokera pa MilomoYake Ya Umulungu. Ngati Yesu khristu pa nthawi yonga ngati iyi Adadzichepetsa kotheratu, tangoganizani kuti pemphero Lake Lidali lotani – *Pemphero loona mtima kwa Atate kuwapempha kuti tchimo lina lirilonse lomwe munthu adachimwapo libwere pa Iye*. Angelo ndi onse okhala kumwamba ayenera kuti adazizwa koposera muyeso wawo kuti amvetsetse chifukwa chenicheni chimene anthu ochimwa, osayamika ndi osayenera akadayenera kupatsidwa chipulumutso, *mwa Yesu Khristu kutenga kuchimwa kwa munthu*. Zidali zobvutiratu kuti iwo amvetsetse Chikondi choterechi. Adamu adakhala munthu wochimwa pamene adasankha kukhulupirira satana m’ malo mokhulupirira Mulungu. *Chikhalidwe chake chidasinthika kuchokera ku chikhalidwe chosachimwa kukhalano chikhalidwe cha uchimo*. Yesu Khristu *Adasankha kudzitengera pa Iye Yekha* tchimo la dziko lonse lapansi, kuphatikizapo chibadwa cha munthu cha uchimo. Chiyeretso cha munthu chidayenera kufikira kuposa zochita za munthu, kufikira ku gwero lake – lomwe ndi chibadwa kapena maganizo a munthu. Ndipokhapo pamene Yesu Khristu Angatipatse mtima watsopano, maganizo atsopano ndi chibadwa chatsopano. Njira imeneyi ndiyo yomwe imakwaniritsa kubwezeretsedwanso kwa munthu, mu nthawi yomweyonso siidetsa Wobwezeretsayo, po-

peza tchimolo silinali Lake, koma lathu – chomwecho padafunika Mulowam 'malo Wolowa m 'malo mwathu mwa chisankho Chake. O, nzeru yozizwitsa nanga ya Mulungu yopulumutsira munthu.

Pamene Yesu Khristu Analowa m'chipululu kukayesedwa, Adanyamula katundu wolemera wa machimo a dziko lapan-si. Anali katundu wolemera koposa akatundu onse, wosatha kunyamulidwa ndi munthu wina aliyense koma Mulungu yekha. Yesu Khristu Anali munthu wathunthu, komanso Mulungu wathunthu, chinsinsi chobvuta kuchimvetsetsa.

Ngati Yesu Khristu Anali ndi chibadwa cha umunthu *monga chongochita kutengera, Sakadakwanitsa kukhala Chifanizo Cha Atate Wake* . Mtanthauzira mawu wa Webster amatanthauzira liwu lakuti uchimo monga “kudzadzidwa ndi tchimo.” Iye Mwini Adati, “...Iye amene wandiona Ine, waona Atate...” Yohane 14:9 (woonjezedwa)

Chibadwa cha uchimo chochita kutengera chikhoza, mu njira ina yocheperako mphamvu, kutheka kulamulirika. Komano, ndiye kuti tinganene kuti umenewu ndiwo ufulu womwe Yesu Khristu Amapereka kwa wokhulupirira? Zingatheke bwanji kuti ife tipulumutsidwe ku mphamvu ndi chilango cha uchimo? “*Chifukwa chake ngati Mwana Adzakuyesani inu Afulu, mudzakhala mfulu ndithu.*” Yohane 8:36. (Owonjezedwa)

Ngati *Moyo Wa Yesu Khristu Womvera* Unakwaniritsidwa kupyolera *mu kutha kulamulira chikhalidwe cha uchimo*, ndiye kuti Chitsanzo Chake kwa ife ndicho cholamulira *chibadwa chathu chauchimochi*. Baibulo Limatiuza *kuti chibadwa choterocho pokhala chosakonzeka* ndipo kuti chikuyenera chife, *ndipo ife tibadwensho mwatsopano*. Chifuniro cha Mulungu Chalembedwa m'mawu otsatirawa: “Iye Akulakalaka ife kuti tizindikire mwakuya za Chikondi Chake popereka Mwana Wake kudzatiferira kuti Alimbane nalo tchimo, *Nachotse chidetso cha uchimo pa cholengedwa chake cha Mulungu*, ndikubwezeretsanso m'chimate munthu wotayikayo, pomukweza munthuyo kumuikanso *m'chiyambi chake chaungwiro kupyolera mu Chilungamo cha Khristu Chopatsidwa kwa ife.*”³¹ Kutengapo mbali kwa Chilungamo Chake koterekuru ndiyo ntchito imene Iye Akuichita tsopano kwa onse amene amkhulupirira Iye. Iye Akukonzetsera Amayi ndi Abambo, kupyolera mu njira yowalungamitsa, pololera kutenga machimo awo olembedwa m'bukhu, kutino mbiri ya anthu ochimwawo iwoneke mwakuti “*monga ngati sitinachimwepo.*”

Sizikadatanthauza kanthu ngati Yesu Khristu Akadangobvomera chibadwa chathu cha uchimochi ndi kukhala ngakhale Atapanda kuchimwa mochita kuonekera. Lamulo La Mulungu Limatitsutsa ife za tchimo, osati pochita pokha, komanso ngakhale poganiza.

“Lamulo La Mulungu, monga momwe Lionekera M’malembo, ndi lakuya m’kutanthauzira kwake. Lembo lina lirilonse ndi lachiyero, langwiro ndi la ubwino. Lamulo limamupanga munthu kukhala womvera; Limafikira ku maganizo ndi mamvekedwe; ndipo lidzatonetsera tchimo kwa yense amene alakwira Lamulolo. *Ngati Lamulolo likadati lidzingokhudza kunja kokha, ndiye kuti sibwenzi tikuti anthu ndi olakwa m’maganizo kapena m’zikhumbo zawo. Koma Lamulo Limafuna kuti munthu yense wathunthu akhale wangwiro, wa maganizo achiyero, kuti maganizo ndi momwe munthuyo akumvera ziyanjane ndi mulingo wa chikondi ndi chilungamo.*”³²

Chibadwa cha uchimo ndilo gwero la *nthenda ya uchimo*. Machimowo ndiwo *zizindikiro za nthenda*. “...Mutu wonse ulikudwala, ndi mtima wonse walefuka.” Yesaya 1:5. Ngati Yesu Khristu Akadakhala moyo wangwiro, mbali inayo Ali ndi *chibadwa cha uchimo*, ndiye kuti zikutanthauza kuti Akadakhudzidwa ndi *nthenda imeneyi ya uchimo*, potero *pakadafunika kuti Nayenso Adzipezere Mpulumutsi WakeWake*.

Ngati titanena kuti *Chikhalidwe Chake* ndicho chomwe chinkamuthandiza kusakhala ndi *zilakolako za uchimo*, ndiye kuti sichikadakhala *chikhalidwe Chake*. Ngati Akadakhala ndi *zilakolako za uchimo*, komano Namazigonjetsa, ndiye kuti *zikadakhocha kumuipitsa Iye, pakuti m’maganizo* ndimo momwe mukhala mbewu ya uchimo.

Nangano titanthauzire bwanji nkhani yomwe ikupezeka pa Ahebrei 4:15? “Pakuti sitiri naye Mkulu wa Ansembe wosatha kumva chifundo ndi zofooka zathu; koma wayesedwa m’zonse monga momwe ife, koma wopanda uchimo:

Kuti ife timvetsetse lemba limeneli pakufunikira kuti tichotse maganizo athu operekeratu mayankho, ndi kuliona tchimo monga momwe Mulungu Mwini Alionera tchimo. *Undekha kapena kuti kudzipembedza iwe mwini ndiko gwero la machimo*

onse. (Werengani bukhu la Chuma Cha Maumboni – Testimony Treasures, bukhu 1, Tsamba 518, komanso bukhu la Mkangano waukulu pakati pa Chabwino ndi choipa – The Geat Controversy, Tsamba 294.) *Pa guwa limeneli, munthu aliyense adapembedzapo.* Mwina munthuyo amadzipembedza yekha kapenanso kudana ndi iye yekha mwini. Yesu Adati, “Iye wokonda moyo wake adzautaya; ndipo wodana ndi moyo wake m’dziko lino lapansi adzausungira ku moyo wosatha.” Yohane 12:25. Uwu ndiwo uthenga umene Yesu Adapereka kwa Nikodimo mu Yohane 3:6, “Chobadwa m’thupi chikhala thupi; ndipo chobadwa mwa mzimu chikhala mwa Mzimu.” Zinatheka bwanji Yesu Khristu kuyesedwa monga ife tiri, koma osachimwa? Ngati undekha ndiwo muzu wa machimo onse, ndiye kuti *machimo osiyanasiyana* akutanthauza *mbewu zosiyanasiyana pamene machimowo amamerapo.* Chomwecho zikhoza kukhala zoonza pamene tinena kuti *pamene undekha udabisika mkati mwa yesero lirilonse, yeserolo lidali lamphamvu.*

Tsopano tadziwa kuti “...Mulungu Sakhoza kuyesedwa ndi zoipa...” Yakobo 1:13. Pamene Yesu Khristu Anali padziko lino lapansi Adali Mulungu Wathunthu, komanso munthu wathunthu. Chomwecho popeza khalidwe la Yesu lidali losachimwa, lolingana ndi la Adamu asadachimwe atangolengedwa kumene, ndikutinso Khalidwe la Yesu Khristu lidali Khalidwe La Mulungu, tikhoza kunena kuti *padali chiyanjano chokwanira pakati pa zikhaliidwe ziwirizi – Cha Umulungu ndi chaumunthu.*

“Yesu Khristu Anadana nalo tchimo kotheratu...”³³ Anadana nalo ndi tchimo udani weniweni.

“Mu mtima wosakonzeka muli chikondi cha tchimo, -komanso maonekedwe olilera tchimolo ndikulipezera zifukwa. Komatu mumtima wosinthika mumakhala chidani chauchimo ndi chikhumbokhumbo chosalolera tchimolo.”³⁴

“Kupyolera mu kuyamikira khalidwe la Yesu Khristu, Kupyolera mu kulumikizana ndi Mulungu, tidzatha kudana nalo tchimo.”³⁵

“Iye, [Mulungu] Amafunika kuchotseratu mwa munthu icho chimene Iye Adana nacho, komano n’zofunika kuti

munthu agwirane manja ndi Mulungu mu ntchitoyi. Tchimo likuyenera kusiyidwa, kudana nalo, ndipo chilungamo cha Yesu Khristu chikuyenera kulandiridwa mwa chikhulupiriro. Potero, Umulungu udzalumikizana ndi umunthu.”³⁶

Kodi Mulungu Angathe bwanji kubweretsa udani wa uchimo mwa munthu, pamene munthuyo pa iye yekha ali nalo khalidwe lodana ndi Mulungu m'malo modana ndi tchimo? Aroma 8:7. Izi nzotheke pokhapokha tikalingalira mawu a Paulo opezeka pa Aroma 12:2, “Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe apansi pano: Koma *mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu*, kuti mukazindikire chimene chiri chifuno cha Mulungu, chabwino ndi chokondweretsa ndi changwiwo.” (owonjezedwa.) Potero “...tidzadana nacho icho chimene chiri tchimo, ndi kugwirizana nacho icho chimene chiri chabwino.” Aroma 12:9.

Tikuyenera kudziwa kuti *satana sakadatha kumuyesa Yesu Khristu kuchita zomwe Iye Ankadana nazo*. Chidani chotere cha uchimo chidali chikhalidwe Chake cha Yesu khristu. Komano chidani cha uchimo choterechi sichili cha chibadwa ndi anthu; ndipo tiri nacho kotalitali; kodi tingafananizane Naye Ambuye Wathu?

Tikuyenera kukumbukira kuti idali nkhani yomweyi pamene munthu wamphamvu zoposa, wolengedwa, adagwa napo. Undekha udaonetseredwa m'kunyada, mu nsanje, m'chinyengo ndi m'kuukira. Makolo athu oyamba adagwa ndi machimo onga ngati omwewa. Hava adayesedwa kukayikira chifukwa chomwe Mulungu Adawaletsera chipatso cha mtengo wodziwitsa zabwino ndi zoipa. Chikaikochi chidakula pamene adaona chinjokacho chikudyadi chipatsocho. Hava adati mumtima mwake, “Chondilepheretsa n'chiyani kuti nanenso ndisadye nawo?” Uwu ndiwo undekha odziwikiratu ndi wina aliyense. Naye Adamu adatsimikizika kuti afere limodzi ndi mkazi wake, poganiza kuti zomwe adachita Havazo chidali chikondi chenicheni cha pa iye. Iye adaganiza kuti zinthu zikonzeka. Uwutu udali undekha weniweni ! Kumbukirani, kuti zonsezitu zinkachitika munthu ali ndi *chibadwa chopanda uchimo* . Zidalinso chimodzimodzi ndi *mngelo wina aliyense wakugwa*. Imeneyinso ikuyenera kukhala njira imene satana adaigwiritsa ntchito pomuyesa Yesu Khristu

komanso pomuyesa munthu. Zikadatheka bwanji kuti amupangitse Yesu Khristu kuonetsera undekha? yankho lake nali:

“Inali ntchito yobvuta kwambiri kwa Kalonga Wa moyo kuchita ntchito yomwe Adachita yopulumutsa munthu, pobveka umunthu ku Umulungu Wake. Iye Adali Wolandira Ulemu kumwambako ndipo Adali ndi Mphamvu zonse. Kudali kobvuta Kwa Iye kuti asungebe umunthu pothandiza kuti anthu alekane nacho chibadwa chawo, natenge khalidwe la Umulungu.”³⁷

“ Pofuna kuphimba Ulemerero Wake monga mwana wa mtundu wa anthu wakugwa, kudali kudzisungadi kosaneneka komwe Kalonga Wa Moyoyu Adakhoza kuchita mwa Yekha.”³⁸

Khalidwe la Umulungu lomwe Iye Adalileka mwa kanthawi linali *losachimwa*, langwiro, komanso lodzazidwa ndi mphamvu. Kunali kobvutitsitsa kwa Yesu Khristu, Adakali pano pa dziko, kuti Asaonetsere *Khalidwe Lake La Umulungu*, kuti lisaonekere mu chikhaliidwe Chake cha *umunthu chosachimwa*. Chikhaliidwe chotere chakhala chofookerafookerabe kwa zaka mazana anayi a uchimo padziko lino lapansi, potero n’kobvuta kwa ife kusunga *khalidwe lathu lachibadwa* lopachikidwa ndi lokwiriridwa lomwe linali *lauchimo*, *lonyansa*, komanso lodzazidwa ndi *kunyada*, kuti lisaonekere mu *chibadwa chathu chobadwanso mwatsopano*.

Mayesero ambirimбири ochokera kwa satana ofuna kumuyesa Yesu mu umunthu Wake, adakhazikika kwenikweni *kuti Aonetsere khalidwe Lake la Umulungu*. “Ngati Uli Mwana Wa Mulungu Dzionetsere Wekha.” Awa adali mawu olankhulidwa ndi satana komanso anthu kwa Yesu Khristu. Nthawi zonse Yesu Adali mu yesero lotereli. Ngakhale iwo a pabanja Lake, pamodzi ndi ophunzira Ake omwe, onse adamuyesa yesero limeneli.

Akuluakulu, Ansembe pamodzi ndi atsogoleri, onse adagwiritsidwa ntchito ndi satana kuyesetsa *kumuumiriza Iye kudzichotsa m’manja mwa atate*, ndi *kuti Iye Agwiritse ntchito mphamvu zake*. Ngakhale Yesu Adali Nazo Mphamvu zonse koma Iye Adaima nji ! ku chasankho Chake, “Sindikhoza kuchita kanthu kwa Ine ndekha....” Yohane 5:30 (Owonjezedwa)

Satana akuyesetsa kunamiza mkhristu aliyense wobadwanso mwatsopano, *ngakhale ali nacho chibadwa chatsopano choyanjana ndi Mulungu*, kumpangitsa woteroyo kuti aonetsere *khalidwe lake lakale lomwe adalipachika*. Iye amatiyesa ife kupyolera mu makhalidwe athu akale amene ankatilamulira ife pamene tinali tisanabadwensu kachiwiri. Mayesero amenewa ndiwo *zizolowezi zathu zoipa ndi machitachita ongotengera*. Iye amawadziwa bwino lomwe, popeza ndi iye amene adatipatsa zizolowezi zoipazi. Iye amapemerera zizolowezi zoipazi mwa ife mpaka zitayaka moto, kupyolera mu njira zomwe iye amakonza. Iye amadziwa kuti *sangathe* kudzutsa chikhaliwe chatu chakale chopachikidwa, ndikuti Yesu Khristu *Sangachidzutsa*. *Ndi ife tokha eni ake amene tingayesedwe kuchita izi*. Ndi m'kupyolera muzizolowezi zathu zakale zomwe sitinazipereke kwa Yesu Khristu, zomwe satana amazigwiritsa ntchito pofuna kutiumiriza kuonetsera khalidwe lathu lakale. Ndiye amadziwa kuti ngati angakwanitse kutipanga ife kugwa mu zizolowezi zathu zakale nthawi ndi nthawi, ndiye kuti ife *tikhoza kumangokhumudwa* chifukwa cholephera, mapeto ake tidzatha kudzangogonjeratu. Ndi *pamene ife tiri mu bvuto lotereli pamene timadzichotsa tokha ku mphavu yolamulira* Ya Yesu Khristu, *ndipo poukira, timalekana Naye Mulungu*. Ichi ndicho chifukwa chake Yesu Khristu *Samakhumudwa nafe*.

Yesu Khristu Adayesedwa nthawi ndi nthawi Kuchita zinthu zina za zinthu zabwino zomwe Iye Adachita *pogwiritsa ntchito Mphamvu Zake* – monganso momwe ife tiyessedwera kuchoka pamaso pa Yesu Khristu ndi “kuchita zinthu zathu” kaya zabwino, kayanso zoipa.

Kudzipereka kwathunthu ndiyo inali njira yokhayo yomwe Yesu Khristu Adagwiritsa monga yogonjetsera. Ifenso tikhoza kugwiritsa ntchito njira yomweyo. Iye Adayesedwadi mu njira zonse monga ife tiri. Yesero lirilonse lakhala, ndipo lidzakhala lotiyesa ife *kuonetsera undekha wathu* mu njira ina kapenanso inzake. *Undekha umatilekanitsa ife ndi Mulungu wathu*. *Ichi ndi chiyang'aniro cha satana*.

Ngati Yesu Khristu Akadagwiritsa Mphamvu Zake mwa kusankha kwake, ndiye kuti Sakadakhala chitsanzo Chabwino-chakuti ife titsatirepo, potero nzeru Ya Mulungu Yopulumutsira munthu, bwenzi italephereka, popeza izi zikadatanthauza kuti Yesuyo Sadakhulupirire kotheratu mwa Atate Wake.

“Yesu Khristu Sadaonetserepo khalidwe lina lirilonse, ndipo Sadaonetserepo Mphamvu ina iliyonse, imene munthu aliyense sangathe kukhala nayo mwa chikhulupiriro mwa Iye. Umunthu Wake Wangwiro ndiwo chiyang’aniro cha munthu wina aliyense amene afuna kukhala womvera monga m’mene Iye Adali.”³⁹

Kukhulupirira kwenikweni ndiko tanthauzo lenileni la chilungamo chochita ndi chikhulupiriro !

Pofuna kuika mwa munthu chikhulupiro choterocho, nzeru Ya Mulungu Ya Chipulumutso Idakhazikitsa ubwenzi pakati pa umunthu ndi Umulungu, ubwenzi womwe ndi wamuyaya. “Potitsimikizira ife za Nzeru Yake Yosasintha Ya Mtendere, Mulungu Adatipatsa ife Mwana Wake Wobadwa Yekha kukhala m’modzi wa ife anthu, kwa nthawi zamuyaya Adzakhalabe ndi maonekedwe a umunthuwo.”⁴⁰

“Mwana Wa Mulungu tsopano Akhala ku Dzanja lamanja La Mulungu, kutidandaulira monga Wotipem-bedzera. *Iye Adakali nawobe maonekedwe a umunthu*, Ndiye Mpulumutsi wa anthu onse.”⁴¹

“...Iye Adapatsa Mwana Wake Wobadwa Yekha kubwera ku dziko lino lapansi, kutenga khalidwe la umunthu, osangoti mwa kanthawi kochepe, koma kukhala nalo khalidwe loterolo *kwa nthawi zamuyaya* kumwamba, kutionetsera za kukhulupirika kwa Mulungu.”⁴²

“Podutsa mu zochitika za kuchititsidwa manyazi Kwake, *Yesu Khristu Sadataye umunthu Wake*.....Iye Saiwala kuti Ndiye Wotiyimira ife Wathu, ndikutinso Amatisenzera *chikhalidwe chathu*.”⁴³

“Nkhani yakuti Yesu Khristu *Adatenga khalidwe la munthu*, ndikuti kupyolera m’moyo wodzichepetsa *Akweze munthuyo* kumufikitsa pa mulingo wa mtengo wofanana ndi Mulungu: Ndikuti Atenge khalidwe Lake la umunthu kukwera nalo kwa Mulungu Atate, ndikupereka pamaso pa Mulungu, ana Ake, powapatsanso ana Akewo ulemu woperekedwa kwa angelo – zonsezi ndizo

zomwe zidzakhala chozizwa cha zoziwa zonse, chozizwa chimene Angelo alakalaka kuchiona.”⁴⁴

“Ntchito Ya Yesu Khristu Inali *Yoyanjanitsa munthu kwa Mlengi wake kupyolera mu chibadwa Chake Cha umunthu, komanso kuyanjanitsa Mulungu kwa munthu kudzera mu chikhalidwe Chake cha Umulungu.*”⁴⁵

“Mulungu Akulalalaka kutichiritsa ife, ndi kutipanga ife kukhala afulu. Komano popeza ichi chifunika *kusinthika kwenikweni, kukonzanso kwa chibadwa chathu chonse, tikuyenera ife kudzipereka kotheratu kwa Iye.*”⁴⁶

“Kumwambako angelo otumikira amati: Utumiki womwe ife tapatsidwa kuchita ife tachita. Tidabwezera mbuyo angelo a satana. Tinabweretsa kuwala ndi nyali m’mitima ya anthu, kufulumizitsa kumvetsetsa kwao kwa chikondi cha Mulungu choonetseredwa mwa Yesu. Mitima yawo idadzazidwa ndi chizindikiritso cha uchimo chomwe chidapachikitsa Mwana Wa Mulungu. Iwo adatsutsika mu mtima. Adaona makwerero oyenera kutembenukira mtima; adamva mphamvu ya uthenga wabwino; Mitima yawo idasanduka yanthete pakuona ukoma wa Chikondi cha Mulungu. Adaona kukongola kwa khalidwe la Yesu Khristu. Koma kwa anthu ambiri zonsezi zinali zachabe. *Sanaleke zizolowezi zawo ndi chikhalidwe chawo.*”⁴⁷

“Kupyolera mu Chipambano cha Yesu Khristu *mwayi womwe Iye Adalinawo ifenso tikhoza kukhala nawo; popeza tikhozano kukhala nayo mphamvu yoposa mphamvu yathu, ndiyo mphamvu ya Chikhalidwe cha Umulungu, chimene ife tikhoza kugonjetsa nacho chibvundi chomwe chiri m’dziko kupyolera mu chilakolako.*”⁴⁸

“*Ubwino wonse wa munthu uli wopanda ntchito pamaso pa Mulungu. Iye Sakondweretsedwa ndi Munthu amene abwereranso ku khalidwe lake la kale, ndipo*

saonetsa kusinthika mu nzeru ndi m'chisomo chakuti iyeyo ndi wobadwanso mwatsopano mwa Khristu.”⁴⁹

“Iye Amalalakala ife kuti tione mwakuya za Chikondi Chake popereka Mwana Wake kudzatifera mu nkondo yolimbana ndi uchimo, kuti Akachotse chionongeko chobwera ndi uchimo, kuchichotsa mwa munthu, *ndi kubwezeretsanso, kukuza ndi kulungamitsa munthu ku chiyambi chake cha chiyero, kupyolera mu Chilungamo cha Yesu Khritu Chopatsidwa kwa ife.*”⁵⁰

Iyi ndiyo ntchito yomwe iyenera kugwirika Mwa Mkristu wina aliyense wobadwanso mwa Yesu Khristu kupyolera mu mphatso yosaneneka ya Mulungu ya kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro.

Funso lomwe likuyenera kufunsidwa ndilo lakuti: Ngati Yesu Khristu Anali ndi chibadwa cha uchimo, ndiye kuti Adzakhalacho chibadwacho mpakana muyaya? Ngati sichoncho, ndiye kuti zikadatengera kutula khalidwe loterolo pa nthawi ina. Nangano tinganene kuti zoterezi zidachitika liti? – Nzachidziwikire kuti sipadali pa Gologota ! Iye Adali Nsembe Yokwanira – Mwa Iye Munalibe tchimo lina lililonse. Ngati Yesu Khristu akadaganizirapo tchimo ngakhale nkamodzi kokha, Akadangofanana wamba ndi wansembe wina aliyense wa padziko lino lapansi. Wansembe wina aliyense, mwa chibadwa chake, wadetsedwapo ndi chibadwa cha umunthu cha uchimo. Poto akuyenera iye mwini kupereka nsembe kamodzi pa chaka (Ahebri 9:7) asadatumikire monga woimirira wa Yesu Khristu. Poto tikhala otsimikizika kunena kuti pa Mtanda “*Iye [Yesu Khristu] Adagonjetseratu satana mu njira yomwe satanayo adagonjetsera m'munda wa Edeni.*”⁵¹ Chibadwa chotero, mwachidziwikire, chidali chibadwa cha umunthu chosachimwa, popeza ndicho chomwe Adamu adalengedwa nacho. Iye (Adamu) adagonjetsedwa mu chibadwa chake chosachimwa.

Ngati Yesu Khristu pa Mtanda Adali ndi chibadwa cha umunthu chonga ngati cha Adamu atangolengedwa kumene, sizikadatheka kukhala ndi chibadwa cha uchimo nthawi yomweyo. Nyumba yogawikana pa iyo yokha siingathe kuima chiriri. Komabe, chibadwa Chake cha umunthu cha uchimo sichidathe

kuchepetsa mazunzo Ake pa Mtanda ngakhale pa moyo Wake wonse. Iyeyu Adatenga thupi Lake la umunthuli koma losachimwa kulowa nalo kumwamba ndipo Adzakhala nalo mpaka muyaya, Wolumikizana komanso Wokhala pamodzi ndi anthu ku nthawi za muyaya.

“Yesu Khristu sindiye kuti Sadamve chitonzo cha manyazi ndi kupeputsidwa. Zonsezi zidamugwera mowawitsa. Adazimva mwakuya ndi mowawitsa koposa m’mene ife tingamvere kuwawa ndi mazunzo, pakuti *chikhalidwe Chake chinali chokwezeka ndi changwirowo ndi chachiyero choposa icho cha mtundu wochimwa wa anthu womwe Iye Adaufera.*”⁵²

Ife ndife owomboledwa kuchokera ku chibadwa chathu cha umunthu cha uchimo kupyolera mu kubadwanso kachiwiri. Komano Yesu Khristu sipadafunikire kuti Achite kubadwanso. Chibadwa Chake Chidali Changwirowo chofanana ndi icho chomwe Adamu adali nacho asadachimwe. Ubatizo kwa Yesu siudali chisonyezo cha kufa, kuikidwa m’manda ndi kuukanso kumoyo watsopano. Iyeyo Anangotipatsa kokha chitsanzo chakuti ife titsatire. Munthu aliyense akuyenera kukhala womasuka kuchochera ku chibadwa chake cha uchimo chomwe chiri “Chodana ndi Mulungu.” (Aroma 8:7) asadakhale wotsatira wake wa Mulungu. Kusinthika kotereku sikudali kofunika kwa Yesu Khristu, popezano Iyeyo Adali Adamu wachiwiri.

Khalidwe lochimwa la umunthu lidzakhala mbiri ya makedzana mu dziko latsopano. Kwa mkhristu wobadwanso, kukhala womasuka ku chibadwa cha uchimo chotero – Kudzera mu njira ya Mulungu ya chipulumutso- kumapangitsa kuyamba kumva kukoma kwa kumwamba kuyambira padziko lapansi lomwe lino. Tithokoze chotani nanga kuti Mpulumutsi Wathu Adakhala pakati pa anthu kutibwezeretseranso chikhalidwe chathu ku nthawi zamuyaya.

Mabuku omwe agwiritsidwa ntchito:

1. Mlangizi wa Achinyamata, (The Youth's Instructor,) October 13, 1898.
2. The Review and Herald, April 5, 1906.
3. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages) Tsamba 174, 175. (Lowonjezedwa).
4. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7A, Tsamba 650, Mlangizi wa Achinyamata, (The Youth's Instructor), June 2, 1898.
5. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 745.
6. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7A, Tsamba 655, The Review and Herald, November 8, 1887.
7. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7A, Tsamba 650, Zizindikiro za Nthawi, (Signs of the Times), June 9, 1898.
8. Mauthenga kwa Achinyamata, (Messages to Young People), Tsamba 236.
9. Mauthenga kwa Achinyamata, (Messages to Young People), Tsamba 151
10. Zizindikiro za Nthawi, (The Signs of The Times), January 16, 1896.
11. Mapazi Opita Kwa Khristu, (Steps To Christ), Tsamba 18, 19. (Lowonjezedwa).
12. Zizindikiro za Nthawi, (The Signs Of The Times), April 25, 1892.
13. Mapazi opita Kwa Khristu, (Steps To Christ), Tsamba 62.
14. Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 140. (Owonjezedwa).
15. Mauthenga Osankhika, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 272, 273 (Lowonjezedwa).
16. Maphunziro, (Education), Tsamba 29.
17. Mtsogozo wa Ana, (Child Guidance), Tsamba 475, (Lowonjezedwa)
18. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7A, Tsamba 665, Mzimu wa Chinenero, (The Spirit of Prophecy,) Bukhu 2, (Lolembedwa m'chaka cha 1877) , Tsamba 9, 10. (Lowonjezedwa.)

19. The SDA Bible Commentary, Bukhu 1, TSamba 1110, Zolemba (Manuscripts) 42, 1901 (Zowonjezeredwa).
20. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, TSamba 1129, Kalata 8, 1895 (Lowonjezerewa)
21. Chokhumba cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 172. (Lowonjezeredwa).
22. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7A, Tsamba 651, Mlangizi wa Achinyamata, (The Youth's Instructor), April 25, 1901.
23. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1128, Kalata (Letter) 8, 1895. (Lowonjezeredwa).
24. Mapazi Opita kwa Khristu, (Steps to Christ), Tsamba 43. (Owonjezeredwa).
25. Maumboni, (Testimonies), Bukhu 8, Tsamba 289. (Lowonjezeredwa).
26. Utumiki wa za Chipatala, (Medical Ministry), Tsamba 181. (Lowonjezeredwa).
27. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7, Tsamba 904, Kalata (Letter) 5, 1889.
28. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1131, Zizindikiro Za Nthawi, (Signs of The Times) June 9, 1898. (Lowonjezeredwa.)
29. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1129, Kalata (Letter) 8, 1895.
30. Kudziletsa, (Temperance), Tsamba 284, (Lowonjezeredwa).
31. The Review and Herald, November 8, 1892. (Lowonjezeredwa).
32. Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 211 (Lowonjezeredwa).
33. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7, Tsamba 904, Zizindikiro za Nthawi, (Signs of The Times), January 20, 1898.
34. Mkangano Waukulu, (The Great Controversy), Tsamba 508.
35. Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 668
36. Maumboni, (Testimonies), Bukhu 5, Tsamba 632.
37. The SDA Bible Commentary, Bukhu 7, Tsamba 930, The Review and Herald, April 1, 1875..

38. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1081, Kalata(Letter) 19, 1901.
39. Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire of Ages), Tsamba 664.
40. Zizindikiro za Nthawi, (Signs of The Times), Tsamba 25.
41. Zizindikiro za Nthawi,(Signs of The Times), July 15, 1908, (Lowonjezeredwa)
42. Mauthenga Osankhidwa, (Selected Messages), Bukhu 1, Tsamba 258, (Lowonjezeredwa).
43. Maumboni kwa Abusa, (Testimonies to Ministers), Tsamba 19 , (Lowonjezeredwa).
44. Ana Aamuna ndi Aakazi a Mulungu, (Sons and Daughters of God), Tsamba 22, (Lowonjezeredwa).
45. The Review and Herald, August 4, 1874. (Lowonjezeredwa).
46. Mapazi Opita Kwa Khristu, (Steps to Christ), Tsamba 43, (Lowonjezeredwa).
47. Mafanizo A Yesu, (Christ's Object Lessons), Tsamba 318, (Lowonjezeredwa)
48. Zizindikiro za Nthawi,(Signs of The Times), January 16, 1896, (Lowonjezeredwa.)
49. Chisomo Chozizwitsa Cha Mulungu, (God's Amazing Grace.) Tsamba 66, The Review and Herald, August 24, 1897. (Lowonjezeredwa).
50. The Review and Herald, November 8, 1892. (Lowonjezeredwa).
51. The SDA Bible Commentary, Bukhu 5, Tsamba 1108, Mafunso okhudza Ziphunzitso, (Questions on Doctrines), Tsamba 651, Mlangizi wa Achinyamata,(The Youth's Instructor.) April 25, 1901.
52. The Review and Herald, September 11, 1888. (Lowonjezeredwa).

MAWU OWONJEZERA B:

CHIFUNIRO

Cha Munthu

Mphamvu ya Chifuniro

“Popanda *ufulu wa chisankho*, kumvera kwake [kwa munthu] sikukadakhala kwa chifuniro, koma kukadakhala kochita kuumirizidwa. Potero, khalidwe lake la munthu silikadakula.” Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets) Tsamba 49. (Loonjezeredwa).

“Ambiri amafunsa, ‘kodi ndingatani kuti ndidzipereke ndekha kwa Mulungu?’ ...Chomwe tiyenera kumvetsetsa ndicho mphamvu ya chifuniro cha munthu. *Iyi ndiyo mphamvu yotsogolera mu chilengedwe cha munthu, ndiyo mphamvu ya chisankho kapena yosankha.*” Mapazi Opita Kwa Khristu, (Steps to Christ), Tsamba 47. (Loonjezeredwa).

“Chifuniro ndicho *mphamvu yotsogolera ya chilengedwa cha munthu*, yolamulira *zina zirizonse* zochitika m’ moyo wa munthu. Chifuniro sindicho kungolawapo kapena kungopenderako, komano ndicho *mphamvu yeniyeni ya kusankha* yomwe imagwira ntchito mkati mwa anthu kuwapititsira ku kumvera Mulungu kapenanso ku kusamvera Mulungu.” Maumboni, (Testimonies), Bukhu 5, Tsamba 513. (Loonjezeredwa).

Chifuniro

“Pamene mubvomereza pamaso pa anthu chitsimikizo chanu mwa Mulungu, mphamvu zoonjezeredwa zimapatsidwa kwa inu. Khalani otsimikizika nthawi zonse kupereka mayamiko kwa Iye. *Ndi chitsimikizo chokhazikika, pomwepo idzabwera mphamvu ya chifuniro yochuluka; ...*” The SDA Bible Commentary, Bukhu 3, Tsamba 1143, Zolemba (Manuscripts) 116, 1902. (Zoonjezeredwa).

“Palibe china chirichonse chobvuta kwa iwo amene ali ndi *chifuniro champhamvu* choposa kusiya njira zawo za iwo eni, ndi kudzipereka ku chiweruzo cha ena.” Antchito a Uthenga Wabwino, (Gospel Workers), Tsamba 447.

Kupirira, kutsimikizika, kukhazikika, zonsezi zimasonyeza *mphamvu ya chifuniro* ndipo zimakhala mdalitso pamene zig-wiritsidwa ntchito mu njira yoyenera.

KHALIDWE LA MUNTHU

Laumunthu, Lachibadwa, Lochimwa

“Pamene munthu anaswa Lamulo La Mulungu, *Khalidwe lake linakhalano la uchimo*, ndipo anali *m’chijanano* osati *mu chidani, ndi satana*. *Mwachibadwa chathu* palibe udani [kudana] pakati pa *munthu wochimwa* ndi *woyambitsa tchimoyo*. Onsewa adaipa kupyolera mu kuukira kwao.” Mkangano Waukulu, (The Great Controversy), Tsamba 505. (Loonjezeredwa).

“Mawu [Baibulo] *amaononga chibadwa chathu cha pa dziko lino*, ndipo amatipatsa ife moyo watsopano mwa Yesu Khristu. Mzimu Woyera Amabwera m’*moyo wa munthu ngati Nkhoswe Wotonthoza*. Mwa Mphamvu Yake Ya Chisomo Chakusintha, Chifaniziro Cha Mulungu Chimaonetseredwanso mwa kusunga mwambo; potero munthuyo amakhala *wolengedwa watsopano*.” Chokhumba Cha Mibadwo, (The Desire of Ages) Tsamba 391. (Loonjezerdwa).

“...Iwo [Adamu ndi Hava] *akadagwa ku mayesero, chibadwa chawo chikadakhala choperewera* kotero kuti mwa iwo okha sakadakhala nayo mphamvu ngakhale *maonekedwe*, okhoza *ku-gonjetsa satana*.” Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 53 (Loonjezeredwa).

“Monga Adamu adalengedwa *opanda tchimo*, m’chifaniziro cha Mulungu, chomwechonso Seti, monga Kaini, *adatengera chibadwa cha uchimo chakugwa* cha makolo ake.” Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 80.

“Pakuti chomwe Lamulo Silikadatha kuchita, popeza lidali lofooka ku thupi” – Silikadatha kulungamitsa munthu, pakuti *mu chikhalidwe chake cha umunthu munthuyo sakadatha kusunga Lamulo*.” Makolo ndi Aneneri, (Patriarchs and Prophets), Tsamba 373. Loonjezeredwa.

Wokhala monga munthu, Waumulungu, Wosachimwa

“Monga nthambi ilandira moyo pamene ilumikizidwa ku mpesa, chomwechonso wochimwa amatenga nawo mbali mu Chikhalidwe Cha Umulungu, pamene alumikizana ndi Yesu Khristu.” [Maumboni, \(Testimonies\)](#) Bukhu 4, Tsamba 355. (Loonjezeredwa).

“...Munthu adapangidwa mu chifaniziro cha Mulungu. *Chikhalidwe chake chinali choyanjana ndi Chifuniro Cha Mulungu.*” [Makolo ndi Aneneri, \(Patriarchs and Prophets\)](#), Tsamba 45. (Loonjezeredwa).

“Ngati wina akonda Ine adzasunga mawu Anga; ndipo Atate Wangwa Adzamkonda, ndipo tidzadza kwa iye, ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo.” Yohane 14: 23. Chikoka cha maganizo amphamvu ndi angwiro chidzakhala mwa ife; popeza tidzakhala olumikizana kotheratu ndi Kasupe wa Mwinimphamvu yonse. *M'moyo wathu wa Umulungu tidzakhala omangika kwathunthu kwa Yesu Khristu.* Sitidzakhalanso moyo wa wamba wa undekha, komano Yesu Khristu Adzakhala mwa ife kotheratu.” [Mafanizo a Yesu, \(Christ Object Lessons\)](#), Tsamba 61. (Loonjezeredwa.)

Mawu akuti “*Chibadwa cha umunthu*” akhoza kugwiritsidwa ntchito potanthauza Khalidwe losachimwa (Lisadalowe tchimo), kapenanso akhoza kutanthauza khalidwe la Mkhristu amene wabadwanso mwatsopano. Komanso mawu omwewa akhozanso kutanthauza *chibadwa cha uchimo* molingana ndi m'mene ife tingawagwiritsire ntchito.

Khalidwe

“Khalidwe limaonetseredwa, osati mu ntchito zabwino za apa ndi apo, kapenanso mu ntchito zosakhala bwino za apa ndi apo, komano limaonetseredwa mu ntchito za mawu achizolowezi ndi machitachita a chizolowezi.” [Mapazi Opita Kwa Khristu, \(Steps to Christ\)](#), Tsamba 57, 58.

“Machitachita amapanga chizolowezi, ndipo chizolowezi chimapanga khalidwe...” [Magwero a Maphunziro a Chikhristu, \(Fundamentals of Christian Education\)](#), Tsamba 194.

Potero tikhosha kunena kuti, machitachita obwerezabwereza amapanga zizolowezi, ndipo zizolowezi zimapanga khalidwe, ndipo khalidwe limapanga tsogolo lathu la nthawi ino komanso la nthawi zamuyaya.” [Mafanizo a Yesu, \(Christ Object Lessons\)](#), Tsamba 356.

Kulungamitsidwa

“Ngati utadzipereka kwathunthu kwa Iye, ndi kumulandira Iye monga Mpulumutsi wako, chomwecho, ngakhale udakali munthu wochimwa, komano mwa Iye iwe udzayesedwa wolungama. Khalidwe La Yesu Khristu Limakhala m’ malo mwa khalidwe lako, potero udzabvomerezedwa pamaso pa Atate monga ngati kuti sudachimwepo.” [Mapazi Opita Kwa Khristu, \(Steps to Christ\), Tsamba 62.](#)

“Ngakhale wochimwa sangadzipulumutse yekha, iyeyo ali nawobe mwayi wakuti akhoza kuchitapo kanthu kena kakuti adzapulumuke. Yesu Khristu Adati, ‘Yense wodza kwa Ine, Sindidzam’ taya kunjja.’ Komano chofunikira ndicho chakuti ife *tidze* kwa Iye; ndipo pamene tilapa machimo athu tikuyenera kukhulupirira kuti Iye Watilandira ndipo Watikhulukira. Chikhulupiriro ndi mpatso yochokera kwa Mulungu, komano ziri kwa ife kuchita nacho chikhulupirirocho... Yesu Khristu Adatifera ife chifukwa pa ife tokha sitikadakhocha kuchita chinthu chotere. Mwa Iye ndimo muli chiyembekezo chathu, kulungamitsidwa kwathu komanso chilungamo chathu.” [Makolo ndi Aneneri, \(Patriarchs and Prophets\), Tsamba 431.](#)

“Njira yokhayo imene munthu [wochimwa] angafikire chilungamo ndiyo kupyolera mwa chikhulupiriro. Mwa chikhulupiriro munthu angathe kutenga khalidwe la Yesu Khristu ndipo Mulungu Amamuwerengera munthu woteroyo Khalidwe La Yesu Khristu kukhala khalidwe lake. Chilungamo cha Yesu Khristu chimalandiridwa m’ malo mwa kulephera kwa munthu, potero Mulungu Amamulandira munthuyo, Amamukhulukira ndi kumulungamitsa munthu wolapa choteroyo, Namuona iye monga munthu wolungama, Namukonda umo m’ mene Akondera Mwana Wake Yesu Khristu. [The SDA Bible Commentary, Bukhu 6, Tsamba 1073, The Review and Herald, November 4, 1890.](#)

Kuyeretsedwa

“...Kuyeretsedwa ... kumatanthauza kufa ku undekha tsiku ndi tsiku, komanso kusanthulika mtima tsiku ndi tsiku pa kuchita chifuniro cha Mulungu. Chiyeretso cha Mtumwi Paulo chinali cholimbana ndi undekha nthawi ndi nthawi. Iye adati, ‘Ndimafa ine tsiku ndi tsiku.’ Chifuniro chake ndi khumbo lake tsiku ndi tsiku chidalimbana ndi ntchito komanso chifuniro cha Mulungu.

M'malo motsatira chizolowezi cha uchimo, iye adachita chifuniro cha Mulungu, ngakhale chinkaoneka chosasangalatsa komanso chopachikitsa chibadwa chake.” [Maumboni, \(Testimonies\), Bukhu 4, Tsamba 299.](#)

“Kuyeretsewa kumatanthauza chizolowezi cholumikizana ndi Mulungu nthawi zonse.” [The SDA Bible Commentary, Bukhu 7, Tsamba 908, The Review and Herald, March 15, 1906.](#)

“...Tikuyenera ife kulingalira mawu a Mtumwi amene akudandaulira kwa abale ake, mwa zisomo za Mulungu, kupereka matupi awo, ‘Nsembe ya moyo, yachiyero, ndi yobvomerezeka pamaso pa Mulungu.’ Ichi ndicho chiyeretso chenicheni. Sindi cho chiphunzitsa chabe, kapena kungotengeka kokha, kapena nkambakamwa, komano ndicho chikhazikiko cha moyo cha machitachita chomwe chimakhala m'moyo wa munthu tsiku ndi tsiku.” [Malangizo a zakudya ndi kadyedwe, \(Counsels on Diet and Foods\), Tsamba 164, 165.](#)

‘Phunzirani kwa Ine’, Yesu Adatero; ‘pakuti ndiri Wofatsa ndi Wodzichepetsa: ndipo mudzapeza mpumulo.’ Tikuyenera kulowa mu maphunzira a Yesu, kuphunzira kuchokera kwa Iye maphunzira a kudzichepetsa ndi kufatsa. Chiombolo ndicho ntchito imene imachitika m'moyo kuukonzetsa ku khalidwe la kumwamba. Kuphunzira kotereku ndiko kumudziwa Yesu Khristu. Kukutanthauza kumasuka ku maganizo, zizolowezi ndi machitachita amene tidaphunzira kuchokera kwa mfumu ya midima, satana. Moyo wathu ukuyenera kuombedwa ku zonse zotsutsana ndi kumvera Mulungu.” [Chokhumba cha Mibadwo, \(The Desire of Ages\), Tsamba 330.](#) (Loonjezedwa.)

Chilungamo Cholandira

Mtanthauziramawu wa Webster’s New College, wa 1973, akutanthauzira liwu limeneli lakuti kuyesedwa wolungama monga “*kupereka kwa munthu kapena kupereka ku ntchito.*”

“Pakati pa chinamtindi cha anthu odzitchula okha kuti ndi Akhristu, Ululu wophwanya Lamulo La Mulungu mwadala ndi wosadziwika. Ambiri satha kumvetsetsa kuti chipulumutso chimalandiridwa kupyolera mwa Mwazi Wa Yesu Khristu kupyolera mu Chilungamo Chake Choperekedwa kwa ife. Komano izi pa izo zokha ndi zokwanira kumpanga munthu wakugwa kukhala momwe ayenera kukhalira, ndi kumukuza kuti akhale chiwalo

cha Banja Lachifumu.” [The Review and Herald](#), November 8, 1892. (Loonjezeredwa).

M’kulungamitsidwa, Khalidwe la Yesu Khristu Limaperkedwa kwa ife (Kulandiritsidwa kwa ife). Poto timaoneka osinthika pamaso pa Mulungu.

Chilungamo chotengapo mbali

Mtanthauziramau wa Webster’s New College, wa 1973, amatanthauzira liwu limeneli lakuti kutengapo mbali monga “Kupatsa, kapena kupereka uthenga.”

“Yesu Khristu Amapereka Chilungamo Chake kwa iwo amene amabvomereza kuti Iye Awachotsere machimo awo. Ife ndife amangawa ake a Yesu Khristu chifukwa cha Chisomo Chake [Khalidwe Lake] Limene Limatipanga ife kukhala athunthu mwa Iye.” [The SDA Bible Commentary](#), Bukhu 7, Tsamba 972, [Zolemba](#), (Manuscript) 40, 1900.

“Chilungamo chomwe ife timalungamitsidwa nacho ndicho chochita kulandira; Chilungamo chomwe ife timayeretsedwa nacho ndicho chomwe ife timatengapo mbali. Choyambacho ndicho Dzina lathu lolowera kumwamba, chachiwiricho ndicho chotiyeneretsera ife kulowa kumwamba.” [Mauthenga kwa Achinyamata](#), (Messages to Young People), Tsamba 35.

Mu chiyeretso, Khalidwe La Yesu Khristu limapatsidwa kwa ife (Kapena kuti kuperekedwa kwa Wokhulupirira, ndipo limakhala mbali ya chikhalidwe chake). Poto munthuyo amakhala wosinthika.

Kufa ku Undekha

“Pamene undekha upachikidwa ndipo Yesu Khristu Akhazikika mwa ife, Chiyembekezo cha ulemerero, tidzaonetsera, m’maganizo athu, m’mawu, ndi muzintchito, choonadi cha chikhulupiriro chathu mu choonadi.” [Maumboni](#), (Testimonies), Bukhu 7, Tsamba 116.

“Palibe mawu okwanira amene angathe kunena za mtendere ndi chimwemwe chomwe chimakhala mwa munthu amene akhulupirira mawu a Mulungu. Munthu wotereyu, sazunguzika ndi mayesero, kapenanso kutopa ndi kupeputsidwa. Undekha udapachikidwa kale mwa iye.” [Mauthenga kwa Achinyamata](#), (Messages to Young People), Tsamba 98.

“Podziwa ichi, kuti umunthu wathu wakale unapachikidwa pamodzi ndi iye, kuti thupi ili la uchimo likaonongedwe, kuti ife tisakhalenso akapolo a tchimo.” Aroma 6:6.

“Nthawi zonse tirikusezasenza m’thupi kufa kwake kwa Yesu, kuti moyonso wa Yesu Uoneke m’thupi mwathu. Pakuti ife amene tiri ndi moyo tiperekeka ku imfa nthawi zonse, chifukwa cha Yesu, kuti moyonso wa Yesu uoneke m’thupi lathu lakufa. Chotero imfa ichita mwa ife, koma moyo mwa inu.” 2 Akorinto 4:10-12.

Surrender

“Alipo ena amene akufuna, nthawi zonse kufunafunadi ngale ya golide. Komano ambiri a iwo *salekeratu zizolowezi zawo zoipa*. Iwowa *safa ku undekha* kuti Yesu Khristu Akhale mwa iwo. Poto sakhocha kupeza ngale ya mtengo wapataliyo.” [Mauthenga Osankhidwa, \(Selected Messages\), Bukhu I, Tsamba 399.](#) (Loonjezeredwa.)

“Kukhulupirira kwenikweni mu Mawu a Yesu ndiko kudzichepetsa kwenikweni, “kudzipereka kwenikweni.” [Chokhumba cha Mibadwo, \(The Desire of Ages\), Tsamba 523.](#)

“Pamene munthu adzipereka yekha kwa Yesu Khristu, *Mphamvu yatsopano imayamba kulumulira mtima wake*. Kusinthika kumaoneka kumene munthu aliyense sangathe kukwaniritsa mwa iye yekha. *Ndi ntchito Yauzimu, imene imabweretsa zochitika za uzimu mu chikhalidwe cha munthu*. Moyo woterewu, umene wadzipereka kwathunthu kwa Yesu Khristu, umakhala Linga lolimba lomwe Yesu Mwini Amautchinjuriza mu dziko loukirali, ndipo Yesu Khristu Salolera kuti moyo wotere ukhalenso wa wina, koma Iye Mwini Ndiye. Moyo woterewu, wosungidwa ndi angelo a kumwamba, sungathe kugonjetsedwa ndi satana... njira yokhayo yogonjetsera choipa ndiyo Mphamvu ya Yesu Khristu Yokhala mwa ife mwa chikhulupiriro mu Chilungamo Chake. Pokhapokha titalumikizana kotheratu ndi Mulungu, sitingathe kugonjetsa zotsatira zopanda chiyero za kudzikonda tokha, ndi mayesero a kuchimo. *Tingakhoze kusiya zizolowezi zambiri za uchimo, mwa kanthawi tingakhoze kulekana naye satana; koma ngati sitilumikizana kotheratu ndi Mulungu podzipereka tokha athunthu kwa Mulungu kupyolera m’kugonjera kwa ife tokha kwa Iyeyo mphindi ndi mphindi, tidzagonjetsedwa*”. [Chokhumba cha Mibadwo, \(The Desire of Ages\), Tsamba 324.](#)

Kudzipereka ndi kufa ku undekha ndi zinthu ziwiri zofanana.

Kubadwanso

“Pamene Mzimu Wa Mulungu Alamulira mtima wa munthu, mtima wa munthuyo umakhala wosinthika... *Mdalitso umbwera pamene mwa chikhulupiriro munthu adzipereka yekha kwa Mulungu.* Pomwepo Mphamvu imene diso la munthu silingakhoze kuona imalenganso munthu watsopano ofanana ndi Chifaniziro Cha Mulungu... Chinsinsi chake ndi choposa chidziwitso cha munthu; *komabe iye amene adutsa kuchoka ku imfa kupita ku moyo amazindikira kuti ndichochitika cha Umulungu.*” [Chokhumba cha mibadwo, \(The Desire of Ages\), Tsamba 173.](#) (Loonjezeredwa).

“*Nangano tingapulumeke bwanji?* ‘Monga Mose anakweza njoka m’chipululu,’ chomwecho Mwana wa munthu Wakwezedwa, potero aliyense amene wachimwitsidwa ndi kulumidwa ndi chinjokacho akuyenera kuyang’ana nakhale ndi moyo. *‘Onani Mwanawankhosa Wa Mulungu Amene Achotsa tchimo lake la dziko lapansi.’* Yohane 1:29. Nyali yowalira kuchokera pa Mtanda imaonetsera Chikondi cha Mulungu. Chikondi Chake Chimatikokera ife kwa Iye Mwini. Ngati ife sitingalimbelimbe ndi chikoka choterechi, pomwepo tidzatsogozedwa pansu pa mtanda polapa machimo amene anampachikitsa Mpulumutsi. Pomwepo Mzimu Wa Mulungu, *mwa chikhulupiriro Umabereka moyo watsopano.*” [Chokhumba cha Mibadwo, \(The Desire of Ages\), Tsamba 175,176.](#) (Loonjezeredwa).

“Chinthu chimodzi chikusowa,’ Yesu Anati. ‘Ngati ungakhale wangwiro, pita kagulitse izo uli nazo, nupereke kwa osauka, pomwepo udzakhala ndi chuma kumwamba: Pomwepo idza unditsate Ine.’ Yesu Khristu Adawerenga mtima wa mwinchumayo. *Adasowekera chinthu chimodzi chokha, koma chinthucho ndicho chidali chofunikira kwambiri.* Iye adasowekera chikondi Cha Mulungu mu mtima mwake. Chosowekera chimenechi, pokhapokha chitaperekedwa, munthuyo adzanka ku chionongeko; chibadwa chake chonse chidzakhala choonongeka. Mwa kutengapo mbali, undekha udzakulira kulirabe. *Pofuna kulandira chikondi cha Mulungu, chikondi chake chapamwamba chikuyenera kusiyidwiratu.*” [Chokhumba cha Mibadwo, \(The Desire of Ages\), Tsamba 519.](#) (Loonjezeredwa).

“Kubadwanso mwatsopano ndi nkhani yosowa mu m’badwo uno wa makono. Icho ndicho chifukwa chake mu mpingo muli

mabvuto ochuluka. Anthu miyandamiyanda amene amadzitchula okha kuti akhristu ali opanda chiyero ndiosapatulika. Inde, iwowa anabatizidwa, komano ubatizo wawowo adangokwiridwa adakali amoyobe, asadafe. Undekha udali usadafe, potero sadaukitsidwe ku moyo watsopano mwa Yesu Khristu.” [The SDA Bible Commentary, Bukhu 6, Tsamba 1075, zolemba 148, 1897.](#)

Nkhani yobadwanso mwatsopano imabweretsa kudzipereka kotheratu, kufa ku undekha, wolengedwa watsopano asanabadwensho mwa Mphamvu Ya Mulungu. Zoonadi ife tinalibe chisankho mu kubadwa kwathu kwa umunthu, komano kubadwanso kwatsopano mu Uzimu, kukuyenera kukhala mwa chitsankho chathu.

Chikhulupiriro

“Chikhulupiriro ndiyo njira yokhayo imene kulungamitsidwa kungakwaniritsidwire, ndipo chikhulupiriro sindicho kungokhulupirira kokha, koma kukhulupirira kotheratu.” [Mauthenga Osankhidwa, \(Selected Messages\), Bukhu 1, Tsamba 389.](#)


Chikhulupiriro ndicho kukhulupirira Mawu a Mulungu.

Ambuye Mulungu Akudalitseni kochuluka pamene mukugawana uthengawu ndi anthu ena. Thandizani so anthu ena ndi chidziwitso ndi zakuya zomwe mwapeza powerenga bukhuli mwa Ambuye Mulungu...AMEN.

**MAWU OWONJEZERA C:
MAKWERERO A CHIYERO**

God's Character Revealed in the Christian

Peter's Ladder




“This is the way, walk ye in it.” Isaiah 30: 21

SATAN'S COUNTERFEIT PLAN

Hinderances to walking in the way.

Note: To enable ease of study, this ladder is presented in reverse order, with the bottom rung at the beginning of the document and the top rung at the end.




"There is a way that seemeth right. . . ." Proverbs 16: 25

MAWU OWONJZERA D

MABUKU OTHANDIZIRA

God's Method of Imparting the Divine Nature to Man is Righteousness by Faith



Righteousness by Works is Satan's Counterfeit of Perfecting the Human Nature

Key: Satan's Plan ---- God's Plan

HELPFUL LINKS ON THE INTERNET:

Ellen White Estate:

www.ellengwhite.org (download materials)

Path to Prayer:

Learn about Prevailing Intercessory Prayer
www.path2prayer.com

David Gates:

www.gospelministry.org (sermons and books)

The Crucified Walk

www.thecrucifiedwalk.com (bible studies)
thecrucifiedwalk@gmail.com

upavision.com

ruben@upavision.com

Justified Walk Ministries

www.justifiedwalk.com (see below)
justifiedwalk@justifiedwalk.com

For our address and phone number (see copywrite page)
All materials are free of charge and download for free from the internet.

Other materials available from Justified Walk Ministries:

His Robe or Mine in other languages and English large print:

Spanish, Portugese, Chinese, Malagasy, French, Korean, as well as Russian, Romanian, Dutch. German is almost ready for print. If you would like to translate this book into your language please call Justified Walk Ministries.

Dying to self websites in other languages:

Chinese: www.xinxiangyuan.com

French: www.lamarchejustifiee.com

French e-mail: info@lamarchejustifiee.com

You can find the series listed below on the web at www.justifiedwalk.com. You can listen to them on-line or download them. You can also find the associated handouts for the Justified Walk series as downloadable pdf files. This book, His Robe Or Mine, is also available as a downloadable pdf file. (All sermons are now online.)

The Justified Walk series,

(9 sermons on-line, CDs, Cassette, MP3)

The Justified Walk handout materials, (on-line & pdf)

The Branch & The Vine series,

(6 sermons on-line, CDs, etc.)

Righteousness By Faith series, (10 sermons on-line, MP3)

His Robe or Mine (on-line, pdf and print)

God's Last Effort by Dart (the little red book)

(online and in print)

New Sermon Series available:

The Atonement (Audio 13 part series online, CDs)

Child Guidance (7 part series, online, CDs)

The Cross of Christ (3 part series, online, CDs)

Christ Our Righteousness (26 part series, CDs)

Last Week of Christ's Life (8 part series, CDs)

Impending Conflict (14 part series, CDs)

How Righteousness by Fatih Worked in Bible Characters

Lives (12 part series, CDs)

Along with **other books and sermons** from speakers who expound on the dying to self message.

Like this book: God's Last Effort to Awaken His People (in English, French, Spanish, and Chinese.)

May God richly bless you as you share this message and these materials with others. To help them gain the saving knowledge and heart experience you have found in this message through God.

